

KHAMA



Zikomo inu, M'bale Neville. Ambuye akudalitseni inu. Zikomo inu.

Mmawa, abwenzi. Ndi chamwayi kudzakhala pano mmawa uno mu Kukhalapo kwa Ambuye, mu kachisi ndi anthu. Ndipo ndi tsiku la mvula kunjako, ndipo ndangoyendetsa kudzafika pakali pano, ndipo momwe inu mumaimbira ndi kumawomba mmanja mwanu, iwo ayenera kuti akukhala ndi mivumbi ya madalitso mkatimo. Kotero izo nzabwino kwambiri. Chotero ndife othokoza kwambiri chifukwa cha tsiku lino. Ndi . . . Ife tiyenera kukhala ndi mvula. Ngati sitikhala nayo mvula, ndiye Mbuye sangakhoze kusonkhanitsa zipatso Zake. Chotero ife tiri ndi—mvula mkatimu, yauzimu, kapena sipakhala zipatso zirizonse za kukolola. Ife tiyenera kukhala ndi mvula kunjako kapena ife sitikhala nazo zokolola zachirengedwe zirizonse. Ndiko kulondola.

² Ndipo, inu mukudziwa, ziwiri zonsezo, izo zimatengera chinachake chimene chinafa kuti ife tikhoze kukhala ndi moyo. Zokolola zimabweretsa moyo, ndipo moyo uyenera kubala imfa. Kupyolera mu imfa ife tikukhala moyo. Inu mukudziwa, tsiku lililonse, mmoyo wanu wachibadwa, chinachake chiyenera kuti chife kuti inu mukhoze kukhala moyo. Iwe uyenera kuti . . . chinachake chimafa. Kotero iwe—iwe umadya ndi kukhala moyo pakudya zinthu zakufa. Ngati udyā nyama ya nkhumba, nkhumba inafa. Ngati udyā nyama ya ng'ombe, ng'ombe inafa. Ngati udyā chimanga, icho chinafa. Ngati udyā mkate wa tirigu, chabwino, iwo unafa. Iwe ukadya kale, iye anafa. Iwe umakhala moyo pakudya zinthu zakufa, mwachibadwa. Ndiye, kodi zimenezo si chitsimikiziro kuti Chinachake chinayenera kuti chife kuti ife tikakhoze kukhala Mwamuyaya? Khristu anafa, Mwana wa Mulungu, kuti ife tidzakhoze kukhala moyo Wamuyaya. Chotero ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha zonse zimenezo mmawa uno, pomadziwa kuti nthawi zowopsya izi zimene ife tikukhalamo tsopano, ndipo tikudziwa kuti Khristu anafera ochimwa, ndipo ameneyo anali ine, kuti Iye anandifera ine.

³ Tsopano, ine ndikuganiza Lamlungu lapitali inu mukukumbukira kuti Ambuye masiku pang'ono apitawo anayankhula kwa ine ndipo anati ife tinali ku . . . Inu mukuzindikira mu tepi ya Lamlungu lapitali munali kubwera ngozi. Ndikubwera kuno ine ndinali kumvetsera kuwulutsa, ndipo Germany ali ndi kusefukira koipitsitsa kumene iwo anayamba akhalapo nako mu fukoli. Iko kwapha mahandiredi, ndipo anthu akudzipachika okha. Ine ndinazilemba izi pansu, ndikubwera kuno. Ndipo mitumbira yaphwasuka, ndipo

chirichonse, mu Germany. Ndipo England akukhala ndi mphepo yamkuntho yowopsya kwambiri, iyo yawomba, ine ndikukhulupirira, manyumba sevente sauzande agwa, kale. Mukuona? Chabwino, ife tiri pa nthawi yotsiriza. Yesu awonekera limodzi la masiku awa, ndipo ife tiri pa nthawi yotsiriza. Ingokumbukirani, ichi ndi chiyambi chabe, zimenezo zizipitirira kumabwerabe ndi kumapitirira pitirira. Mukuona? Ife tiri kumapeto.

⁴ Tsopano, mawa, ukatha uthenga lero, ife tikukonzekera kuti tizipita ku Arizona kachiwiri, chotero ife tikupempha mpingo kuti utipempherere ife, ndipo pamene ife tikupita. Ndiyeno ndiri ndi zigamulo zazikulu zimene ine ndiyenera kuti ndizipange, abwenzi, ndipo ine sindingakhoze kuzipanga izo ndekha, chifukwa sindikudziwa choti ndichite. Ndipo ndiwufunsa mpingo uwu, ngati gulu la okhulupirira amene tikuyenda limodzi pano ndi ine, kuti inu mundipempherere ine, kuti malingaliro anga akakhale malo oyenera oti ndipiteko. Mizinda ina firii handiredi ya kutsidya kwa nyanja, ine ndikuganiza, ikuyitana, ndi—ndi—ndi Switzerland, Germany, ndi—ndi Afrika, ndi kulikonseko. Chotero ife tikupemphera kuti Mulungu angotithandiza ife kuti tichite chinthu choyenera pamene Iye angatigwiritsepo ife ntchito. Ndipo inu mundipempherere ine. Ine ndidzakhala ndikukupemphererani inu nthawizonse, inu mukudziwa zimenezo. Chotero inu muzindipempherera ine kuti Ambuye Mulungu anditsogolere ine.

⁵ Tsopano, pobwerera kuchokera ku Arizona, Ambuye akalola, Ine—ine ndikufuna kuti ndidzaitanire tcheru ndipo ife tidzalengeza zimenezo pa mpingo, iwo adzatero kuno, ndipo ine ndikufuna kudzakhala ndi nthawi yotalikirapo pang'ono yolankhula ndi osonkhana pano. Ine ndiri ndi Uthenga, ndipo ine ndimakonda kulalikirira pafupifupi maora eyiti kapena chinachake, mwaona, chotero monga choncho. Pamene ife. . .

⁶ Dona anali kuyankhula ndi ine, Akazi a Wood kuno a pa tchalitchi, ine ndinali kuyankhula ndi iye, ndipo ine ndinali ku Milltown ku mpingo wa Baptisti kumeneko kumene ife tinali ndi msonkhano, ndiyeno ine ndikukhulupirira umodzi wa msonkhano wawo woyambirira, anati, “Ine ndinadzalowa pa teni koloko, M'bale Branham, inu munali mukulalikirira.” Ndipo anati, “Inu munalalikirira mpaka masana, kenako madzulo onse, kenako iwo anali ndi nthawi ya fifitini pang'ono, maminiti twente kuti adye chakudya cha masana.” Ndipo anati, “Ife tinachoka usiku umenewo teni koloko, inu munali mukulalikirabe.”

Ine—ine ndinati—ndinati, “Chabwino, inu mukudziwa ine sindimadziwa zochuluka kwambiri, koma, inu mukudziwa, pamene ine nditenga zochepa zimene ndikuzidziwa panjirapo, ndi kumusiya Iye azichita kuyankhulako, ine. . . Iye amadziwa zochuluka zonse.” Chotero, ndipo ine ndimangokonda kuzimva

izo, nanenso, chotero ine . . . Koma ine ndimangonena zimenezo mwanjira yozungulira.

⁷ Koma, podzabwerera, Ambuye akalola, Ine ndikufuna kuti ndidzayambe molawirira ndi kudzangodutsapo pa Uthenga umene Ambuye akuwuyika pa mtima wanga. Ndipo ine ndikupemphera kuti Iye akapereke chidzalo cha izo kwa ine uko mu chipululu, kwa mpingo mu tsiku lotsiriza tsopano. Mwaona, kumodzi kokha kwa kusuntha kotsiriza kwa Mzimu, ine ndikukhulupirira, kuli pafupi. Ndipo ife tikukhulupirira kuti Ambuye Yesu akukonzekera kuti amasule miyamba ndi mphamvu za Mulungu, zimenezo zidzang'amba miyamba, zimenezo ife tikukhulupirira kuti Iye achita zimenezo. Ndipo chotero ife tikudalira kuti Iye adzapereka uthenga wodzadza pa izo pamene ife tikubwerera. Ndipo kudzakhala pafupifupi . . . kuyambira pafupifupi naini koloko mmawa, ndi, kapena hafu pasiti naini, ndi kudutsa mofulumira mpaka pafupifupi thuu kapena firii koloko, kapena paliponse pamene ine ndidzapeze nthawi yoti ine ndathana nazo izo, inu mukuona. Pamene . . .

⁸ Ndiye ine ndikuganiza ndiye mwinamwake kudzapita ku Afrika kuchokera kumeneko, chotero, ngati Ambuye azipitirira kumatsogolera njira imeneyo, kapena, Switzerland choyamba, kenako Palestina ndi Afrika, pa misonkhano yaikulu. Chotero, mukhale mu pemphero. Chirichonse chimene inu mukuchita, mungoyang'ana mmwamba lero ndi kupemphera, kupemphera. Ndizo zonse, ndicho chiyembekezo chokhacho chimene ife tiri nacho, ndicho pemphero.

⁹ Ife tadutsa . . . Ine ndikuyembekeza kuti ine sindikumveka mosinjirira, kapena monga ena—winawake amene samadziwa chimene iwo anali kuchikamba, koma ine ndikukhulupirira fuko lathuli, monga fuko, ilo ladutsa kale chiwombolo. Pali zambiri . . . Ngati pakanakhala Akhristu okwanira kapena okwanira pamodzi kuti achikokere icho pamodzi, koma kukoka kochuluka kwachitika, alaliki aakulu ndi mautumiki aakulu kulikonseko, ndipo komabe ilo mosalekeza likugwera mu chisokonezo. Chotero ine—ine ndikukhulupirira kuti monga ngati mafuko onse aakulu, mwaona, onse a iwo ayenera agwe. Iwo, machitidwe onse awa ndi zina zotero ziyenera kugwa.

¹⁰ Kuganizira za amuna akupereka miyoyo yawo chifukwa cha demokarase. Ndicho—ndicho chinthu chokhulupirika kwa fuko. Izo nzabwino. Palibe chotsutsa izo. Koma nanga bwanji miyoyo yathu kwa Khristu? Inu mukuona? Munthu kukhala ngwazi; nkudzakula, mnyamata wamng'ono ali pachimake cha moyo, ndipo mutu wake nkuwomberedwa cha pa mapewa ake pomwe, ndi kudzakhala ngwazi, ndipo mwinamwake osamva nkomwe za izo kupatula ngati liri banja lake lomwe kwawo, kapena winawake kuzungulira oyandikana nawo ake amene ankamudziwa iye. Koma komabe ife tikuwopa kutuluka ndi kukatenga kusuntha kokwanira uko kwa Khristu, inu mukuona,

kumene, “Iye amene awupeza moyo wake adzawutaya iwo; iye amene awutaya moyo wake chifukwa cha Ine adzawupeza iwo, adzawusunga moyo wake.” Chotero tiyeni—tiyeni tingoyika chirichonse chimene ife tiri nacho kumene mwa Ambuye Yesu ndipo tingodzisindikizira tokha kutali ndi zinthu za mdziko, ndi kuyang’ana kwa Iye ndi kukhulupirira Mawu Ake ndi kumayenda chitsogolo ndi Iye.

¹¹ Tsopano, basi asanati. . . Tsopano, lero, mundikhululukire ine, ine. . . Lamlungu lapitali ine ndinakusungani inu motalika kwambiri pa phunziro limenelo la umodzi pakati pa Mulungu ndi anthu Ake. Ndipo tsopano lero ine ndimaganiza kuti ine ndikutulutseni inu molawirira lero, chifukwa Lamlungu lapitali panali ambiri oti apemphereredwe ndipo ine ndinalibe nthawi yoti ndiyendetse mzere wa pemphero titatha—ife titamaliza kulalikirira. Ndipo—ndipo ine ndikuganiza iwo anapereka makadi ena Lamlungu lapitali kapena chinachake cha anthu, kapena chirichonse chimene icho chiri, ife tiwaitana iwo ngati iwo ali mchipinda muno, ndipo, ngati mulibemo, ife tidzapemphera mulimonse.

¹² Tsopano, lero ine ndikungofuna kuti ndiyankhule pa phunziro kukhala ngati timange chikhulupiriro. Inu muyenera kutero. Ngati inu mukumanga chirichonse. . . Ngati pali atumiki pano zimene sindikukaikira kuti alipo, akudziwa kuti pamene iwe ukuyankhula ndi anthu umakhala ndi chikhalidwe cha kulalikirira kwa chipulumutso, ndiye umafuna kuti upange kuyitanira kumeneko kwa izo. Ndiyeno ngati iwe ukufuna chikhalidwe cha machiritso, iwe—iwe umakapeza kudzozako wekha, ndi Mawu a Mulungu, ndi kukupereka iko kwa anthu, ndipo zimenezo zimadzayika gulu lonselo mu kudzoza kwa chinthu chinachake. Mwinamwake, pansi pa ziyembekezo za zinthu zina. Mwaona, ife tikuyembekezera chinachake.

¹³ Ndipo inu mukudziwa, ine ndimakhulupirira zikatero, kuti ndizibweretse zimenezo mokwerrerapo pang’ono, kuti Mulungu ali nawo Mpingo Wake wonse tsopano, oyitanidwa-atuluke, otsalira a Mpingo Wake, pansi pa ziyembekezo za Kudza Kwake, inu mukuona. Ine ndikukumbukira pa chipata pa kudza Kwake, payenera kuti panali Lachisanu Labwiño lopambana pamene iwo ankadziwa kuti Iye anali kubwera ku phwando, ndi ziyembekezo. Ambiri a iwo anali kumuyembekezera Iye kuti adzakhale kumeneko, kuti adzawone mtundu wina wa chozizwitsa chimene Iye akanati adzachite. Kapena, ndipo ena ankafuna kuti amuwone Iye. Ena ankafuna kuti adzamuseleule Iye. Ndipo izo zinali ngati a—paskha yosinthika kuposa mmene zinkakhalira kwa nthawi yaitali, pamene Iye ankalowa mu mzinda. Tiyeni tingokhala tikumuyembekezera Iye kuti abwere kudzatitengera ife Kwathu, ndiyeno ife tidza. . . pamene Iye akudzabwera nthawi iyi.

¹⁴ Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu pamene ife

tikuyankhula kwa Iye. Tsopano pa omvetsera awa a anthu, ngati pali chopempha chirichonse pano chimene chingafune kudziwika kwa Mulungu, kodi mungakwezere dzanja lanu kwa Iye, ndipo, monga, “Mulungu, mundichitire ine chifundo. Ine—ine ndikusowa chipulumutso, ine ndikufuna machiritso, ine ndikufuna kuyenda pafupi ndi Inu.” Mulungu akudalitseni inu. Izo ziri paliponse mchipindamu.

¹⁵ Atate athu Akumwamba, pamene ife tikuyandikira mpando Wanu wachifumu wa chisomo, mu Dzina la Ambuye Yesu, Mmodzi uyo Amene antibweretsera ife chisomo chodabwitsa ichi, momwe ife tikukuthokozerani Inu ndi mitima yathu yonse chifukwa cha Iye Amene anali wopanda tchimo ndipo anabwera kuno ndipo anadzatigulira ife chipulumutso, osayenerawo, kuti ife pokhala osayenera panobe tidzakhoze kubweretsedwa pafupi kwa Iye mwa kukhetsa kwa Magazi Ake, kuti Iye adzakhoze kutitsuka ife ndi madzi a Mawu ndi kutipereka ife kwa Atate Ake ngati namwali wangwiro, anatsukidwa, anayeretsedwa ndi Magazi Ake, ndipo anapangidwa wolandiridwa pamaso pa Mulungu, wotsukidwa ndipo wokonzeka. Pamene ife tikuganizira za kutsuka kwa Nsembe, tikuganiza kuti pamene Yohane anamuwona Iye akubwera mmadzi, iye anayankhula ndipo anati, “Ine ndikusowa kuti ndibatizidwe ndi Inu, ndipo ndi chifukwa chiyani Inu mukubwera kwa ine?”

¹⁶ Anati, “Balola izo, Yohane, kuti zikhale chomwecho.” Oh, ine ndikuzikonda zimenezo. Mu mawu ena, “Yohane, ndiwe mneneri, Ndine Mulungu wako. Ndife amuna otsogolera a tsiku lino. Ine ndikudziwa iwe ukumvetsa, ndipo chomwechonso ine ndikumvetsa. Koma, kumbukirani, Yohane, izo zikutikakamiza ife, izo zikutiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.” Yohane, podziwa kuti Nsembe iyenera kutsukidwa Iyo isanaperekedwe nsembe, ndipo Iye anali Nsembe, kotero iye anamubatiza Iye, Mmodzi wopanda tchimoyo, akutsuka Nsembe Iyo isanaperekedwe.

¹⁷ Mulungu, tsukani mitima yathu mmawa uno. Titsukeni ife ndi madzi a Mawu, kuti ife tikhoze kudzipereka tokha kwa Inu. Tiyeretseni ife, Ambuye, ku kusakhulupirira konse, kuti ife tikhoze kukokedwera pafupi ndi Inu ngati nsembe yamoyo, oyera ndi ovomerezeka kwa Mulungu, pakuti uwu ndi utumiki wathu womveka bwino. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha munthu aliyense yemwe ali pano. Ndikupemphera kuti Inu mudalitse Mpingo wawukulu wa konsekonse wa Mulungu wamoyo, kudutsa mafuko onse ndi kuzungulira dzikoli. Mmawa uno, kumene atumiki akuima pa guwa, ine ndikupemphera kuti Inu mutsanulire Mzimu Wanu, Ambuye, mwanjira yozizwitsa pa m’busa wokhulupirika aliyense pa malo ake antchito, pa alaliki, pa amishonare. O Mulungu, pamene ine ndiganizira za iwo kunjā uko, ena a iwo osavala nsapato, mathalauza akale

amasanza atawakulunga mozungulira iwo, akupita kudutsa mu nkhalango, kuti akabweretse mtendere ndi chiwombolo kwa iwo amene ali kutali ndi Khristu.

¹⁸ Mulungu, ife tikuti, “Mutumizeni Yesu mwamsanga. Bwerani, Ambuye Yesu.” Ndipo tsopano ife tikuwona chirengedwe, chizindikiro chomwecho monga nyenyezi imene inkawatsogolera amuna anzeru akupita ku Betelehemu, ikuyendanso kachiwiri. Yesu anati padzakhala kudodometsa kwa nthawi, kupsyinjika pakati pa mafuko, zizindikiro kumwamba ndi dziko lapansi, nyanja ikubangula, mikuntho yaikulu ndi mafunde ndi zivomezi mmalo osiyanasiyana. Zinthu izi ziri basi . . . izo ndi maberu omwe akutchera maberu a mtima wathu, Ambuye, kuti ife tidziwe kukonzekera. Ife sitikudziwa miniti yanji kapena ora limene Iye angawonekere.

¹⁹ Ndipo pamene ife tikubwera lero, ife tikupemphera kuti Inu mudalitse chinsinsi kuseri kwa dzanja lililonse limene linakwezedwa mmwamba. Mulungu, Inu mukudziwa zonse za izo. Ine ndikupemphera kuti Inu muwasambitse iwo, Ambuye, ndi nsembe yawo ndi chikhumbo, ndipo mupereke kwa iwo chimene iwo akuchisowa. Ndipo pamene ife tikubwera lero, Ambuye, ine ndikupemphera ngati angakhalepo iwo pano amene sakukudziwani Inu ngati Mpulumutsi, kuti ili likhale tsiku limenelo, tsiku lalikulu lija la moyo wawo, pamene iwo adzanene kuti “inde” kwa Ambuye Yesu. Perekani izi, Ambuye.

²⁰ Adalitseni iwo tsopano, Atate, pamene ife tikuyesetsa kuti tiwakonzekeretse anthu kuti akhale ndi chikhulupiriro, pa kuwerenga Mawu Anu. Mulungu, atumizeni Mawu Anu ndi mphamvu, uko kudutsa mchipinda muno, ndi kupita ku maiko kumene matepi ati adzapiteko, ndi mafuko akunja, kulikonse kumene izo zingakhale, ndipo mulole ambiri apulumutsidwe ndipo achiritsidwe lero kwa ulemelero wa Mulungu. Ife tikupempha izi mu Dzina la Mwana Wake wokondedwa Woyera, Ambuye Yesu Khristu. Amen.

²¹ Ife tikupemphera kuti Mulungu awonjezere madalitso Ake opambana tsopano pamene ife tikuwerenga Mawu Ake. Kumbukirani, mawu anga adzalephera, iwo ndi mawu a munthu, koma Mawu Ake sangakhoze kulephera. “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita koma Mawu Anga sadzapita.” Ndi chiyembekezo bwanji chimenecho lero! Ine ndikumverera ngati ndiyimbe ndi Eddie Perronet, “Onse yamikani mphamvu ya Dzina la Yesu, lolani angelo agwe modzilambatitsa; bweretsanipo nduwira yachifumu, ndi kumuveka korona Iye Ambuye wa onse. Pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine ndaima; maziko ena onse ndi mchenga wotitimira, maziko ena onse.”

²² Tsopano, kwa ambiri a inu amene mumawerenga ndi ife ndipo mukufuna kuti mulembe mutu, ndipo nthawizina izo zimalozera ku Malemba amene ine ndawalemba apa pa zolemba,

ife tikuti tiyambe, tiwerenge mmawa uno kuchokera ku Mateyu Woyera 15:21.

Ndipo Yesu anachoka kumeneko, ndipo ananyamuka kupita mmagombe a ku Turo wa Sidoni.

Ndipo, taonani, mkazi wa Kenani anabwera kuchokera ku magombe omwewo, ndipo anafuulira kwa iye, kuti, Ndichitireni ine chifundo, O Ambuye, inu mwana wa Davide; mwana wanga wamkazi wazunzika kowopsya ndi mdierekezi.

Koma iye sanamuyankhe iye mawu. Ndipo ophunzira ake anabwera ndipo anamupempha iye, kuti, Muuzeni iye apite; pakuti iye akutiririra ife.

Koma iye anayankha ndipo anati, Ine sindinatimidwe koma kwa nkhusa zotayika za nyumba ya Israeli.

Ndiye anabwera iye ndipo anamupembedza iye, akuti, Ambuye, ndithandizeni ine.

Ndipo iye anayankha ndipo anati, Icho sichoyenera kutenga mkate wa ana, ndi kuvuponyera iwo kwa agalu.

Ndipo iye anati, Zooni, Ambuye: komabe agalu amadya... zinyenyetswa zimene zagwa kuchokera pa gome la mbuye wawo.

Kenako Yesu anayankha nanena kwa iye, O mkazi, chikhulupiriro chako ndi chachikulu: zikhale kwa iwe monga iwe wafunira. Ndipo mwana wake wamkazi anachira kuchokera ora lomwelo.

²³ Tsopano, mmawa uno ife tikufuna kuti tiyankhule pa chikhulupiriro. Tsopano, phunziro langa mmawa uno ndi: *Khama. Khama zimatanthauza* “ku—kukhala wolimbikira, kukhala ndi cholinga.” Tsopano, “Chikhulupiriro ndi thunthu la zinthu zoyembekezeredwa, umboni wa zinthu zosawoneka.”

²⁴ Ife tiri nalo thupi lathu, ndipo umunthu wathu kuno uli ngati mbewu. Ndipo mbewu kunjako imakhala ndi chikhakha; mkati mwa chikhakhacho mumakhala chikhokho, kapena chamkati, ndikhululukireni ine; ndipo mkati mwa chamkati mumakhala nyongolosi. Umo ndi momwe ife tiriri: thupi, solo, mzimu. Tsopano, kwa thupi muli zokhudzira zisanu: kupenya, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva. Kwa solo muli chikumbumtima, ndi zina zotero, njira zisanu kwa iyo.

²⁵ Mkatimo muli imodzi, njira imodzi. Ndipo njira imeneyo ndi malo omwewo amene Mulungu anamuikira munthu aliyense kuchokera kwa Adamu ndi Eva, chifuniro-chayekha. Iwe udzafuna kukhala moyo kapena udzafuna kufa, imodzi iliyonse imene iwe ukufuna. Ndizo, iwe unayikidwa pa ufulu wakudzisankhira, ndipo mzimu uliwonse umene umawulola kuti ukulamulire udzabala zipatso, moyo wako udzalamuliridwa

ndi mkati. Ndipo chikhulupiriro . . . Anthu ambiri amadalira pa mphamvu zisanu izi kunjaku. Izo ndi zabwino, palibe chotsutsa izo, ngati izo zikugwirizana ndi mphamvu ya chisanu ndi chimodzi iyi. Solo iyi . . . mzimu uwu ukhoza kokha kukhala wa mitundu iwiri, umodzi wa iwo ndi Mzimu wa Mulungu, winawo ndi mzimu wa mdierekezi. Iwe sungakhoze kutumikira mabwana awiri pa nthawi imodzi. Iwe umadzipereka kwathunthu kwa mmodzi kapena kwathunthu kudzipereka kwa winayo. Ndipo ngati uli ndi Mzimu wa Mulungu mwa iwe, uli nacho chikhulupiriro, ndipo udzakhulupirira Mawu aliwonse amene Mulungu anawalemba. Ndipo ngati ulibe, ukhoza kukhala . . .

²⁶ Tsopano, mdierekezi sali monga anthu ena amaganizira, “iye ndi waliuma ndi chirichonse,” koma iye ndi wachinyengo. Mdierekezi amakupangitsa iwe kuganiza kuti ukulondola. Koma pamene ukutsutsana ndi Mawu, zimenezo zimasonyeza kuti si Mzimu wa Mulungu, chifukwa Mzimu Woyera unalemba Baibulo. Ndiyeno izo ziyenera kukhala zogwirizana ndi Mawu. Ndipo kumbukirani Lamlungu lapitali, kusakhulupirira kumodzi kokha mu Mawu a Mulungu. Eva, Satana anamuuzza iye choonadi, ndipo iye sanawakane konse Mawu kukhala owona, koma gawo limodzi laling’ono ilo la Mawu linayambitsa vuto lonse ili. Mkaziyo sanawakhulupirire Iwo chifukwa iye anali akusaka nzeru mmalo mokhala ndi Mawu. Pamene Mulungu anena chirichonse, miyamba ndi dziko lapansi zidzapita koma Mawu Ake sadzapita konse. Mawu a Mulungu ayenera kukwaniritsidwa pa dontho. Kungofikira pa mutuwo ndi kulemba, Iwo ayenera kukwaniritsidwa.

²⁷ Tsopano, khama, kukhala wolimbikira, kuyesetsa kuti upange cholinga, kuyesetsa kutero, iwe umakhazikitsa malingaliro ako pa chinachake, ndipo ndiwe—iwe wolimbikira mu zimenezo chifukwa ukukhulupirira kuti ndi chinthu chimene ukuchifuna, ndipo iwe umakhulupirira kuti ukhoza kuchipeza icho. Tsopano, [M’bale Branham akukonza kummero kwake—Mkonzi]. (Mundikhululukire ine.) kukhala wolimbikira, iwe uyenera kukhazikitsa malingaliro ako tsopano izo zomwe uti uchite. Tsopano, iwe sungakhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu popanda kuwadziwa Mawu a Mulungu kapena kudziwa chinachake chokhudza Mulungu.

²⁸ Tsopano, winawake atakuuzani inu, “Ngati mutapita kukakhudza chikhomo icho, inu mukhala bwino. Inu mukudwala.” Ine sindingakhulupirire zimenezo. Inu mukhoza kuchita zimenezo. Koma zimenezo ndi zamphamvu pang’ono kwambiri kwa chikhulupiriro changa. Ine—ine sindikukhulupirira kuti muli ukoma uliwonse mu chikhomo chimenecho, mosaposa momwe ine ndimakhulupirira kuti mungakhale ukoma mu chosemedwa kapena chosemedwa kapena mtanda, kapena chinachake chonga izo.

²⁹ Ine ndimakhulupirira ukoma uli mwa Khristu, ndipo Khristu ndi Mawu. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Tsopano, Mawu Iwoeni akubweranso mmawonekedwe a Mzimu Woyera, mwa ife, ndipo Iwo ndi Mawu mwa inu. Mulungu mwa inu. Ambiri amafuna kulozera Mulungu ku chinthu china chachinsinsi njira ya kutali, kapena kutali kwambiri iwo amachidutsa icho. Mulungu ali mwa inu. Chiyembekezo cha Ulemelero, Khristu, malingaliro omwe anali mwa Khristu, mwa inu. Inu mukufikira kutali kwa izo, kuyesera kuti mutenge chimene chinaperekedwa kwa inu. Mulungu, mwa munthu! Zonse...

³⁰ Khristu, pamene Iye anali pa dziko lapansi, linali thupi la Mulungu. Mulungu analenga thupi ili. Ilo linali thupi losiyana, komabe ilo linali thupi la munthu. Inu mukudziwa, Solomoni anamumangira Iye nyumba. Koma Stefano anati, “Komabe Wammwambamwamba samakhala mnyumba zopangidwa ndi manja, koma thupi Inu mwandikonzera Ine.” Tsopano, Mulungu anadzikonzekeretsa Yekha thupi mmawonekedwe a Ambuye Yesu, amene anali Khristu, kutanthauza Iye wodzozedwayo. Ndipo, tsopano, zonse zimene Mulungu anali, zinali mwa Khristu, Iye anali chidzalo cha Umulungu mthupi. Ndicho chimene Lemba limanena. Tsopano, ndipo zonse zimene Mulungu anali, Iye anazitsanulira mwa Khristu. Iye anali Immanueli, Mulungu nafe!

³¹ Ndipo zonse zimene Khristu anali, Iye anazitsanulira mu Mpingo. Ndi chiyani chimenecho? Wodzozedwayo, kuti adzapitirize ntchito Yake kuti Mawu Ake akakhoze kukhala moyo mowirikiza. Iye ankakhala moyo ndi Mawu a Atate. “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu aliwonse amene akutuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Ndipo Mpingo sumakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu a Khristu. Ndipo Mzimu Woyera umabweramo ndipo umatenga Mawu a Khristu ndi kuwapanga Iwo kuchita kwamoyo lero. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.”

³² Mwaona, Mulungu sangakhoze kusintha. Ngati Mulungu apanga konse chigamulo, icho chiyenera kukhalabe mwanjira imeneyo. Ngati Iye asintha, ndiye Iye ndi munthu monga ine ndiriri, Iye—Iye ndi munthu chabe yemwe angakhoze kulakwitsa. Koma Iye ndi wopandalire! Chotero, ndipo Iye ndi wopandalire ndipo Iye—Iye ndi wamphamvuzonse, ndipo Iye sangakhoze kulakwitsa ndi kukhala Mulungu. Chotero chigamulo Chake choyamba...Pamene munthu anachimwa Iye—Iye anamukhululukira iye pa maziko a kukhulupirira Mawu Ake. Munthu wachiwiri akubwera, Iye ayenera kumachita mwanjira yomweyo kapena Iye anachita molakwitsa pamene

Iye anachita nthawi yoyamba. Ngati munthu anachiritsidwa ndi machiritso Auzimu, mwa chikhulupiro mwa Mulungu, Iye anapereka izo kwa munthu woyamba, ngati munthu winayo abwera, Mulungu ayenera kuti adzachite mwanjira yomweyo ngati izo zikumanzidwa pa maziko omwewo. Ngati Iye akanati asatero, Iye ndi wolemekeza wa munthu ndipo akusonyeza kukondera, zomwe ndithudi sizingamupange Iye Mulungu. Mukuona?

³³ Iwe uyenera kukhala ndi chikhulupiro mu chimene iwe ukuchita. “Ndipo ngati mtima wanu sukutitsutsa ife.” Ngati iwe tikudziwa kuti Baibulo limatiphunzitsa ife chinachake ndipo ife nkulephera kuchita zimenezo, ndiye kuti pali chinachake chimene ife sitingakhoze kukhala nacho chikhulupiro. Mwaona, iwe—iwe sungadziyike wekha pamodzi, chifukwa iwe ukudziwa kuti pali zinthu zina pamenepo zimene Mulungu amaphunzitsa, zomwe sungagwirizane nazo. Ndipo pamene uchita zimenezo, ndiye uli pati? Inu mwaona, iwe—iwe sungakhoze kukhala ndi chikhulupiro pa chimene ukubwerako. Inu sungakhoze kubwera kuno ndi kudzati, “Ine—ine—ine, usiku wathawu ine ndinali uko woledzera, ndipo, Ambuye, ine ndikufuna kuti Inu mundichiritse ine mmawa uno. Ine—ine, ine ndi—ine sindimwa mochuluka kwambiri.” Inu uyenera kudzipereka wekha, uyenera kudzipereka wekha kwathunthu kwa Mulungu. Uyenera kumvera chidutswa chirichonse cha Mawu. Kudzigulitsa kwathunthu ndiyeno ukatero utenge Mawu. Mawu amenewo ali mu mpingo. Iwo ndi Mawu amoyo.

³⁴ Baibulo linati, “Mawu ndi mbewu imene wofesa anapita kukafetsa.” Tsopano, iwe sungayembekezere kuti wafetsa chisoso ndipo nkukapeza tirigu. Ngati wafetsa tirigu, iwe ukolola tirigu. Ngati wafetsa chisoso, iwe ukolola chisoso. Chotero, uyenera kukhala ndi Mawu a Mulungu.

³⁵ Ndipo palibe wokhulupirira ati adzawaike konse Mawu a Mulungu penapake mmbuyo, sadzamupanga konse Iye wofooka kapena wambiriyakale—Mulungu wambiriyakale. Iye ndi Mulungu wambiriyakale, ndithudi, koma “Iye ali yemweyo,” Baibulo linati, Aheberi 13:8, “yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse.” Chotero, mochuluka basi monga Iye anali mu mbiriyakale, Iye ali lero. Iye sangakhoze kutaya mphamvu Yake. Ndipo pamene kufooka kuli kumene kunagwera mmpingo yathu, pachiyambi, mu mpingo woyambirira wa atumwi. Ndipo kodi ife tinachita chiyani? Ife tinayamba kuwutenga mpingo umenewo ndi kumaphwasula chiyanjano ndi kupanga anthu amipatuko osiyanasiyana ndi mabungwe, mpaka ife tazifikitsa izo mpaka ku chisokonezeka chachikulu chachabechabe. Kubwerera ku Mawu! Kubwerera kwa Mulungu! Kubwerera ku Mawu amoyo!

³⁶ Baibulo limenelo silimabereka chirichonse chimene

Ilo likunena kuti Ilo liri, pa lonjezo lirilonse, ine ndiribe chikhulupiriro chirichonse mwa Ilo. Koma Mawu oyamba omwe amene anati, “Idzani kwa Ine nonse inu olema ndi othodwa,” pamene ine ndinawayesa iwo, iwo anali choonadi. Ndiye kodi Awa ndi Mawu kapena kodi Iwo si Mawu? Ngati Iwo ali Mawu, Iwo ayenera kubala chirichonse chimene Iwo analonjeza. Ngati sichoncho, ndiye izo... Chimene chiri cholondola ndi chimene chiri cholakwika? Zonsezo ndi Mawu a Mulungu kapena, kwa ine, palibe chimodzi cha izo ziri. Palibe kapena zonsezo, chimodzi. Chotero ine ndikukhulupirira Iwo, langizo lirilonse, mzere uliwonse, kuvomereza kulikonse, chopumira chirichonse, kaphatikizidwe kalikonse, ine ndikukhulupirira chinthu chonsecho ndi Mawu a Mulungu. Ndikapachikapo solo yanga pa Iwo!

³⁷ Osati kukhudza mtengo, kukhudza chinachakenso, kapena chosemedwa, kapena mwamuna wina kapena mkazi wina; Ine ndimakhulupirira mu kumukhudza Mulungu kupyolera mu kukhulupirira Mawu Ake, kupyolera mu chikhulupiriro. Ndiye pamene inu muchita zimenezo, Mawu amenewo amakhala mwa inu moyo, Mawu omeretsedwa. Ndipo amodzi aliwonse a Mawu a Mulungu amamera. Chinthu chokhacho, kuti mutenge tirigu wodzaza mdzanja ndi kumugwira iye apa pa nsanja, iye sadzapanga konse kalikonse akakhala apa. Iye ayenera kulowa mu nthaka. Osati mnthaka yokha, koma mnthaka yoyenera kuti amuthandizire iye. Ngati Mawu abwino agwera mu nthaka yosauka, iwo adzabweretsa mbewu yosauka. Inu mutenge mbewu yabwino ndipo muiyike iyo mu nthaka yabwino, pa chikhulupirira choyenera iyo idzabala ka handiredi. Chomwechonso Mawu a Mulungu pamene Iwo abweretsedwa mu mtima wa munthu, ndi chikhulupiriro, chikhulupiriro chosafa mwa Ambuye Yesu Khristu, ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu ya Mulungu pamenepo kuwathirira Iwo, Iwo adzamera ndi kubala chirichonse chimene Iwo anati Iwo akanadzachita. Iwo ndi Mawu. Iwo—Iwo ndi Mawu a Mulungu.

³⁸ Yesu anati, Yohane 14:12, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuchita iyenso adzazichita.” Bwanji, ndithudi! Ine ndimakhulupirira zimenezo. “Ntchito izi zimene Ine ndikuchita,” kumasulira kolondola kwa izo, “zochuluka kuposa izi inu mudzazichita.” Ilo limati, “Zazikulu kuposa izi inu mudzazichita.” Inu simungakhoze kuchita zazikulu; Iye anaimitsa chirengedwe, Iye anaukitsa akufa, Iye anachita chirichonse. Koma, mwa kuyankhula kwina, Mulungu anawonetseredwa mwa Munthu mmodzi, Khristu, tsopano Iye akuwonetseredwa konsekonse mu Mpingo Wake. “Zochuluka kuposa izi,” ntchito zomwezo.

³⁹ Winawake ananena kwa ine osati kale litali, kuti ndikhale wotsutsa pang’ono, anati, “‘Ntchito zazikulu,’ Iye anati, ‘inu mudzazichita.’ Ife timachita ntchito zazikulu.”

⁴⁰ Ine ndinati, “Uzichita zazing’ono iwe usanachite zazikuluzo. Ungondisonyeza ine ntchito zazing’onozo.” Inu mukhoza kuwapanga Iwo, kuwapotoza Iwo mozungulira ndi kuyesetsa kuwapanga Iwo kunena chinachake, komabe Iwo nkukhalabe omwewo. Ndipo inu mumuwone aliyense amene ali ndi chikhulupiriro chokwanira kuti akhulupirire zimenezo, Iwo adzadziwonetsera Okha mwanjira yomweyo imene Mulungu anachitira izo. Tsopano ife tiri nazo zochuluka kwambiri lero pansu pa zotengeka, ndi zina zotero, izo, ndi zinthu, Ine ndiribe kanthu koti ndinene motsutsa zimenezo, izo ziri pakati pa munthuyo payekha ndi Mulungu.

⁴¹ Koma, kwa ine, mawu aliwonse, chochitika chirichonse chiyenera kubwera kuchokera mu Baibulo ili. Iwo ayenera kukhala Mawu a Mulungu, zikatero ine ndikudziwa kuti ndi zooni. Ngati Mulungu, Baibulo, limawathandizira iwo ndi kuti iwo ndi owona, ndi lonjezolo, ndiye kuti ndi Choonadi. Ndi winawake amene wapeza chikhulupiriro, amene amaima pamenepo pa Mawu amenewo ndi kuwapanga Iwo kukhala amoyo kachiwiri. “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Pamene tiziwona zimenezo mu lonjezo la Mulungu, ndiye ife timakhoza kukhala olimbikira. Ife tikhoza kukhulupirira kwenikweni, kukhala pamenepo chifukwa ndi lonjezo la Mulungu. Kukhala kumene ndi zimenezo mosalabadira kuti zitenga nthawi yayitali bwanji, izo zidzatulutsa.

⁴² Inu mukudziwa, Iye anayankhula nthawi ina za mbewu ya mpiru, kapena chikhulupiriro ngati njere ya mpiru, yaing’ono kwambiri. Mbewu ya mpiru imakhala pakati pa mbewu zazing’ono zochepetsetsa zomwe ziripo mu dziko lapansi lero. Koma ndi chiyani iyo? Iyo siyingasakanizikane ndi kalikonse. Mbewu ya mpiru siyidzasakanizikana ndi ina iliyonse. Inu mukhoza kutenga kale ndi sipinachi, ndi kupanga repu ndi zina zotero, ndipo inu mukhoza kubweretsa zinthu zosiyanasiyana posakaniza mbewu. Koma mpiru sumasakanizidwa, iwo amandiuza ine kuti inu simungakhoze kumusakaniza iye ndi kalikonse. Iwo ndi mpiru, ndipo umakhalabe mpiru.

⁴³ Ndipo pamene munthu atenga Mawu a Mulungu, ziribe kanthu momwe chikhulupiriro chimenecho chiriri chaching’ono, koma ngati icho sichisakanikirana ndi kusakhulupirira kulikonse, icho chidzamubweretsa iye ku Kuwala. Ena a ife tiri ndi chikhulupiriro chachikulu chimene chidzangochita zozizwitsa. Ena ali ndi chikhulupiriro choti azingogwiritsitsabe mpaka icho chitachitika. Koma ngati icho chiri chikhulupiriro chenicheni, chikangogwira kamodzi zimenezo, palibe chimene chingakugwedezeni inu kwa icho. Icho sichingasakanizike. Ndiye munthu ameneyo amalimbikira. Iye amakhala wakhama. Ziribe kanthu kuti ndi anthu anganene kuti, “Masiku a zozizwitsa anapita,” iye samazikhulupirira izo. Iye

amagwiritsitsabe chifukwa iye wakwaniritsa zikhaliidwe ndipo wawamiza Mawu amenewo mu mtima wa chikhulupiriro umene umawakhulupirira Iwo. Pamenepo iye amakhala.

44 Ine ndikudziwa zimenezo. Ine ndawonapo khansa ya sarcoma ikuchoka pa anthu, ndipo ogontha, osayankhula, ndi akhungu, konsekonse, kuzungulira dziko lapansi, akufa kuwuka, ndipo ine ndikudziwa kuti ndi zooni. Kulondola! Kugwira ntchito pa masomphenya, ndithudi, ndiye iwe nkumadziwa. Ndiye iwe nkumadziwa chomwe chiri chifuniro cha Mulungu. Iwe sungakhoze kugwira ntchito mpaka utadziwa chifuniro cha Mulungu. Lonjezo mu Baibulo limene limakuuzani inu chinthu chinachake, ndicho Mawu a Mulungu. Ndiye Iye amatumiza Mzimu Wake kubwerera mu mpingo mwa mphatso, kuti adziwonetsere Yekha kuti athetse kusiyana pang'ono ndi zina zotero, kuti adzipange Yekha kukhala weniweni pakati pathu. Oh, chiyani, ife tingapemphe bwanji chirichonse chosiyana, mukuona? pamene Iye akubwera kwa ife ndi kudzipangitsa Yekha kudziwika kwambiri, anadzipangitsa Yekha munthu, Mulungu pakati pa anthu Ake.

45 “Kanthawi pang'ono ndipo dziko,” dziko, pali mawu a Chigriki, *kosmos*, amene amatanthauza “dongosolo la mdziko.” Ilo lidzamira. Dongosolo lirilonse la dziko liyenera kumira, fuko lirilonse limene likulamulidwa ndi Satana. Nthawizonse zakhala ziripo ndipo nthawizonse zidzakhala ziripo, kunja kwa Israeli, pamene iwo adzakhala fuko. Satana anamutengera Yesu pamwamba pa phiri, anati, anamusonyeza Iye maufumu a mdziko, zonse zimene zinali ndipo zikanadzabwera, anati, “Ine ndi—ine ndidzawapereka iwo kwa Inu ngati Inu mungagwere pansu ndi kundipembedza ine.”

46 Iye anati, “Choka apa, Satana.” Iye ankadziwa kuti Iye adzakhala wolandira wa iwo mu Zakachikwi. Koma mmodzi aliyense. . . Ine ndinayima pamene Afarao nthawi ina ankalamulira dziko, odziwika, ndipo iwe umayenera kukumba mapazi twente pansu pa nthaka kuti ukawapeze maufumu amenewo, mipando yawo pamene iwo ankakhalapo, Kaisala wa ku Roma ndi—ndi Afarao aku Igupto, zinthu zonse izi. Ndipo ngati dziko lingapitirire, momwemonso ma demokalase awa adzakhala. Koma pali. . . kodi iwo onse amayankhula za chiyani? Chinachake mu mtima wa munthu kuyesera kuti apeze umodzi umenewo.

47 Ndipo ngati inu mutangoyang'ana mmwamba, umodzi umabwera kuchokera kwa Mulungu, mphanvu ya Mulungu. Pamene wokhulupirira, chirengedwe kuno pa dziko lapansi chimene Mulungu wachilenga, chalumikizana ndi Mulungu, kenako pamabwera umodzi ndikudzapereka chikhulupiriro. Ndipo pamene munthu awona zimenezo, iye amakhala wolimbikira, palibe chimene chingamugwedeze iye.

48 Yesu ananena pamenepo, “Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita. Kanthawi pang’ono ndipo dziko, *kosmos*, silidzandiwonanso Ine.” Ndiro dongosolo la mdziko, “Iwo sadzandiwonanso Ine.”

49 Mamembala ambiri a mpingo, anthu abwino amapita ku tchalitchi, amakhala pansu pa lingaliro limenelo kuti iwo ali bwino. Bwanji, inu simuli bwino ngati membala wa mpingo. Ndinu mzika. Inu mukhoza kuyesera kuchita molondola, koma, mzanga, ndiroleni ine ndikuuzeni inu, inu muyenera kubadwa mwatsopano. Inu simumabwera mu Mpingo, inu simumabwera mu Mpingo pogwirana chanza, inu simumabwera mu Mpingo mwa umembala wa mpingo. Inu mumabwera mu Mpingo mwa kubadwa.

50 Ine ndakhala ndiri m’banja la a Branham zaka fifite-thuu, iwo sanandifunsepo ine kuti ndijowine banjalo kuti ndipange dzina langa kukhala Branham. Ine ndinabadwira m’banja la a Branham. Ndine Branham mwa kubadwa.

51 Ndipo umo ndi momwe inu muliri Mkhristu, mwa kubadwa, pamene inu mwabadwa mwa Mzimu wa Mulungu. Kulimbikira! Inde, ndipo pamene inu mungathe kukwaniritsa chinachake. Amuna onse kudutsa m’mibadwo nthawizonse akhala okhoza kukwaniritsa zimene . . . Iwo amakhala olimbikira ngati iwo ali—ngati iwo ali ndi chikhulupiriro mu chimene iwo akuyesetsa kuti achikwaniritse. Izo zimatengera chimene kupindula kwanu kuli. Zimatengera chimene iwe ukuyesera kuti uchite, kaya ndiwe wolimbikira kapena ayi, ndi chikhulupiriro chochuluka bwanji chimene iwe uli nacho mu zimene iwe ukuchitazo. Ife tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Ife tiyenera tizimukhulupirira Mulungu.

52 Ine ndiri nawo Malemba ambiri ndalemba apa amene ine ndikufuna kulozerako. Tsopano, ngati munthu akuyesetsa kuti akhale wolimbikira, ndipo iye—iye ayenera kukhala ndi chinachake choyamba chimene chingamupatse iye chikhulupiriro mu zimene iye akuchitazo. Tsopano ife tikukumbukira, pakuyamba pomwe, Baibulo limatiuza ife kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Tsopano, kumbukirani zimenezo. Mulungu, pamene Khristu anali pa dziko lapansi, Iye anati, “Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita.” Marko 16, anati, “Pitani inu ku dziko lonse.” Kuyankhula kotsiriza kumene Yesu anapereka kwa mpingo. Mvetserani.

53 Kutuma koyamba kumene Iye anayamba wawupatsa Mpingo Wake, kunali, pitani m’ Mizinda Iye asanabwere, Mateyu 10, ndipo kuti “mukachize odwala, kuyeretsa akhate, kuwukitsa akufa, kutulutsa mdierekezi, ndipo monga mwaulere inu munalandirira, mwaulere muperekenso.” Kumeneko kunali kutuma Kwake koyamba kwa Mpingo.

⁵⁴ Kutuma kotsiriza, kapena mawu otsiriza amene anagwa kuchokera pa milomo Yake pamene Iye anakwera mmwamba, mpaka Iye adzabwerenso ndi mfuu, Liwu la Mngelowamkulu, Iye anati, “Pitani mdziko lonse, mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye amene akhulupirira nabatizidwa adzapulumutsidwa. Iye amene sakhulupirira adzalandidwa, ndi. . .” Ndi ndi cholumikizira, kulumikiza chiganizo chanu pamodzi. “Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa adierekezi, adzayankhula ndi malirime atsopano. Ngati iwo atatola njoka kapena kumwa zinthu zakupha, izo sizidzawapweteka iwo. Ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Baibulo linati, “Iwo anabwerera akusangalala, Ambuye akugwira nawo ntchito, kutsimikizira Mawu ndi zizindikiro zikutsatira.” Mukuona? Iwo anali. . . Iwo anali olimbikira mu izo chifukwa iwo anali ndi chinachake choti apindule. Iwo anali nako kutuma kolunjika. Kodi kutuma kumeneko kunali mpaka kuti? Ku dziko lonse, kwa cholengedwa chirichonse. Ndi mibadwo ingati? M’badwo uliwonse, cholengedwa chirichonse.

⁵⁵ Petro ananena, pa Tsiku la Pentekoste, “Lapani, mmodzi aliyense wa inu. Mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezo liri kwa inu ndi kwa ana anu ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.” Mungawuyike bwanji Mzimu Woyera ndi mphamvu ya Khristu kumbuyo mu zina (pafupifupi mbiri yakale) kutali mmbuyo mu kam’badwo kena kumbuyo uko? Mulungu ankadziwa kuti iwo akanati adzanene zimenezo. Ndi chifukwa chake Iye anati, “Ine sindidzakusiyani inu opanda chithonhozo. Ine ndidzapemphera Atate akutumizireni inu Mtonthozi wina, Mzimu Woyera. Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine pakuti Ine. . .” Ndipo *ine* puronauni ya umwini. “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumalekezera a chimaliziro.” Amen. Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mulungu akukhala mu Mpingo Wake, mwa anthu Ake.

⁵⁶ “Chipembedzo chiti, M’bale Branham?” Iye samakokera zingwe pa chipembedzo. Mulungu amachita ndi aliyense payekha. Mwamuna aliyense, mkazi aliyense, mnyamata kapena mtsikana amene ati akhulupirire pa Iye. Ziribe kanthu kuti iwowo ndi a chipembedzo chiti, Iye akusaka mitima ya njala.

⁵⁷ Tsopano, kulimbikira, kuyesetsa kuti apindulire chinachake. Anthu onse kudutsa mmibadwo yonse akhala ali mwanjira imeneyo. Tsopano ife titenge, ngati chitsanzo, Nowa. Nowa anali wolimbikira kwambiri iye atatha kupeza chifuniro cha Mulungu.

⁵⁸ Iwe uyenera poyamba kupeza chifuniro cha Mulungu. Tsopano, iwe uyenera kupeza chifuniro cha Mulungu mmawa

uno, pamene inu mukubwera kuti mudzapemphereredwe, inu muyenera mupeze chifuniro cha Mulungu, kaya ndi chifuniro cha Mulungu kuti akuchizeni inu kapena ayi. Ndipo chinthu chotsatira chimene inu mukuyenera kuchita, ngati inu mukubwera kudzapeza chipulumutso, inu muyenera kupeza ngati icho chiri chifuniro cha Mulungu kuti akupulumutseni inu kapena ayi. Chinthu choyamba chimene inu mukuyenera kuchipeza, chimene chifuniro cha Mulungu chiri. Ndiyeno, ngati inu munailandiradi mbewu mu mtima mwanu, ndiye inu mukhoza kukhala wolimbikira. Palibe chimene chingakusuntheni inu. Ziribe kanthu nzeru zimene munthu angayesere kunena, “Izo siziri chomwecho, ndipo si *izi* ndi *izo* ndi *zinazo*,” izo sizimakusunthirani inu dontho limodzi, chifukwa inu mukudziwa chimene chifuniro cha Mulungu chiri. Iye anayankhula izo mu mtima mwanu, kikhulupiriro chanu chimakhala pamenepo ndipo icho chidzagwirabe ngakhale ngati palibe choposa ngati njere ya mpiru. Iwo udzakuberetsani inu mpaka ku—ku malo. Chifuniro cha Mulungu. Inde.

⁵⁹ Nowa, iye atatha kumva Liwu la Mulungu likumuuzwa iye kuti kudzakhala kusefukira panadzabwera, kukubwera, mundikhululukire ine, chimene chikanati chidzawononge dziko lapansi, chirengedwe chikanati chidzadulidwe. Kodi Yesu sananene kuti, “Monga izo zinali mmasiku a Nowa, chomwecho izo zidzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu”? Chirengedwe chikanadzasokonezeka, ndipo ife tikuziwona izo lero.

⁶⁰ Ine ndikufuna ndiime apa kwa miniti. Pamene ine ndinali kubwera mu Bombay, kumene ife... Ambuye anatipatsa ife gulu lalikulu kwambiri limene ife tinayamba takhalapo nalo, faivi handiredi sauzande pa nthawi imodzi, kuti tiwalalikireko. Munali nkhanu mu nyuzipepala imene ine ndinali kuwerenga, inati, “A, chabwino, chivomezi chiyenera kuti chatha.” Anati, “Masiku pang’ono chisanafike chivomezi, zonse...” Mu India iwo ndi osauka, osawuka kwenikweni. Iwo amamanga mipanda yawo kuchokera ku miyala, ndi zina zotero. Ndipo mbalame zazing’ono zinkawuluka kuchokera mu miyala kuchokera ku zisa zawo ndi kumapita kunja mmunda ndi kukakhala mmitengo. Ng’ombe zimene zinkaima kuzungulira makoma ndi nyumba zazitali zitali, zinapita kunja mmunda mu dzuwa lotentha, sizinakaima mu mthunzi. Izo zinakaima mu dzuwa kunja uko. Iwo sanadziwe chomwe chinthu chachirendo ichi chinali. Ndiye, zonse mwakamodzi, chivomezi chinagwedezera makoma pansu, nyumba zazitali pansu. Ngati mbalame zazing’ono zikanakhala mmenemo, izo zikanaphedwa. Ngati ng’ombe zikanakhala zitaima pansu pa izo, izo zikanaphedwa.

⁶¹ Kodi inu simukumuwona Mulungu yemweyo amene anachenjeza mbalame ndi zamoyo mmasiku a Nowa? Ndipo nchifukwa chiyani inu mukufuna kuzitcha izo malangizo, kapena chirichonse chimene inu mukufuna kuti munene,

momwe Mulungu anachitira ndi mbalame izi? Iye anazipatsa izo kununkhiza kuti ziwuluke kuchokera pa khoma limenelo ndi kuchokako ku chinthu chimenecho icho chisanakanthe. Kodi inu mukuganiza kuti Mulungu amaganiza mokwanira za mpheta kuti iye anayichotsa iyo pa khoma, ndi mochuluka bwanji momwe inu muliri kuposa mpheta? Iye amadziwa momwe angasamalire Ake Omwe.

⁶² Mlongo wagona apa pa machira awa, machira, ngati Iye anadyetsa mpheta ndipo anawuveka munda ndi udzu, ndi mochuluka bwanji momwe Iye amaganizira za inu! Ndi mochuluka bwanji momwe inu muliri kuposa mpheta? Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu mosalabadira zomverera kapena china chirichonse. Ndi Mawu a Mulungu. Inu muchigwire Icho ndipo mugwiritsitse kwa Icho. Kulondola! Ndipo mukhale olimbikira, muwakhulupirire Iwo, mugwiritsitse ku Mawu Ake.

⁶³ Ndiye chivomezicho chitatha, mbalame zazing'ono zinawuluka kumabwerera, zinawulukira mmalo awo ndipo zinapanga miyala yawo kuti izo zikhoze kugwirako, kapena malo mmiyala kachiwiri, ndipo zinamanga chisa chawo; ng'ombe.

⁶⁴ Mulungu yemweyo amene anali mmasiku a Nowa. Nowa! Chabwino, inu mukuganiza kuti sayansi ikananena kwa iye. . . Iwo anali ndi sayansi yaikulu kuposa momwe iwo akuchitira tsopano. Iwo akanakhoza kukwaniritsa zokwaniritsa zazikulu kuposa zomwe iwo angathe tsopano. Iwo—iwo anali ndi utoto womwe umapangitsa kuti zinthu ziziwoneka bwino mpaka pano. Iwo anali ndi madzi owumitsira mitembo omwe iwo amakhoza kupanga matupi osavunda. Ife sitingathe kuchita zimenezo lero, ine ndimauidwa chomwecho. Ndiye ndi chinthu china, iwo ankamanga piramidi. Ndani angamange piramidi lero? Matanthwe aakulu amenewo apo amene ankayima pamenepo ndipo ankayang'ana mmwamba apo ndipo ankawona choimikidwa, ndipo, bwanji, zingatengere magalimoto ambiri kuti ayike phazi lake limodzi pamenepo. Kodi iwo ankanyamulira mmwamba chotani mathanthwe amenewo pamenepo? Kodi nkuti ankachita zimenezo? Mphamvu ya mafuta siyingachite zimenezo. Palibe chimene ife tiri nacho, kupatula icho chitakhala mphamvu ya atomiki, ndipo icho chikhoza kukhala chinthu chomwecho chimene chinayambitsa chiwonongeko cha chigumula zomwe zinaliponyera dziko kunja kwa kanjira kake ndi kuliponyera ilo kutali ndi dzuwa, kulikankhira ilo chammbuyo ndipo zinayambitsa mvula.

⁶⁵ Ngati Mulungu anati kudzakhala mvula, pakanati padzakhale mvula mosalabadira kuti inayamba yakhalapo kapena ayi. Ziribe kanthu ndi kutsimikizira kwa sayansi kungati komwe kunali kwa Nowa, Nowa anamva Liwu la

Mulungu, linati, “Ivumba mvula.” Ndipo apo panali isanayambe yavumbapo mvula pa dziko lapansi. Inu mukuona?

⁶⁶ Pamene Iye anamutengera Abrahamu pamwamba pa phiri, ndipo kumeneko anamuza iye kuti akapereke nsembe mwana wake yemwe. Ndipo pamene Abrahamu anamukonzekeretsa Isaki, ndipo Isaki wamng’ono anamufunsa. Chabwino choyimira cha Mulungu ndi Mwana Wake. Anammanga manja ake kumbuyo kwake. Iye anati, “Apa pali moto, ndipo apa pali nkhu, ndi zina zotero, apa pali miyala, apa pali guwa, koma nsembe ili kuti?”

⁶⁷ Ndipo bambo wokalamba uyo, tsopano pafupifupi usinkhu wa zaka handiredi ndi fortini, ali ndi mwana yemwe iye anali atamuyembekezera kwa zaka twente-faivi, kudutsa mu zovuta ndi zina zotero, ndi momwe iye anagwirira ku Mawu a Mulungu osafa amenewo, anali atabzalidwa mu mtima mwake, iye anali woti akhala ndi mwanayo mulimonse. Kodi iye anali chiyani? Kulimbikira. Iye anati, “Ine ndamugwira iye mpaka pano. Ine ndikudziwa kuti ngati Mulungu amupereke iye kwa ine pa kumukhulupirira Iye, Iye amuukitsa iye kwa akufa.” Ndi zimenezotu pamene. Kulimbikira, kugwiritsitsa Mawu a Mulungu amenewo poyamba.

⁶⁸ Ndipo, kuti, pamene iye anakonzeka kuti atenge moyo wake, panali Mngelo anagwira dzanja lake ndipo anawuimitsa mpeni. Ndipo apo panali nkhoa yamphongo itamangiridwa ndi nyanga zake, mu chipululu kumbuyo kwake. Kodi nkhoa imeneyo inachokera kuti? Iye anali ulendo wa masiku atatu, ndipo munthu aliyense tsiku limenelo amakhoza kuyenda mophweka mailosi twente-faivi. Ine ndimayenda twente-faivi ndi sarte nthawi iliyonse imene ine ndimapita kokasaka kapena kulondera, kapena chirichonse, ine ndimayenda mophweka mmenemo. Ndipo ife tiri nawo otchedwa mapazi a mafuta. Munthu ameneyo anayenda kuchokera ku ulendo wa masiku atatu, ndipo kenako anayang’ana kutali ndipo anawona phiri. Bwanji, zinyama zakuthengo zikanamupha mwanawankhosa ameneyo. Ndipo chinthu china, iye anali pamwamba pa phiri kumene kulibeko madzi ngakhale kalikonse. Nzosadabwitsa iye anawatcha malowo *Yehova-yire*, “Ambuye adzadzipezera Yekha nsembe.”

⁶⁹ “Iye angakhoze bwanji kuchita zinthu izi, M’bale Branham, mmasiku a sayansi, mmasiku a dziko lalikulu la sayansi? Iye angachite motani izi? Inu mukuganiza kuti Iye adzapitirira nazo chotani izi?” Iye akadali *Yehova-yire*, Ambuye. Ife timasunga Mawu Ake ndipo Iye ndi wokhoza kuchita icho chimene Iye ananena. Amen. Iye akhoza kuwutenga mpingo wakufa, wofunda wozizira, Iye akhoza kumutenga membala kuchokera mu mpingo umenewo ndi kuika Moyo wa Mulungu mwa munthu ameneyo, ndi kumuyatsa iye moto ndi Uthenga. Iye akhoza kumuchotsa hule pa msewu, Iye akhoza kutenga chidakhwa

kuchokera ku ngalande kutali uko, nkumupanga mwamuna ndi dona kuchokera mwa iwo, chifukwa Iye ndi Yehova-yire, “Ambuye adzadzipezera Yekha nsembe.” Amen.

⁷⁰ Momwe ife timamuikira Mulungu pansu pa maziko athu! Ife timaganiza pa maziko athu. Ife timakhulupirira pa maziko athu. Chimasuleni chinthu chimenecho. Ndicho chimene chinamufikitsa Eva mu vuto, iye anali kuganiza pa maziko ake omwe. Tiziganiza pa maziko a Mulungu, chimene Mawu Ake amanena. Muzidzikwezera nokha pamwamba pa zimenezo, mwa chikhulupiriro, kukhulupirira Mawu Ake.

⁷¹ Nowa anati, “Ine sindikusamala kuchuluka kwa momwe sayansi ingatsimikizire kuti kulibeko madzi kumwamba uko, Mulungu ndi wokhoza kuika madzi kumwamba kumeneko. Iye adzachita zimenezo chifukwa Iye analonjeza izo. Ngati Iye analonjeza izo, Iye adzazichita izo.”

⁷² Ndipo iye—iye, kodi iye anachita chiyani? Iye samangopita mozungulira ndi kuti, “Chabwino, Iye anandiuza ine zimenezo. Inde, ine—ine ndikukhulupirira izo zitero.” Iye anachita chinachake chokhudza izo. Oh, m’bale, mlongo, kodi inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Iye sanangokhala pamenepo ndi kumati, “Mulungu ananena chomwecho,” iye anachita chinachake chokhudza izo. Ngati inu mukufuna kuti mupulumutsidwe mmawa uno, Mulungu analonjeza chipulumutso. Ndiye muchite chinachake cha izo, osati mungokhala pamenepo. Osati kujowina tchalitchi chimodzi ndi kutenga kalata yanu kuchokera ku mpingo kupita ku mpingo. Iye analonjeza chipulumutso, chiwombolo.

⁷³ Ngati mukudwala, “Bwanji mwakhala apa?” Monga wakhate ananena tsiku lija pamene mzinda unazingidwa, “Bwanji ife tikhala pano mpaka ife titafa?” Pamene Samaria anazingidwa ndi Asiriya, iwo anati, “Ife takhala pano mpaka ife titafa, ife tidza—ife nthawizonse tizikhala kuno. Ife tifera pano. Ngati ife titapite mu msindawo, iwo akufa mmenemo ndi njala. Tiyeni tipite ku msasa wa mdani.” Oh, mai, ndi osauka bwanji... Ndi chikhulupiriro chaching’ono bwanji chimene iwo akanakhoza kukhala nacho. Ndi chinthu chaching’ono bwanji... Iwo anapita ku msasa wa mdani yemwe ankayesera kuti awaphe iwo. Koma anati, “Ngati titi tife, ife tifa mulimonse. Chotero ngati tipulumuke... ife tipulumutsa moyo wathu, bwanji, ife tichita bwino.” Ndipo iwo anapita kumusi uko, ndipo Mulungu analemkeza kachidutswa kakang’ono ako ka chikhulupiriro cha mdima. Ndipo osati kokha kuwawombola iwo, koma anawombola Israeli.

⁷⁴ Chimene ife tikusowa lero ndi amuna ndi akazi amene angamutenge Mulungu mwa Mawu Ake ndi kukhala akhama ndi Iwo. Mulungu adzapangitsa zivomezi ndi kugwedeza kuti apite

mu msasa poyamba. Mulungu adzasamalira kaya kukhala mvula kumwamba uko kapena ayi.

⁷⁵ Mukuti, “Chabwino, M’bale Branham, adokotala anandiuza ine kuti ndikufa. Ine ndiri ndi khansa.” Izo zikhoza kukhala chomwecho. Mwamunayo akukuuzani inu zonse momwe akudziwira. Koma, chinthu chokha chimene iye angathe kuchita, iye ali ndi zokhudzira faivi zoti agwire nazo ntchito, ziwiri za izo zimene iye angathe kuzigwiritsa ntchito. Ndi chiyani izo? Chokhudzira chimodzi kumverera, malo otsatira ndi—ndi kuwona. Kuwona ndi kumverera, iye akhoza kumverera chinachake, kapena kuwona chinachake kupyolera mu x-ray. Ndizo zonse zomwe mwamuna ayenera kugwira nazo ntchito. Ndizo zonse zomwe iye amadziwa, koma iye akuchita zonse zomwe iye angathe. Koma musamayang’ane pa zimenezo, iye wabwera kumapeto ake. Yang’anani pamwamba apa zomwe Izi zinalonjezedwa! Kuti, “Izo zingakhoze kuchitidwa motani?” Mulungu ananena chomwecho. Izo zikukhazikitsa izo pamene Mulungu ananena izo. Izo zikukhazikitsa, izo zakhazikika Mwamuyaya kwanthawizonse Kumwamba, Mawu Ake ali. Ndipo Mawu Ake anasandulika thupi, ndipo Iwo ali thupi lero mwa inu, ngati inu mungawalole Iwo kuti abwere thupi. “Ngati inu mukhala mwa Ine ndi Mawu Anga mwa inu, ndiye pemphani chimene inu mukufuna ndipo icho chidzachitidwa,” Yohane Woyera 15. Mwaona, ife tikufuna kungowalola Mawu amenewo kuti azikhala muno. Mukhulupirire izo, icho ndi choonadi. Iwo ndi mbewu, ndipo iyo—iyo idzakwaniritsa chirichonse chimene Iye analonjeza.

⁷⁶ Tsopano, zindikirani, za sayansi kukanabwera kumeneko, gulu la asayansi, ndipo anati, “Bambo Nowa, ndinu mtumiki wabwino. Ife—ife tikukuyamikirani inu. Inu muli ndi gulu labwino kuno, banja lanu, koma, ndipo komabe, ngati inu...ife sitimagwirizana nanu inu, ndipo ife tikudziwa kuti ndinu—ndinu wosinthika. Ndinu—inu mukungopangitsa kutentheka kuti kufetsedwe pakati pa anthu, ndipo inu mpaka mukuwawopsyeza ena a anthuwo, kumawauza iwo kuti dziko likufika ku mapeto. Ife tikufuna kuti tisonyeze ndi kutsimikizira mwasayansi kwa inu.”

⁷⁷ Oh, mdierekezi ameneyo sanafe konse. Iye—iye akungoyeserabe kuti achite zimenezo. Mmodzi yemweyo amene anati, “Ngati Inu muli Mwana wa Mulungu, mundilole ine ndiwone chozizwitsa. Muchite chozizwitsa ndipo mutembenuze mkate uwu, uwu. Inu muli ndi njala, mupange miyala iyi mkate, ine ndikukhulupirirani Inu.” Mdierekezi yemweyo mwa anembe ophunzira awo, anati, “Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, tsika pansu pa mtandapo ndi utsimikizire izo kwa ife.” Mukuona? Mdierekezi ameneyo satero, iye samafa basi. Mwaona, mdierekezi nthawizonse amatenga munthu wake koma mzimu wake umakhala kuno kwa wina. Koma ndiroleni

ine ndikuuzeni inu chirimbikitso china: Mulungu amamutenga munthu Wake koma Mzimu Wake umakhala pano kwa wina, nayenso. Inde. Winawake alandira Mawu amenewo. Winawake adzozedwa mwanjira ina kapena imzake. Izo zimatengera chimene iwe, mzimu umene uli mkati mwa njere iyi. Ndi ameneyo, inu mukhulupirira Izo kapena ayi kukhulupirira Izo. Ndizo, chabwino, inu simuli. . .

⁷⁸ Winawake ananena kwa ine osati kale kwambiri, mtumiki. Inu mukhala wodabwa. Ndipo ine ndinali mu ofesi ya dokotala pamene iye ankanenai zimenezo. Ndipo ine ndikukuuzani inu choonadi, ine ndinapeza madokotala okhulupirira kwambiri mu machiritso Auzimu kuposa omwe ine ndiri nawo atumiki. Uko nkulondola. Inde, bwana. Ine ndakhala ndiri pansu pa. . . Ine ndinafunsidwa, inu mukudziwa, pamenepo, pa chifukwa cha magazini ya *Look*, kapena osati *Look*, koma. . . Magazini aja anali chiyani amene analemba “Chozizwitsa cha Donny. . .?” *Reader’s Digest*. Eya. Ndipo pamene iwo anandifunsa ine uko kwa a Mayo Brothers, inu mukudziwa zimene iwo ananena? “Ife sitimadzinenera kuti ndife ochiritsa, ife timangodzinenenera kuti timathandizira chirengedwe. Alipo Mchiritsi mmodzi yekha, ndiye Mulungu.” Oh, mai! Ndi zimenezotu. Ndi munthu yemwe angakhoze kuganiza. Winawake yemwe angakhoze kuyang’ana kunja uko ndi kuyang’ana pa chinthu chonsecho. Ife ndife anthu. Ndife ogonjera ku imfa, zolakwitsa ndi chirichonse. Iye ndi Mulungu, wopandamalire.

⁷⁹ Ife tiyenera kukhulupirira izo. Ngati ine ndingakhoze kuzifotozoza izo, ndiye icho sichirinso chikhulupiriro. Ine sindingakhoze kufotozoza chifukwa chomwe ng’ombe yakuda ingakhoze kudya udzu wobiriwira ndi kupereka mkaka woyera, koma iyo imachita zimenezo. Uko nkulondola. Inunso simungathe kuzifotozoza izo. Ayi, bwana. Ine sindingakhoze kufotozoza momwe Mulungu amachitira zinthu izi, koma Iye anangoti Iye akanadzachita izo. Ine sindidzadziwa konse izo, inu simudzadziwa konse izo, koma ife tikuzikhulupirira izo. Mwa chikhulupiriro inu munapululumutsidwa. Mwa chikhulupiriro inu munachiritsidwa. Chirichonse chimene chimabwera, aponso, kuchokera kwa Mulungu, chiyenera kubwera mwa chikhulupiriro.

⁸⁰ Nthawi ina kale, nditaima pa kuwulutsa, munthu wina anali kuwuseka msonkhano, samadziwa yemwe ine ndinali. Iye anati, “Ine sindikukhulupirira Zimenezo.” Anati, “Izo sizingakhoze kuchitidwa. Ine sindingakhoze basi kuzikhulupirira Izo monga choncho.” Iye anati, “Ine ndiyenera kutero. . . Izo ziyenera kutsimikiziridwa mwasayansi kwa ine.”

⁸¹ Ine ndinati, “Ndiye iwe sungakhoze konse kukhala Mkhristu. Iwe sungakhoze konse.”

Iye anati, “Oh, ndine Mkhristu.”

82 Ine ndinati, “Iwe sungakhoze kukhala. Iwe sungakhoze.” Ine ndinati, “Mwasayansi utsimikizire kwa ine kumene Khristu ali.” Ine ndinati, “Kodi ndiwe mwamuna wokwatira?”

Iye anati, “Inde.”

Ine ndinati, “Kodi iwe umamukonda mkazi wako?”

Iye anati, “Inde.”

Ine ndinati, “Mwasayansi utsimikizire kwa ine chomwe chikondi chiri.” Iye, ine ndinati. . .

“Chabwino,” iye anati, “Ine sindingathe kuchita zimenezo.”

83 Ine ndinati, “Ndiye iwe ulibe kalikonse kamene ine ndimakatcha chikondi. Mukuona? Tsopano, iwe basi... iwe, ndicho chikhulupiro chodzipangitsa mmalingaliro mwako. Mukuona? Ngati iwe sungathe kutsimikizira zimenezo mwasayansi. Ndiuze ine chiyani... Pita kumusi kuno ndipo ukandigulire ine chikondi cha mtengo wa kotala. Ukandigulire ine chikhulupiro cha kobiri. Iwe sungakhoze kuchita zimenezo.”

84 Ndipo zida zonse za chikhulupiro cha Mulungu, chikondi, chimwemwe, mtendere, kupirira motalika, ubwino, kufatsa, kudekha, chipiro. Zida zonse za wokhulupirira ndi chikhulupiro. Ife timamukhulupirira Mulungu mwa chikhulupiro, chifukwa, Mulungu ananena chomwecho. Ndiye ndi chiyani chimenecho? Abrahamu analungamitsidwa, ndi Paulo, mwa chikhulupiro; koma, ndi Yakobo, mwa ntchito. Abrahamu anali kuyankhula zomwe Mulungu anaziwona, ndipo Yakobo anali kuyankhula zomwe munthu anaziwona. “Ndisonyezeni ine chikhulupiro chanu mwa ntchito zanu,” “popanda ntchito zanu,” ndi zina zotero. Mukuona? Ndiye ngati inu mulibe ntchito ndi chikhulupiro chanu, izo zisonyeza kuti inu mulibe chikhulupiro, inu mukungoyankhula kuchokera mkamwa mwanu. Koma ngati inu muli ndi chikhulupiro kwenikweni, inu mumakhulupirira izo ndi kumachita monga chomwecho. Uko nkulondola, muziyike izo mu kuchitapo!

85 Nowa anatero, iye anaziyika izo mu kuchitapo. Iye anapita patsogolo pomwe kukamanga chombo. Ziribe kanthu zomwe sayansi iliyonse inanena, “Tsopano, taonani apa, ife titsimikizira mwasayansi kwa inu kuti kulibeko mvula kumwamba uko.”

86 “Ine sindikusamala kuchuluka kwa momwe inu mungatsimikizire kwa ine, kuchuluka kwa momwe inu munganene izo mwa kafukufuku wa sayansi, kapena chirichonse chimene inu mukufuna kuzitcha izo, Mulungu wandiuza ine ‘Kukubwera mvula,’ ndipo ine ndikumukhulupirira Mulungu.” Ndi zimenezotu. “Ivumba mvula.”

87 “Kodi iyo ikuchokera kuti? Bambo Nowa, ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu, bwana, abusa, kodi mvula imeneyo ikuchokera kuti? Kodi iyo ili kuti?”

88 “Chabwino, Mulungu akhoza kuyiyika iyo kumwamba uko ngati Iye atandiuza ine kuti idzakhala kumeneko.” Kulondola!

89 Ndipo lero iwo akuti izi sizingachitike. Iwo amawona kuzindikira za mumtima mu msonkhano. Iwo amati, “Izo ziyenera kukhala kuwerenga maganizo.” Kuwerenga maganizo, kuwerenga maganizo? Kuzindikira kwa mzimu, kwa masomphenya a Ambuye! Ndi kuwerenga maganizo kwa mtundu wanji kumene aneneri anali nako? Kodi Yesu anali ndi chiyani pamene Iye anaima pamenepo tsiku limenelo?

90 Ndipo apa panabwera Filipino, ndipo iye anapulumsidwa ndipo anapita uko ndipo anakamutenga Nataniele, anamubweretsa iye pamaso pa Yesu, ndipo Nataniele anati, “Ah, tsopano sipangakhale kanthu kabwino kangabwere kuchokera—kuchokera ku Nazareti.”

91 Chotero pamene iye anafika kumene Yesu anali, Yesu anayang’ana pa iye ndipo anati, “Ndiwe—ndiwe wachi Israeli. Iwe ulibe chinyengo.”

92 Ndipo iye anati, “Rabbi, ndi liti pamene Inu munandidziwa ine? Inu munandidziwa ine bwanji?”

93 Anati, “Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo Ine ndinakuwona iwe.”

94 Tsopano, mwathupi, izo zinali... Ngati inu munayamba mwakhalapo kumeneko, ndi mamailosi fifitini kuzungulira phirilo. Malo awiriwa, ulendo wa tsiku kuzungulira phiri. Iye akanakhoza bwanji kumuwona iye? Ndiye chiyani? Pokhala munthu wa chikhulupiriro, pokhala munthu yemwe ankafuna kuti awawone Mawu a Mulungu akuwonetseredwa, ankafuna kuti adziwe kuti Mulungu anati, “Ambuye Mulungu wanu adzawukitsa, pamene Mesiya adzabwera Iye adzakhala Mneneri,” chimodzimodzi monga iye anachitira. Ndipo iye anawona zimenezo, ndipo iye anadziwa. Iye anati, “Rabbi, Ndinu Mwana wa Mulungu.” Uko nkulondola. Dzina lake ndi lachisavundi.

95 Koma apo panaima ansembe aakulu okhuthara awo amene anali ndi DD., Ph.D., ma LL.D ali kumbuyo kwawo, mwinamwake, anabwera kudutsa mzere wa atumiki atayima pamenepo, ankaganiza kuti iwo ankawadziwa Mawu. Iwo anatero, mawu, koma alipo ambiri amene sama... Osadziwa Mawu Ake, koma kumudziwa Iye, kumudziwa Iye amene ali mu Mawu. Uko nkulondola. Kumudziwa Iye, Moyo umene uli mu Mawu. Tsopano, iwo anayima pamenepo ndipo anati, “Munthu uyu ndi Bezezebule. Iye ndi wambwebwe. Iye amawona zinthu zimenezo. Iye—Iye ndi wambwebwe. Ndizo...”

96 Yesu anapotoloka ndipo anati, akudziwa. Tsopano dikirani, iwo sananene konse izo momveka, iwo ankaganiza zimenezo mu mtima mwawo. Ndipo Iye ankadziwa malingaliro awo. Kodi Baibulo limanena zimenezo? Luka Woyera. Eya, Iye

ankadziwa malingaliro awo. Mwaona, iwo ankaganiza kuti Iye anali kuwerenga maganizo awo. Anazindikira malingaliro awo. Iye anati, “Inu mukayankhula mawu motsutsa Ine, Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha zimenezo. Koma,” mwanjira ina, “tsiku lina Mzimu Woyera udzabwera kudzachita chinthu chomwechi, ndipo inu mukadzayankhula mawu amodzi motsutsa izo, inu mukadzayankhula motsutsa izo, izo sizidzakhululukidwa konse kwa inu mu dziko lino, ngakhale mu dziko likudzalo.” Mukuona?

⁹⁷ Mwaona, Mzimu Woyera, iwo sakanakhoza kuwumvetsa Iwo. Iwo ankayenera kuti awayankhe osonkhana awo, chifukwa osonkhana awo anali ataima pamenepo. Ndipo iwo anati, “Chabwino, Iye—Iye ayenera kuti akuwerenga maganizo awo. Iye ali nako kuwerenga maganizo. Iye ndi Bezezebule, wambwebwe.” Ndipo aliyense amadziwa kuti wambwebwe ndi wa mdierekezi. Ndipo iwo anaitcha ntchito ya Mulungu “mdierekezi,” kumadzitchula ntchito za Mulungu.

⁹⁸ Kodi inu simukudziwa kuti chirichonse chimene mdierekezi ali nacho ndi chinachake chimene chapotozedwa kuchokera kwa chenicheni? Bodza ndi chiyani? Ndi choonadi chopotozedwa. Chigololo ndi chiyani? Ndi kachitidwe kolungama kopotozedwa. Tchimo lonse ndi—ndi choonadi ndi chirungamo chopotozedwa. Kodi imfa ndi chiyani? Moyo wapotozedwa. Ndithudi, ndi momwe izo ziriri mu Mawu Ake. Umo ndi momwe izo ziriri, ndipo anthu amangoyesera kuzichitira mthunzi, kuzimphimba izo, kuzipanga izo kunena zinthu chifukwa iwo sakudziwa, iwo sakudziwa. Iwo alibe chikhulupiriro kuti atenge Mawu. Koma Nataniele anatero.

⁹⁹ Nanga bwanji Simoni pamene iye anabwera kumeneko? Anamumva Mfarisi wachikulire uja bambo wake, akuti, “Simoni, mwana wanga, nthawi yotsiriza isanafike, apo mwinamwake. . . Ine ndamuyembekezera Iye kuti abwera mmasiku anga, koma Iye sanabwere. Iye akhoza kudzabwera mu nthawi yako. Ndipo ngati Iye adzatero, Simoni, ichi ndi chimene chiti chidzachitike: Padzakhala chirichonse chikuchitika, mwana, ndipo padzakhala mitundu yonse ya zinthu zabodza zikuwuka paliponse. Koma udzakumbukire izi, udzakhale ndi Mawu. Mukuona? Tsopano, Mesiya uyu adzauka, Iye adzakhala Mneneri. Ndipo Mesiya uyu adzakhala Mneneri chimodzimodzi monga Mose anali, chifukwa Mawu athu a Mulungu amati Iye adzakhala Mneneri wonga iye. Tsopano, inu mudzadziwa kuti Iye adzakhala woposa Mneneri, Iye adzakhala Mulungu-Mneneri. Koma zochita Zake ndi mawu zidzakhala Mneneri, chifukwa iwe sungapite patali kuposa zimenezo mpaka iwe utapita kwa Mulungu. Mukuona?” Chotero iye anati, “Iye adza, Iye adzakhala Mulungu-Mneneri. Ntchito Zake kuno pa dziko lapansi zidzasonyeza Mneneri, kotero ife tikudziwa kuti izo ziri, uyo adzakhala Mulungu. Udzakumbukire zimenezo.”

100 Ndipo ine ndikuganiza pamene Andireya anabwera ndipo anadzamuuza iye usiku umenewo, “Oh, ife tinamuwona Mesiya,” ine ndikuganiza Simoni anati, “Choka, choka. Pita kutali. Ah, kazipitirira, usandivutitse ine.”

101 Koma tsiku lotsatira pamene iye anakhala nawo pa msonkhano, anayenda kupita mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu, ndipo Iye anati, “Dzina lako ndi Simoni, ndipo ndiwe mwana wa Yonasi.” Izo zinachotsa kukhuthala mwa iye. Kodi Iye anachita chiyani? Iye, Yesu...Nsodzi mbuli uja yemwe sankakhoza ngakhale kulemba dzina lake lomwe, Baibulo linati iye anali zonse mbuli ndi wosaphunzira. Koma chinamukomera Mulungu, ndi chikhulupiriro chimenecho, kuti amupange iye kukhala Petro, mwala wawung’ono, anamupatsa iye mafungulo aku Ufumu, “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga.” Chiyani, pa thanthwe monga Akatolika amanenera? Ayi. Pa chiyani, ndi chiyani chimenecho? Pa vumbulutso lauzimu. Mwaona, “Thupi ndi mwazi sizinaulule izi kwa iwe, koma Atate Anga amene ali Kumwamba awulula izi kwa iwe. Pa thanthwe ili, pa Mawu olembedwa a Mulungu kukhala akuwululidwa mwauzimu, ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka Iwo.” Bwanji? Ndi zoposa mbewu ya mpiru. Ndi mphamvu ya Mulungu ikuyenda pakati pa zivundi pa Mawu, Mawu opangidwa kukhala moyo.

102 Ndicho chimene chinali mwa Nowa. Iye anati...Mawu ali Moyo mwa iye. “Ndipo Ine ndikonzekera izo.”

103 “Chabwino, iyo siyinagwe dzulo. Inu munati ivumba mvula. Ndi liti pamene iyo iti ivumbe?”

“Ine sindikudziwa, koma mvula ivumba.”

“Inu mukudziwa bwanji kuti iyo ichita zimenezo?”

“Mulungu wanena chomwecho.”

104 Monga iwo ananena kwa Abrahamu, bwanji, usinkhu wa zaka eyite, iye; ndi mkazi wake, usinkhu wa zaka nainte. Mkazi wachikulire wamng’ono wosauka akuthamanga motsatira pamenepo, anali akulongeza mapini ndi zinthu za tinsapato tating’ono ta mwanayo, kwa zaka twente-faivi; apa iye ali nainte, pa ndodo yaying’ono yoyendera, monga *chonchi*, akuyendayenda. Abrahamu, nsana wopindika, ndi ndevu zikulendewera pansu. “Nanga bwanji zimenezo, Abrahamu? Hei, iwe unasiya—iwe unasiya mzinda wa Uri nthawi yaitali yapitayo. Iwe unati iwe udzakhala ndi mwana. Nanga bwanji izo tsopano?”

“Ulemelero kwa Mulungu, ife tidzakhala naye iye mulimonse!”

“Bwanji?”

“Mulungu wanena chomwecho!”

“Bwanji, izo zakhala ziri zaka twente-faivi zapitazo.”

¹⁰⁵ “Mulungu ananena chomwecho! Izo sizikupanga kusiyana kulikonse ngati ziri zaka handiredi ndi twente-faivi, Iye achita izo mulimonse!” Mukuona? Kulimbikira, khama, kuzilondoloza, kuzilondoloza pambuyo. Iweu wachigwira icho!

Monga mnyamata wamng'onoyo amawulutsa kaiti. Anati, “Ili kuti iyo?”

¹⁰⁶ Iye anati, “Ine sindikudziwa, koma iyo ili kunja uko kwinakwake, ine ndikukhoza kuimverera iyo pa mapeto a chingwecho.”

¹⁰⁷ Ndi zimenezotu. Mwamuna kapena mkazi amene amatenga Mawu a Mulungu, iwe wagwira chinachake. Nangula wako wagwira mkati mwa chopimba. Mkuntho ndi mphepo zamkuntho zikhoza kukankha ndi kugwedeza mwanjira iliyonse, koma iwe wakhazikika. Iye akubwera mpaka pamwamba pa malo pomwe. Iwe ukulimbikira. Iwe ukhulupirira Iwo.

¹⁰⁸ Nowa anakhulupirira Iwo, zedi, ndipo iye anapindula cholinga cha Mulungu kwa moyo wake. Kodi inu mukufuna kukwaniritsa cholinga cha Mulungu pa moyo wanu? Ndiye mukhale ndi khama pamene inu... kulimbikira pamene mwawapeza Mawu. Gwiritsitsani kwa Iwo, lonjezo, ndi lanu.

¹⁰⁹ Mose. Ndi anthu angati amene ine ndingapiteko tsopano! Ine ndikunena apa Mose, uko mu Eksodo, Mose, iye anali sikolala, kazembe, msilikari. Osati kokha msirikali, iye anali mkulu wa ankhondo. Iye si wamkulu wa ankhondo yekha, koma iye anali Farao wakudza. Ameni. Ine ndikumverera mwachipembedzo pakali pano, chotero mundikhululukire ine. Inde, Farao wakudza. Ngati iye akanafuna kuti awawombole anthu ake, chabwino, iye anali ndi Igupto m'dzanja lake. Iye anali Farao wakudza, iye akanadzachita zimene iye ankafuna kutero pamene iye anadzakhala Farao. Koma Mulungu anayankhula kwa iye, uh-huh, tsiku lina kutsidya mu chitsamba choyaka.

¹¹⁰ Oh, iye anathamanga ngati wamantha, ndi maphunziro ake onse. Fioloje yake yonse, iye analephera. Zinthu zake zonse zazikulu, iye analephera. Koma tsiku lina, mu chitsamba choyaka, Mulungu anakumana naye iye. Pamene Mulungu anabwera kwa iye mu chitsamba choyaka ichi, mpenyeni iye, ali ndi ndodo m'dzanja lake, mkazi wake ali pa bulu, ndi Geshomu wamng'ono atakhala pa ntchafu yake, ali pa ulendo wake waku Igupto. Kodi iye anali chiyani? Akupita uko kuti akalande. Iye anali, anali ndi khama, iye anali wolimbikira kwambiri.

¹¹¹ “Mose, kodi iwe ukuganiza kuti iwe, pa usinkhu wa zaka eyite, ndipo uli ndi ndodo yokhota m'dzanja lako, yowuma mmene iyo ingakhali?” Hum! Ndodo yokhotakhota, kuwukira kwa munthu mmodzi, akupita ku Igupto monga munthu mmodzi akupita ku Russia kuti akalande. Ife tikungosowa... Mulungu

amangosowa munthu mmodzi. Ndi zokhazo, Iye amangosowa munthu mmodzi kwathunthu m'dzanja Lake. Munthu mmodzi, ndizo zonse zimene Iye akuzisowa. Iye akhoza kumugwedeza Russia mzidutswa ndi munthu mmodzi ameneyo.

¹¹² Iye anamutenga Nowa, kapena Mose, mundikhulukire ine. Iye anamutenga Mose pamene iye anali kuthamangira mbali *iyi*, anakhazikika ku moyo wabwino, mtsikana wamng'ono wokondeka, anamukwatira iye, anali ndi mwana, akulowa cholowa cha nkhosa za mpongozi wake, Yatero, wansembe wa Midiyani. Iye anali ndi chirichonse chopangidwa. Anali ndi nyumba yabwino, malo, amakhala momasuka kunja uko, ndi kukasaka kamodzi mu nthawi ndi uta wake, mwinamwake, ndi kupha gwape, ndi zipatso zochulukana ndi nkhosa zochulukana, ndi ubweya ndi malonda, apaulendo amabwera akudutsako. Bwanji, iye anali atapanga izo, palibe chimene iye ankayenera kuti azidandaula nacho. Koma tsiku lina, tsiku lina kulemedwa kwa anthu, anali atawaiwala anthu amene anali akuvutika. Iwo anali uko mu Igupto. Iye anali atalephera, kotero Mulungu akhoza kuchita chinachake cha izo. Koma tsiku lina pamene Mulungu anakomana naye iye mu chisamba choyaka, inu mukuyankhula za khama, apa iye akupita!

“Ankhondo ako ali kuti?”

¹¹³ “Ine sindikufuna chirichonse. Ankhondo anga ndi ankhondo osawoneka.” Monga izo zinali ku Dotani mmawa wina, pamene mneneri. . . “Ankhondo anga ndi ankhondo osawoneka.” Apa iye akupita, chinthu chokha chimene inu mungakhoze kuwona ndi ndodo yokhotakhotakhota, ikutsogolera mphongolo iyi mmbuyo, ndipo ndevu zikuwuluka. “Mulungu alemekezeke!” Maso ake anakhala cha Kumwamba, akupita kumeneko kuti akalande.

¹¹⁴ Nthawizina chikhulupiriro chimakupangitsa iwe kuchita zopusa, kwa malingaliro achithupithupi. Koma ngati iwo ali Mawu a Mulungu, iwo ayenera kufika pokwaniritsidwa. Muzikhala olimbika, onani Mulungu anazipangitsa izo kukwaniritsidwa.

¹¹⁵ Iye anapita kumeneko, iye anali wolimbikira kwambiri. Anayenda nafika pamaso pa Farao, zinkawoneka ngati kuti alephera. Iye anati, “Ine ndikusonyeza iwe ngati ine ndatumidwa ndi Mulungu kapena ayi.” Iye anaponyera ndodo pansu monga *chomwecho*, ngati kuti tinene. . . ndipo inasanduka njoka; iye ndi Aroni. Ndipo iye anangoyitana akasidi awiri, kapena amuna awiri ogwidwa ndi ziwanda monga ife tiri nawo mmasiku otsiriza, akutsanzira bwino mwakuti ngakhale Osankhidwa omwe, ngati nkotheke. Uko nkulondola. Anabwera kumeneko, anaponyera ndodo zawo pansu, anatembenusa chinthu chomwecho. Tsopano, Mose ankadziwa chinthu chimodzi ichi, kuti Mulungu amene anamutumiza iye anali

wokhoza kumusamalira iye. Tsopano, iye samadziwa choti achite motsatira.

¹¹⁶ Iwe umafika pa malo amene sumadziwa choti uchite, ndipo anthu amati, “Iye sanachiritsidwe. Bwanji, ndi chimenecho chinthucho chikadali pamenepo.” Ngati Mulungu anaziyika izo mu mtima wako, iwe umayima njii. Iwe umangopitirira kuchitira umboni kwa ulemelero wa Mulungu. Kumapitirirabe!

¹¹⁷ Mose anati, “Ine ndikudziwa Mulungu anandituma ine.” Chinachitika ndi chiyani? Serpenti inafufuma katatu kapena kanai, kukula chonchi, mwinamwake nsato kapena chinachake, inawukapo ndipo inazimeza zinazo. Kodi inu munayamba mwaganizapo zomwe zinachitika ndi ndodo zinazo? Iwo anangotola imodzi yokha. Iye anadya zina zonsezo. Izo panalibenso. Ndipo umo ndi momwe Mulungu ati adzachitire limodzi la masiku awa mwa mphamvu Yake. Inde.

¹¹⁸ Mose anali kuchita khama. Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, Iye anatumiza iye kumeneko, ndipo anati, “Chita ichi, Farao.” Ndipo iye anati, “Ngati suteru, ife tichita *chakuti-ndi-chakuti*.” Ndipo iye anaitanira pa Mulungu, ndipo Iye anatumiza ntchentche, utitiri, china chirichonse pa dziko lapansi. Kodi iye anali chiyani? Iye anali atatsimikiza. Mulungu anamuza iye, “Abweretse ana amenewo abwerere ku phiri ili, kuseri kuno.” Iye ankadziwa kuti iye anali nacho chifuniro cha Mulungu, iye ankadziwa kuti anali ndi masomphenya patsogolo pake. Iye ankadziwa kuti miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma masomphenya amenewo sangakhoze kulephera. Kotero iye anapita kumusi kumeneko, akukakamira.

¹¹⁹ Mvetserani, m’bale, ngati inu mungakhoze kubwera mmawa uno ndi masomphenya a chifuniro cha Mulungu, ngati inu mungakhoze kubwera ndi Mawu a Mulungu, ine sindikusamala zomwe zingachitike, “Ine ndidzakhala wokakamira. Ine ndiri. . . mu mtima mwanga, kuyambira pamene ine ndakhala ndiri pano, ine ndiri ndi masomphenya a Mulungu. Ine ndikukakamira. Ine ndikhala—ine ndikhala wokakamira. Ine ndikupita kumusiko, ine ndikupita kukatenga. Chinthu ichi chiyenera chindisiye ine.” Izo zikusiyani inu, m’bale. Musadandaule, izo zikusiyani inu.

¹²⁰ Davide, atayima pamenepo pamaso pa Goliati, bwanji, iye anali wokakamira. Iye anati, “Inu mukutanthauza kundiuza ine kuti mukuima ndi kulola sayansi yamakono ija, asayansi kunjja uko?” Tsopano izo zikumveka mosinjirira, koma ine ndikuyembekeza inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza. Inu mukutanthauza kundiuza ine kuti asayansi amakono akhoza kuima pamenepo ndi kunena kuti masiku a zozizwitsa anapita, pamene Mawu a Mulungu wamoyo akutsutsa izo? Inu mukutanthauza kundiuza ine kuti mukulola sayansi yamakono izinena kuti kulibeko chinthu choterocho ngati machiritso Auzimu, ndipo Baibulo, sikisite-chakuti peresenti

ya utumiki wa Yesu anali Auzimu. . . eya, eyite-sikisi peresenti, ine ndikuganiza, anali machiritso Auzimu? Ndipo lonjezo, ndi malonjezo otsiriza!

¹²¹ Inu mukutanthauza kuti mudiuze ine, abale anga otumikira, kuti inu mwaima ndipo mukulola zotchedwa miyambo ya zipembedzo zimene zikupita mu Mgwirizano wa Mipingo kuno, kapena Bungwe la Mipingo, ndipo mukutanthauza kuti mudiuze ine kuti inu muziima mu bungwe limenelo ndi kuwalola iwo kuti azibanikitsa Mawu a Mulungu mwa inu, ndi kumakuuzani inu kuti masiku a zozizwitsa anapita? Ndinu ndani mulimonse? Kodi inu munayamba mwakhalapo ndi chokuchitikirani chirichonse? Kodi inu munayamba mwabadwa mwatsopano ndi Mzimu wa Mulungu? Inu, ngati inu muli, m'bale, ndithudi inu muwatenga Mawu a Mulungu pa izo. Mulole china chirichonse chikhale bodza. Ndithudi!

¹²² Zindikirani, Davide anali ndi chomuchitikira. Iye anatenga legeni yaing'ono. Iye analibe zochuluka kwambiri. Iyo inali legeni, koma iye anadziwa kuti Mulungu wa Kumwamba anali ndi iye. Ndipo iye anapita kumeneko ndipo anakapha chimbalingondo ndi mkango, ndipo iye ankadziwa chimene icho chikanati chidzachte. Ndipo iye anati, "Kodi inu mukutanthauza kundiuzi ine, ngati Mulungu angakhoze kupereka chimbalingondo chimenecho ndi mkango mmanja mwanga, ndi mochuluka bwanji momwe Iye angakhozere kumuperekerera wodzitukumulayo, Mfilisti wosadulidwa uyo kunja uko?"

¹²³ Dziko lodzitukumula ili la lero, kumati masiku a zozizwitsa anapita, ndipo Russia akuwuka kuno, kuigwetsera mipingo pansu ndi kuichititsa iyo manyazi. Palibe chirichonse mwa iwo chogwirira ntchito. Ndi chifukwa chiyani Castro wamng'ono wakale kumusi uko, munthu wamng'ono wogwidwa ndi ziwanda uja. . . Tsopano, ine—ine ndikumudziwa iye, ndinagwirana naye chanza ndipo ndinakumana naye iye, ndi zina zotero, pamene ine ndinali kumeneko. Ndipo iye anayankhula zabwino kwa ine, ndi chirichonse monga choncho; anati iye ankakhulupirira kuti kukubwera Zakachikwi ndi Khristu, ndi zina zotero, koma iye anagulitsidwa kwa mdierekezi. Koma kodi iye anachita chiyani? Iye anachita zinthu zina zabwino. Iye anachita chinthu chimodzi, iye anakopera ndalama zonsezo ndipo anayambanso ndalama zatsopano. Ndicho chimene chiti chidzachtike kuno limodzi la masiku awa, kumene odzikonda amphamvu awa otcheza mowa, ndi makampani a fodya amene amatenga msonkho wawo ndi kuwuyika iwo pa televizioni kunja kuno. Ine ndikudziwa ine ndikuyankhula pa matepi. Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu, ndicho choonadi, chonchobe. Ndizo ndalama zomwe ziyenera kupita ku boma. Koma iwo amakhoza kuzizungulira izo. Koma inu mukayamba, kulephera

kulipira yanu nthawi imodzi ndikuwona zomwe zimachitika. Iwo adzakuvulani inu chifukwa cha izo.

124 Kutanthauza kuti mundiuze ine kuti gulu la Afilisiti osadulidwa akhoza kuima pano ndi kunyoza ankhondo a Mulungu wamoyo? Ife timayikira kumbuyo chinthu choterocho. Chimene mpingo ukusowa lero ndi kubwerera kwa Mulungu, kubwerera ku Mawu Ake, kubwerera ku Mphamvu, kubwerera ku Pentekoste, osati kwa bungwe la Pentekoste, kubwerera ku chowachitikira cha Pentekoste. Anyamata amenewo achoka mu gudumu pamene iwo akuyankhula za bungwe la Chipentekoste. Pentekoste ndi chokuchitikira, chimabwera kwa Methodisti, Baptisti, Presbateria, kapena aliyense amene akuchifuna Icho. Uko nkulondola. Mulungu samachita ndi fuko, ndi anthu, ndi chipembedzo, Iye amachita ndi munthu payekha. Nthawizonse, ndi Amitundu, kutenga anthu mwa Amitundu chifukwa cha Dzina Lake. Mukuona? Ndi momwe Iye amachitira nawo iwo. Tsopano, mwamsanga, ine ndiyenera ndifulumire.

125 Davide anati, “Iwe ukutanthauza kundiuza ine kuti iwe ulola izo kuti zichitike?” Iye anati, “Legeni yaing’ono iyi!” Iye anawutsatira mkango umenewo. Chiyani? Ndipo anawupha iwo. Ndipo anatsatira chimbalangondocho ndipo anachipha icho. Iye anati, “Ndi mochuluka bwanji momwe Mulungu ati andipatsire ine Mfilisiti uyo kunjira uko amene akunena kuti masiku a zozizwitsa anapita?”

126 Iye anamuseka iye ndipo anati, “Ine ndikutunga iwe pa nsonga ya singano yolukira iyi, nkondo, ndikakupachika iwe mmwamba, ndi kulola mbalame zidye nyama yako.” Iye akanakhoza kuchita zimenezo.

127 Sauli anamuza iye, anati, “Munthu ameneyo ndi . . . bwanji, zala zake ndi mainchesi fortini.” Iye anati, “Bwanji, munthu ameneyo ndi wankhondo kuyambira unyamata wake, ndipo iwe si kanthu koma mnyamata wamng’ono wosawoneka bwino.”

128 “Oh, koma,” iye anati, “Ine ndiri ndi chinachake choti ndikuuzeni inu. Ine ndiri ndi chinachake chimene inu simukuchidziwa.”

129 “Bwanji, sindinu kanthu,” m’bale wake anati, “bwerera kunyumba. Ndiwe wamwano. Ine ndikawauza abambo akakukwapule iwe ukabwerera.”

130 Kodi iye ananena chiyani? Iye anati, “Ine ndinali kuweta. Wantchito wanu, atate anga, ine ndinali kuweta nkhosa zake kunjira uko tsiku lina. Ine ndimadalira mwa Ambuye Mulungu. Ndipo mkango unadzabwera ndipo unadzatenga imodzi ya anaankhosa, ndipo ine ndinawutsatira iwo.” Bwanji? Iye anapatsidwa ulamuliro, wotsogozedwa ndi abambo ake. “Ndipo ine ndinawugwetsera iwo pansu. Ndipo pamene iwo unauka, ine ndinawupha iwo, chifukwa ine ndinasiyidwa ndi ulamuliro.”

¹³¹ Oh, m'bale wotumikira, ife tinapatsidwa ulamuliro. Mkango umabwera ndipo umadzatenga mmodzi wa antchito Ake ndi kumutulutsa iye, ine ndikubwera ndi legeni mmawa uno. Legeni ya pemphero la chikhulupiro lidzapulumutsa odwala, ndipo Mulungu adzamuukitsa iye. Chimene Iye ananena! Ife tikumutsatira iye, kuti timubweretse mwanawankhosa ameneyo ku khola. Ife tikukusowani inu, Mkhristu aliyense, ife tikusowa mmodzi aliyense wa inu. Ife tikukusowani inu, ife tiyenera kuti tikhale ndi inu. Atate atipatseni ife ulamuliro, tiyeni tipite tikawutenge iwo. Tiyeni tisunge ulamuliro.

¹³² Iye anati, “Ndipo ngati Iye angachite zimenezo kwa nkhosa imeneyo, ndi mochuluka bwanji kuyima pano kunyoza ankhondo a Mulungu wamoyo! Ine ndikuchita manyazi ndi m'bale wanga ndi ena onse a iwo,” iye anati, mochuluka kuti ndinene. “Ine ndikuchita manyazi ndi iwo, kufooka kwanu.”

¹³³ Ndipo ine ndikuchita manyazi ndi gulu langa la azitumiki tsikulina pamene ine ndidzawamve iwo akuyima ndi kugwirizana, kutenga mbali ndi osakhulupirira ponena kuti: “Oh, palibepo chinthu choterocho. Palibepo ayi. Inu—inu—inu simumayembekezera zinthu zimenezo kuti zichitike.”

¹³⁴ Petro ananena, pa Tsiku la Pentekoste, “Lonjezo liri kwa inu ndi kwa ana anu, ndi kwa ana a ana anu, kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.” Ngati Iye akuitanabe, Iye akutsanulirabe Mzimu Woyera. Ngati Mzimu Woyera ukukhalabe mwa inu, Iwo uyenera kukhala moyo womwewo umene Iwo unachita kumbuyo uko mwa Khristu Yesu.

¹³⁵ Ngati inu muwona nthambi ikubwera, ndipo iyo nkubala apulo, chabwino, yotsatira siyikhala peyala ndipo yotsatira pulamu. Ngati ndi choncho, iyo yamezanitsidwa. Uko nkulondola. Koma ngati muzu wapachiyambi wa mtengo utulutsa nthambi ina, iyo idzakhala apulo. Chotero, lero, ife tiri ndi mabungwe ambiri ndi zipembedzo zimene zamezanitsidwa. Mitengo imeneyo idzakhala moyo. Inde, bwana.

¹³⁶ Ine ndinawuwona mtengo tsiku lina ndi zipatso naini zosiyanasiyana pa iwo, ndipo iwo unali ndi makangaza, ndipo iwo unali, ine ndikukhulupirira iwo unali mphesa, mandimu ndi zonse pa iwo, koma iwo kwenikweni unali mtengo wa malalanje. Ndipo ine ndinati kwa munthuyo, Bambo Sharrit, mzanga, ine ndinati, “Chabwino, ziri bwanji zimenezo, pokhala mtengo wa lalanje?”

¹³⁷ Iye anati, “Chabwino, iwe umangowutsegula mtengowo ndi kumezanitsa ichi mmenemo.”

¹³⁸ Ine ndinati, “Chabwino, pamene iwo ukubala chipatso, kodi iwo udzabala lalanje?”

Iye anati, “Ayi, iwo udzabala za mtundu wake.”

¹³⁹ Ndi zimenezotu! M'bale, pamene ine ndikuuzani inu, pamene mipingo yamezanitsidwa mwa Khristu, zoterozo, kapena kuyesera, kumaganiza kuti ali, kungozembera mmenemo mwa dzina, kumadzitcha okha mipingo ya Khristu, pamene iwo atero, kodi iwo amabala chiyani? Zipatso zachipembedzo. Koma ngati nthambi imeneyo iti idzabereke konse nthambi ina, iyo idzakhala monga yoyamba imene inalipo. Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu, m'bale, ngati Mzimu Woyera uli weniweni mu Mpingo lero, mtundu wa Mpingo Iwo unali nawo utalemba Bukhu la Machitidwe kumbuyo kwa Iwo, ngati Mpingo wa Mulungu wamoyo, Mpingo wa Yesu Khristu udzakhalenso wamoyo mwa Mzimu Woyera womwewo umene unagwa pa Tsiku la Pentekoste, Iwo udzalemba Bukhu la Machitidwe kumbuyo kwa Iwo. Kulondola. Iwo udzakhala wokakamira, wopirira mpaka chinthu icho chitafika pochitika. O Mulungu, tichitireni ife chifundo. Inde, bwana. Inde, bwana.

¹⁴⁰ Samsoni, Samsoni, iye anali wopirira kwambiri utali wonse pamene iye amakhoza kumverera mangongo seveni awo pomuzungulira iye. Iye ankadziwa kuti ilo linali lonjezo limene Mulungu anamupatsa iye. Ndipo mwamuna aliyense ndi mkazi akanakhoza kukhala wokakamira monga Samsoni anachitira, bola ngati inu mukukhoza kumverera mphamvu ija ya lonjezo pozungulira inu, ya Mulungu. Apa pali Mawu, Mawu ananena chomwecho. Ndipo inu mukhoza kukhala wopirira bola ngati inu mukudziwa kuti inu muli nalo lonjezo limenelo mu mtima mwanu, chikhulupiriro chija chimene chinakuuzani inu, pamene inu mwakhala apa tsopano, chikhulupiriro chimenecho chimati, "Ine ndachiritsidwa. Ine ndachiritsidwa." Mukuona? Iwe umamverera zimenezo, musingoyendabe. M'bale, Mulungu adzawasamalira Afilisiti, inu musadandaule.

¹⁴¹ Kodi inu munayamba mwaganizapo momwe Samson, ali ndi fupa la chibwanu chakale lija la mphongolo. . . Inu mukudziwa kukhuthala kwa chisoti chimenecho? Ena a iwo pafupifupi inchi, kapena inchi ndi theka la mkuwa wolimba. Amakhoza kutenga lupanga lakuthwa konsekonse ndi kumumenya nalo iye pa mutu ndi ilo, ilo osamupweteka iye. Ndipo Samsoni anatenga wovunda wakale, mundikhululukire ine, fupa lakale louma lija la mphongolo, ndipo analinyamula ilo ndikuwakantha sauzande a iwo. Bwanji, kumenya koyambirira pamwamba pa umodzi wa mitu imeneyo, chibwano chimenecho chikanakhala zidutswa milioni. Koma, onani, chozizwitsa chinali mu chibwanu chimodzimidzi monga mwa Samsoni. Iye anamverera, "Ngati ine ndingamverere lonjezo limenelo pamenepo," iye anati, "abweretseni iwo." Ndipo, m'bale, iye anayamba kugwetsera Afilisiti kumanja ndi kumanzere. Bwanji? Iye anali wolimbikira mpaka Mfilisiti wotsiriza anali atagona pansi. Amen! Kodi iye anali ndi chiyani? Si mochuluka kwambiri. Iye anali ndi chibwano kuti azimenyana ndi malupanga ndi nkondo

ndi amuna ophunzitsidwa. Koma iye anali ndi mphamvu ya Mulungu pa iye. Inu mukuzindikira, mphamvu ya Mulungu inabwera pa iye, poyamba.

¹⁴² Oh, m'bale, mumenye mpaka zizindikiro zirizonse zitapita. Aleluya! Mumenye mpaka chirichonse—kukaikira kulikonse kutapita.

¹⁴³ Mukuti, “Chabwino, vuto langa ndi losiyana.” Anatenga fupa la chibwano ilo ndipo analigwetsera ilo kunja uko.

¹⁴⁴ Mmodzi uyu anati, “Koma, inu mukudziwa, ine ndangokhala wosiyana pang’ono, ine ndikukalamba kwambiri.” Kugwetsera icho kunja. Abrahamu anali wa handiredi. Pitirirani.

¹⁴⁵ “Chabwino, koma vuto langa ndi loipa kwambiri.” Yona anali mmimba mwa chinsomba, manja atamangidwa kumbuyo kwake, atagona pansi mu masanzi a chinsomba. Kulikonse kumene iye amayang’ana kunali mimba ya chinsomba. Iye anali ndi zisonyezo zambiri, koma iye anatembenuka ndipo anati, “Kamodzinso ine ndiyang’ana ku kachisi Wanu woyera, Ambuye.” Simungakhoze kumubisa Iye. Ndi zimenezotu, kulimbikira! Khama, kukhala molondola ndi Mawu a Mulungu. Nchifukwa chiyani Yona anakhala monga choncho? Chifukwa iye anadziwa kuti pamene Solomoni ankampereka kachisi, iye anapemphera ndipo anati, “Ambuye, ngati anthu Anu adzakhale mu vuto kulikonseko ndipo nkuyang’ana ku malo oyera awa, ndiye mudzamve kuchokera Kumwamba, yankhani pemphero lawo.” Ndipo iye ankadziwa chinthu chimodzi ichi, kuti Mulungu akanadzamva pemphero limenelo.

¹⁴⁶ Ndipo ngati Yona, pansi pa zochitika zimenezo, anakhoza kukhala ndi chikhulupiriro chochuluka chotero mwa Mulungu, nanga bwanji inuyo? Palibe mmodzi wa inu pano ali woyipa kwambiri pansi pa zochitika zimenezo. Tsopano ndi mochulukira bwanji! Yang’anani ku kachisi kumene munthu potsiriza anabwerera mmbuyo, Solomoni, yemwe anapemphera pemphero, koma kunali kudzipereka kwa Mulungu pamene Mzimu Woyera unachitira umboni izo mwa Lawi la Moto limene linadzalowa ndi kupita kuseri? Lawi la Moto lomwelo limene inu muli ndi chithunzi chake lero, likuyenda pakati pathu, likuchita zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa. Chavuta ndi chiyani? Mvetserani mwakachetechete. Mvetserani. Ife tingakhoze bwanji, pamene sitikuyang’ana ku kachisi wa padziko lapansi, kapena bungwe lina kapena chipembedzo china, koma ku dzanja lamanja la Mulungu, kumene Yesu akukhala kumeneko ndi zovala Zake Zomwe zamagazi, ameni, Magazi Ake Omwe pamaso pa Atate, kuti azipembedzera pa kuvomereza kwanu! Ameni. Ahebri 3, ananena kuti Iye—Iye ndi Wansembe Wamkulu, wamoyo nthawizonse kuti azipanga chitetezero, oh, mai, pamaso pa Atate mmawa uno. Wansembe Wamkulu! Ngati Yona akanayang’ana panja, nkukana kuwona

mimba ya chinsomba, ndi mochuluka bwanji ife tingalephere kuwona kuwawa kwakung'ono ndi kuwawa pang'ono, kapena pang'ono chirichonse chomwe ife tiri nacho! “Ine ndikuyang'ana ku lonjezo Lanu loyera, Ambuye.” Inu simungakhoze kumubisira woyera pemphero lake, ndizo zonse zomwe ziripo kwa izo, zedi. Oh, iye anali. . .

¹⁴⁷ Ine ndiyenera kuti ndifulumire, abwenzi anga, ine ndikhala nditachedwa kwambiri kachiwiri. Tiyeni angapo ena, mutu waung'ono apa.

¹⁴⁸ Yohane, iye anali wotsimikiza kwambiri, chifukwa Mulungu anamuuza iye. Inu mukudziwa, tsopano abambo ake anali wansembe, inu mukudziwa, koma, zachirendo, iye sanapite uko kukakhala wansembe, iye anapita ku chipululu. Iye sanafune kuti asokonezedwe mu lingaliro la munthu. Iye anapita ku chipululu kuti akafufuze, pa usinkhu wa naini. Bambo ake ndi amake pokhala okalamba, ankadziwa kuti iwo sakanati adzamuwone mwana wawo mneneri akubwera konse mu mphamvu mu tsiku limenelo.

¹⁴⁹ Ndipo, kumbukirani, Mzimu womwewo watilonjeza ife mu tsiku lotsiriza lino, Eliya.

¹⁵⁰ Kumbukirani, Yesu sanalozere konse izo pamene Iye anati. . .Iye anayankhula za Yohane M'batizi. Ngati mungazindikire, “Ine ndikutumiza mtumiki Wanga patsogolo pa nkhope Yanga,” Mateyu 3. Chifukwa, inu simutero, inu mumakhala ndi kutsutsana mu Lemba.

¹⁵¹ Iye anati, “Lisanadze tsiku lino, la tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye kuti adzawotche dziko lapansi ndi moto.” Dziko lapansi silinawotchedwe ndi moto mmbuyo mmasiku amenewo. Dziko lidzawotchedwa ndi moto kutachitika kudza *uku*. Iye akanadzatumiza Eliya kuti adzawongole zinhuzo ndi kuwabweretsa anthu kubwerera ku chiyanjantso. Ndipo chimene Eliya uyu, mmodzi woyamba kubwera, akanadzabwezeretsa, akanadzabweretsa chikhulupiriro cha atate kwa ana, koma mmodzi mmasiku otsiriza akanadzabwezeretsa iwo kubwerera ku Chikhulupiriro cha atate. Mukuona? Mwaona, kubwerera kwa makolo apachiyambi achipentekoste, Uthenga wolondola, chiyambi. Eliya! “Mulungu, mtumizeni iye,” ndiro pemphero langa. “Mtumizeni iye, O Ambuye, mtumizeni iye mwamsanga.” Ife timuzipempherera iye, kuti iye awonekere powonekera. Ndipo Mulungu nthawizonse amakhala ndi womuimirira Wake penapake mdziko lapansi. Iye sanayambe wakhalapo wopanda mboni kwinakwake, nthawizonse amakhala ndi mboni itaima moon. Ndipo ine ndikukhulupirira iye ali. . .Ine ndikukhulupirira kuti ife tikukuchitira mthunzi Kudza kwa Ambuye pakali pano. Nthawi yakuti mphamvu ya Mulungu iwukenso mmawonekedwe a mneneri wa Eliya, ndi kutumiza

pansi kuno ndi kudzawawongola anthu, ndi kuwabweretsa iwo, gulu laling'ono limenelo. Monga izo zinali mmasiku a Nowa, monga izo zinali mmasiku a Loti, chomwechonso izo zidzakhala, basi apang'ono okha, Mpingo udzakhala.

¹⁵² Chabwino, ife tikupeza kuti Yohane sanapiteko kuti akatenge maphunziro ake achipembedzo, koma iye anapita ku chipululu kuti akapeze chomuchitikira. Pamene iye anabwererako, iye ankayankhula chipululu. “M’badwo wa njoka,” njoka zimene iye anakazipeza mchipululu. “Nkhwangwa yaikidwa ku muzu wa mtengo.” Maulaliki ake anakahazikitsidwa pa zonga zimenezo. Koma, penyani, iwo anabwera pamenepo, iye anati, “Pali Mmodzi waima pakati panu tsopano yemwe inu simukumudziwa.” Iye ankadziwa zomwe iye anali kuzikamba.

“Kodi ndinu Mesiya?”

Iye anati, “Ayi.”

¹⁵³ “Kodi ndinu Mneneri ameneyo, yemwe Mneneri-Mesiya amayenera kumudzutsa?”

“Ine sindine ayi,” iye anati, “koma Iye waima pakati panu tsopano.”

¹⁵⁴ Mwinamwake Kayafa, wansembe wamkulu, anakhala ali kumeneko. Chimene, ine ndikuganiza iye sanali, iye anali wolemekezeka kwambiri kuti abwere ku malo ngati amenewo. Koma iye, winawake wa ansembe mwina ananena kuti, “Bwana, apa pali M’bale Jones. Iye ndi munthu wabwino. M’bale *Wakuti-ndi-wakuti* kuno, M’bale John Doe, iye, ine—ine ndikukhulupirira iye, Ambuye akumupanga iye kukhala Mesiya.”

¹⁵⁵ Yohane anati, “Ine ndidzamudziwa Iye. Padzakhala chizindikiro chiti chidzamutsatire Iye.” Iye ankadziwa zimenezo. Odala ali auzimu amene akumvetsa. Odala ali iwo amene ali nawo maso ndipo akhoza kuwona, makutu amene akhoza kumva. Anati, “Ine ndidzamudziwa Iye. Mulungu adzamuzindikiritsa, adzamuzindikiritsa Iye.” Mulungu amawatsimikizira antchito Ake. Inde, bwana. Ndipo patapita kanthawi Iye anabwera, iye anayang’ana kuntunda uko ndipo iye anawona, iye anati, “Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu amene akuchotsa tchimo la dziko lapansi.” Iye anali wokakamira kuti panalibe Ph.D., LL., ma L awiri, chirichonse chimene icho chinali, chikanadzabweramo, wansembe wina, munthu wina wokonedwa wa nthawiyo ndi mtundu wina wa chipwirikiti. Iye anali... Munthu ameneyo anabwera kumeneko ndipo iye anadziwa Yemwe Iye anali chifukwa panali chizindikiro chikumutsatira Iye. Iye ankadziwa Yemwe Iye anali.

¹⁵⁶ “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Mpingo wa Mulungu ukuwukitsidwa ndi kuikidwa mu mphamvu. Inde. Tsopano, tizitsika mpaka nditatsiriza

mutu tsopano. Yohane, akulimbikira. Ndipo iye anali ndi khama chifukwa iye ankadziwa kuti iye akanadzamudziwa Mesiya ameneyo, chifukwa Mesiya anali woti adzakhale ndi chizindikiro. Ndipo ife tikuwona zizindikiro lero, zizindikiro za Mesiya wakudza, zikukanikizira mkati. Tsopano mveterani mwakachetechete tsopano.

¹⁵⁷ Pamene mkazi wa Chigriki uyu, pamene iye anamva za Yesu, “Chikhulupiriro chimadza pakumva.” Tsopano, iye anali wa Chigriki, wachikunja, kotero iye anamva ndipo iye anabwera. Inu mukudziwa chiyani? Chikhulupiriro chimapeza gwero limene ena samaliwona. Chikhulupiriro chimapeza gwero limene ena sangakhoze kuliwona.

¹⁵⁸ Inu mukuti, “Oh, nchiyani chiri mmwamba apoo? Nchiyani chiri pansi apa? Nchiyani chiri kumeneko? Ndi chiyani chaching’ono icho. . . Oh, ndi mishoni yaing’ono. Ndi *chakuti-ndi-chakuti*. Ngati Mulungu akanati achite chirichonse, Iye akanati abwere ku ulumuliro wolowezana wa Roma Katolika, Iye akanabwera kwa arikbishopu wa mpingo wa Methodisti, Iye akanabwera kwa—a—makolo achi Anglikani, kapena ena a iwo. Iye akanadzabwera. . .” Eya, ndicho chimene iwo ankaganiza pachiyambi. Koma kodi Iye anabadwira kuti? Mu khola. Kodi Iye anawatenga kuti ophunzira Ake? Kuchokera ku mtsinje, asodzi, digirii yotsika, opanda maphunziro. Mwaona, Mulungu amachita zimene Iye akufuna kuchita, koma inu mukumudziwa Iye.

¹⁵⁹ Zinali zosiyana bwanji kuno, za Moabu kumtunda kuno, pamene Israeli anali kudutsa? Moabu anapereka ng’ombe seveni, ndendende basi zomwe Israeli anali nazo. Moabu anapereka nsembe seveni, nkhosa zamphongo, ndendende basi zomwe Israeli. Mwachikhazikitso, iwo anali chimodzimidzi ofanana. Ndipo iwo anali kwenikweni abale, Moabu anachokera kwa mwana wamkazi wa Loti. Ndipo apa panali Balaki pamwamba apo akupereka nsembe yomweyo, anachita mwachikhazikitso basi monga iye akanathera. Koma nchiyani chinapanga kusiyanako? Mmodzi wa iwo anali ndi Thanthwe lokanthidwa, Lawi la Moto, liwu la Mfumu mu msasa, gulu la azipembedzo zosiyanasiyana. Iwo analibe nyumba, analibe malo oti aziwatchesa awo omwe. Iwo anali akulowerera, amwendamnjira ndi alendo, oyendayenda, akudzinenera kuti iwo anali amwendamnjira ndi alendo. Iwo anali akufunafuna mzinda.

¹⁶⁰ Umo ndi momwe izo ziriri lero. Osati kulumikizana kwina ndi bungwe linalake lalikulu. Zomwe ziri zabwino, koma, izo, ine sindikusamala kaya ndinu wa bungwe lochuluka bwanji, kaya ndi wa kulikonse kumene inu mukufuna. Koma, chinthu choyamba, ikani dzina lanu pa Bukhu Pamenepo, mulole Mulungu alembe izo mu Magazi a Yesu Khristu, landirani Mzimu Woyera, ndi chikhulupiriro kuti mukhulupirire Mawu aliwonse

amene Iye anawalemba, kuti Iwo ndi owona. Ndi zimenezotu. Eya.

¹⁶¹ Tsopano, mkazi uyu anali Mgriki, kuyamba ndi kuyamba, koma chikhulupiriro chimapeza gwero limene ena sakudziwa kanthu za ilo.

¹⁶² Tsopano, kumbukirani, Ake—Mawu Ake ndi Lupanga. Baibulo linanena chomwecho. Ilo ndi Lupanga. Ahebri, wa 4, 4:12, ngati inu mukufuna kulemba izo. Ahebri 4:12, anati Iye ali, “Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse.” Ndiroleni ine ndiyime apa miniti yokha. Mvetserani. “Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, kupyozza ngakhale mogawanika mwa fupa, ndi zina zotero, mmafupa, ndi Wozindikira maganizo a mu mtima.” Ndi kulondola uko? Izo—izo, tiyeni tiyime miniti yokha, taganizani tsopano, “Wozindikira wa mmalingaliro a mu mtima.” Kodi Lembamba limanama? Ilo silingakhoze. Ngati Ilo lidzitsutsa Lokha, ilo si loyenera pepala limene lalembedwapolo, ilo ndi wonyenga. Ngati malonjezo a Mulungu adzitsutsa okha, chiyani—inu mukhulupirira chiyani?

¹⁶³ Monga mnyamata wa Chimwenye amene anabwera posachedwapa kwa Dokotala Morris Reidhead ndi iwo, purezidenti wa Sudan Mission, ndipo anama pamenepo ndipo iye anati, “Kumbukirani,” anati, “ife tikudziwa Yesu ali moyo,” iye anati, Dokotala Reidhead anati—anati, “chifukwa Iye akukhala mu mtima mwanga. Uko nkulondola.”

¹⁶⁴ Iye anati, “Inde, ndipo Muhamadi amakhala mu mtima mwanga, nayenso.” Anati, “Ife tikhoza kubala kuwerenga maganizo kochulukira basi mu Chimuhamadi monga Chikhristu chingachitire.” Koma anati, “Chabwino, ine ndikufuna ndiwone zipsyera zimenezo za chizindikiro, zizindikiro za Marko 16 zikukwaniritsidwa.”

¹⁶⁵ Iye anati, “Oh, izo,” anati, “ndiwe—ndiwe basi...” Anati, “Inu mukuona, bwana, kuyambira pa mutu wa 9... ndime ya 9 ya mutu wa 16 wa Marko, ndi wosadzozedwa monga ena onsewo. Izo zinangoikidwa mmenemo ndi Vatican.”

¹⁶⁶ Iye anati, “Ndiye mwinamwake ena onse a Iwo ndi osadzozedwa. Koteri kodi inu mukuwerenga Bukhu la mtundu wanji?” Anati, “Koran yonse ndi yodzozedwa.” Ndi chamanyazi bwanji! Ndi chamanyazi bwanji kwa mpingo wa Chikhristu! Amenewo mwina ndi Mawu a Mulungu kapena Iwo si Mawu a Mulungu. Ndipo ngati inu mutangoyika chikhulupiriro mwa Iwo, inu mudzawawona Iwo akugwira ntchito. Inu muwakhulupirire Iwo, muwalandire Iwo. Inde, bwana. Ife timawakhulupirira Iwo.

¹⁶⁷ Chiyani? Wozindikira maganizo a mu mtima. Tsopano taonani, “Pachiyambi panali Mawu, Mawu anali ndi Mulungu,” Yohane Woyera 1, “ndipo Mawu anasandulika thupi, Khristu.”

Ndipo pamene Iye anabwera kuno, Iye anayang'ana pansu pa anthu. Mkazi wamng'ono anakhudza chovala Chake, Iye anapotoloka mozungulira, anati, "Ndani wandikhudza Ine?" Petro anamudzudzula Iye. Iye anayang'ana pozungulira ndipo anati, "Ndani wandikhudza Ine?"

Anati, "Aliyense akukukhudzani Inu."

¹⁶⁸ Anayang'ana pozungulira ndipo anati, "Koma Ine ndazindikira kuti Ine ndafooka." Anayang'ana pamenepo. "Vuto lako la magazzi lasiya." Chiyani? Mawu a Mulungu akuzindikira maganizo.

¹⁶⁹ Afarisi amenewo amanena, mu mtima mwawo, iwo anati, "Iye ndi Bezebule. Mwaona, Iye, ndicho chimene Iye ali. Ndizo ndendende basi."

¹⁷⁰ Iye anapotoloka pamenepo ndipo anati, "Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha zimenezo." Yesu akuyang'ana pa omvetsera ndi kuzindikira zoganiza zawo. Chinali chiyani chimenecho? Mawu, Mawu osandulika thupi, ozindikira malingaliro ndi zamkati mwa mtima. Ndicho chimene Mawu a Mulungu ali tsopano. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mukuona?

¹⁷¹ Iwe uyenera kutengera Mawu amoyo mwa iwe kuti ukhale ndi Mulungu wamoyo mwa iwe, chifukwa Mawu apa ndi Mulungu pamene Iwo asandulika thupi mwa iwe, opangidwa Mzimu, Moyo mwa iwe. Pamene Iwo ulowa mu thupi lako ndi chikhulupiriro chako, ndi kudzakhala Moyo, ndiye ndiwe chitsanzo chamoyo. Ndinu kalata ya Mulungu, yowerengedwa ndi anthu onse. Inu simukhale nawo Iwo monga Khristu, osati chidzalo, chifukwa Iwo unagawidwa pa Tsiku la Pentekoste.

¹⁷² Tsopano, anthu inu amene mumakhulupirira kuti mukuyenera kuyankhula mmalirime kuti mukhale ndi Mzimu Woyera, Ine ndikufuna kuti inu mumvetsere kwa izi miniti yokha. Pamene Mzimu Woyera unatsika, pa Tsiku la Pentekoste, Iwo unali malirime a moto. Limenelo linali Lawi la Moto limene linkawatsogolera ana a Israeli, linali litadzilekanitsa Lokha ndipo linali pa mmodzi aliyense wa iwo, Mulungu mu Mpingo Wake. Inde, bwana, Mzimu Woyera. Uko nkulondola. Apo ndi pamene iwo analandira Mzimu Woyera, pamene iwo anayankhula mmalirime. Ilo silinali lirime losadziwika, iwo anali kuyankhula kwa anthu kunja uko omwe ankawamva iwo. Uthenga un kayenera kutuluka pa nthawi imeneyo. Iwo anapita kunja mwa omvetsera, ndipo kenako mpaka kunja mmabwalo ndipo anayamba kuyankhula ndi zinenero, osati zosadziwika. Inu mukapeza ngolo patsogolo pa kavalo pamene muganiza kuti inu mumayenera kuyankhula ndi malirime osadziwika. Ayi, bwana, iwo ankayankhula ndi zinenero. Anthu ankamumvetsa munthu aliyense, "Ife tikumumva bwanji munthu aliyense mu lirime lathu lomwe mmene ife tinabadwira?" Kuchita kwa

Mulungu kutumiza Mzimu Woyera. Zochuluka kwambiri kwa izo.

173 Mawu awa a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ngakhale Wozindikira malingaliro a mu mtima. Ndipo chiyani? Iwo akhoza kungogwiridwa ndi dzanja limodzi. Lupanga ndi laulamuliro. Ilo—ilo silimakhala ndi kanthu mwa ilo kupatula ilo litagwiridwa ndi dzanja. Ndipo pamene dzanja la chikhulupiriro lingakhoze kuwatenga Mawu a Mulungu, ilo lidzachita chinthu chomwecho chimene Yesu ankachita. “Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita.”

174 Mwinamwake inu mukhoza kudula pang’ono chabe, mwinamwake inu muli ndi dzanja lofooka la chikhulupiriro, inu mukhoza kudula mokwanira kuti munene kuti, “Chabwino, ine ndikukhoza kuwona kuwala kokwanira kuti ndiwone kuti ine ndinapulumsidwa.” Koma nanga bwanji malonjezo ena? Ngati muli ndi dzanja lamphamvu la chikhulupiriro, mutole Mawu athunthu a Mulungu ndipo mudule kudutsa mdima uliwonse, ameni, mpaka Kuwala kwa Mulungu kutawalira mkati, ndi kuyang’anizana nkhope kwa nkhope ndi Mulungu, mutaima pa Mawu Ake. Ameni.

175 Iye anali nazo zotchinga zambiri, mkazi wamng’ono wosauka uyu anatero. Iye anali ndi zotchinga zambiri, koma chikhulupiriro chake chinalibe chirichonse. Ayi, ayi. Iye anali atamva. Chikhulupiriro chinali chitagwira. Iye anamva ndipo chikhulupiriro chake chinali chitagwira. Tsopano, iwo mwina anali atanena ichi kwa iye, “Iwe ukudziwa ndiwe Mgriki. Iwe ukudziwa kuti sudzapeza kalikonse, chifukwa kuli tsankho, iwe ukuona. Iwe sudzapeza kalikonse kuno.” Koma kodi iye anapereka tcheru kwa zimenezo? Ayi, bwana. Iye anali ndi chikhulupiriro, ndipo chikhulupiriro chimenecho chinali chonse chimene iye ankachisowa, chifukwa iye ankadziwa kuti awo anali Mawu a Mulungu ataima pamenepo. Iye anali ndi chikhulupiriro. Ena a iwo mwinamwake akananena kwa iye monga chonchi, “Koma dikirani miniti!” Fuko lake lomwe, mpingo wake womwe mwina ukanakhoza kunena, “Tsopano dikirani miniti, masiku a zozizwitsa anapita. Musati mupite kumusi uko. Masiku a zozizwitsa anapita.” Koma chinachake chimzake chokhudza chikhulupiriro, icho chiri ndi gwero limene silimapereka chidwi chirichonse kwa izo, ndipo basi silimazindikira izo. Iye anali atawatenga kale Mawu amenewo. Iye ndi Mawu. Iye anali ndi chikhulupiriro chowagwira Iwo. Iye anayendabe. Iwo mwina anamuseka iye, anati, “Chabwino, wina aliyense azikuseka iwe, chifukwa mwana wako wamkazi adzakhala akudwala basi chaka chamawa monga akuchitira chaka chino. Iye adzakhalabe ndi mdierekezi ameneyo, iye adzakhala akudwalabe basi.” Koma iye sanapereka chidwi chirichonse kwa zimenezo. Chikhulupiriro chinali chitagwira,

mwaona. “Inu mudzachotsedwa mu mpingo wanu ngati inu muti mudzapite konse uko mu chimodzi cha zimenezo. Kumbukira, iwo akuchotsa iwe. Iwo akuchotsa iwe.” Zimenezo sizinatanthauze kalikonse kwa iye. Chikhulupiriro chinapitirira pamwamba pa zimenezo. Iye anatsimikiza kuti akafike kwa Yesu. Ndi zimenezotu.

¹⁷⁶ Tsopano, kuti tisunge nthawi, pamene ife tikanakhoza kutenga nkhani ya mmodzi aliyense wa iwo ndi kukhala nayo iyo, koma tsopano kuti tisunge nthawi. Pamene iye anafika kwa Yesu, iye akadali ndi chokhumudwitsa, iyemwini, koma osati chikhulupiriro chake. Pamene iye anakafika kwa Yesu, Iye anati, “Ine sindinatumizidwe kwa mtundu wanu.” Kukanidwa kosapsyatira bwanji! “Ine sindinatumizidwe kwa anthu inu.” Tangoganizani, Mmodzi yemwe iye ankaganiza kuti anali naye chikhulupiriro chochuluka, ndipo Iye anamukana iye. “Ine sindinatumizidwe kwa inu anthu, ine ndinangotumizidwa kwa Israeli yekha. Ndinu Wamitundu, Ine sindinatumizidwe nkomwe kwa inu. Ndipo, pambali pake, sindinu kanthu koma agalu.” Psyii! Zimenezo sizinasokoneze chikhulupiriro chimenecho, anangopitirira kumayendabe. Inde, anati, “Ine ndangotumizidwa kwa nkhusa zotayika za Israeli.”

¹⁷⁷ Tsopano, ngati zimenezo akanakhala mmodzi wa ife, oh, mai, izo zikanakhala zimenezo. “Chipembedzo chanu, palibe kanthu kwa icho.”

“Oooh, iye anayankhula za chipembedzo changa, ine sindidzamumvetseranso Iye kachiwiri!” Uh-huh, ndi zimenezotu. Pitirirani nazo, mwaona, inu simudzapeza kalikonse. Mungokhala ndi Mawu amenewo. Kumene kuli Mawu amenewo, inu mupite kumene ndi Iwo. Chikhulupiriro chinali chitazikika!

¹⁷⁸ Ena a iwo mwinamwake anati, “Chabwino, tsopano, ine ndikukuza iwe chiyani, iwo azikuseka iwe. Iwo akuchotsa iwe mu mpingo wako.”

“Asiyeni iwo anditulutsemo ine. Mwaona, izo ziri bwino.”

¹⁷⁹ Yesu anati, “Ine sindinatumizidwe kwa mtundu wanu, ine sindinabwere konse kwa anthu inu nkomwe. Ndipo sindinu kanthu koma agalu, sikuli koyenera kwa Ine kuti nditenge mkate wa ana ndi kuwuponyera iwo kwa inu agalu.” Psyii!

¹⁸⁰ Nanga bwanji ngati izo zikanakhala mmodzi wa inu Amethodisti, mmodzi wa inu Abaptisti, Apresbateria, mmodzi wa inu Achipentekoste? Oh, mai! Inu mukanati, “Bwanji, wonyengezera uja! Ine ndimuuza Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti* ndi *Wakuti-ndi-wakuti* iye—iye anali kulondola.” Mwaona, inu mulibe chikhulupiriro.

¹⁸¹ Iye ankadziwa kuti apo panali thandizo. Iye anali atamva. Chikhulupiriro chimadza pakumva. Kumva chiyani? Mawu. Iye anadziwa kuti panali chinachake chenicheni pamenepo. Inde.

Komabe iye anagwiritsitsabe. Ziribe kanthu ngati iye. . .Iye anati, “Tsopano, kumbukirani, Ine sindinatumizidwe kwa inu. Atate sananditumize konse Ine kwa inu Amitundu, inu gulu la agalu. Kodi inu mukuganiza Ine ndingatengere mkate wa ana ndi kuwuponyera iwo kwa inu gulu la agalu osayenera? Ine sindinatumizidwe kwa inu.” Komabe chikhulupiriro chake chinagwiritsitsabe.

¹⁸² M’bale, iye sanali chomera chokhala mnyumba, kuchita kupembedzedwa, kumasatitsidwa pamenepo monga mbewu zina za lero, “Oh, mai, chabwino, ine sindidzapitako konse kachiwiri, ndizo zonse zomwe ziripo kwa zimenezo.” Oh, mai. Nzosadabwitsa kuti iwe sungakhoze kuligwira Lupanga limenelo la chikhulupiriro, nzosadabwitsa kuti iwe umanyengerera pa Mawu. Inu mumapita kwinakwake kumene inu mungakhoze kukamva mtundu winawake wa chinachake chachikazi chaching’ono chitayikidwa pamodzi. Inu chomera chaching’ono cha mkanyumba, inu. Kachirombo kakang’ono koyamba kukukanthani inu, iko kamakuphani inu, inu mumayenera kupoperedwa nthawi zonse. “Oh, musamakhlupirire zinthu zimenezo, masiku a zozizwitsa anapita,” ndi kupopera kwa mdierekezi. Mlendo!

¹⁸³ Iye sanali. M’bale, iye anali wolimba. Iye anali ndi chinachake kwenikweni. Iye anagwiritsitsabe. Kodi iye anachita chiyani? Iye anavomereza kuti Iye anali kulondola. Iye nthawizonse. . .Ndipo chikhulupiriro choona chenicheni, chimamvetsera, kaya icho chikudula bungwe lanu kapena ayi, icho chidzavomereza Choonadi. Inde, bwana, Choonadi, chikhulupiriro. Ngati iwe uli ndi chikhulupiriro, ndipo ndi Mawu a Mulungu ndi lonjezo la Mulungu, ziribe kanthu zomwe enawo akunena, iwe umakhlupirira Iwo, iwe umawavomereza Iwo. Iye anati, “Icho ndi Choonadi, Ambuye. Ndine Mgriki, ndine wosayenera. Ine—ndine galu, ine sindiri. . .Ine—ndine wosayenera chirichonse, koma ine ndikungofuna zinyenyetswazi basi.”

¹⁸⁴ Ndine wosaka zinyenyetswa, inemwini, sichoncho inu? Ine ndikungofuna zinyenyetswa, Ambuye. Ine sindingakhoze kukhala nawo mpingo monga iwo anachitira pa Tsiku la Pentekoste. Ngati ine sindingakhoze, Ambuye, ndiroleni ine ndingokhala ndi zinyenyetswa zimene zikugwa. Petro ananena, pa Tsiku la Pentekoste, “Ichi ndi Chija.” Ndipo ine nthawizonse ndimanena kuti, ngati ichi sichiri Icho, ine ndingochisunga ichi mpaka Icho chidzabwere, inu mukuona. Eya. Eya. Ine ndingochisunga ichi mpaka Icho chidzawonekere. Mwaona? Awa ndi Mawu. Pamene winawake. . .ine sindi. . . Ine—ine—ine mwinamwake sindingakhale ndi chikhulupiriro chokwanira kuti ndipite monga Enoki, ndikupanga kuyenda kwa masana ndikuyenda kumapita kwathu ndi Mulungu, koma ine ndikuuzani inu chinthu chimodzi, ine sindidzayima konse

mu njira ya aliyense amene ali ndi chikhulupiro chochuluka chotero. Inde, bwana. Ngati iye ali nacho icho, Mulungu alemekezeke, ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha icho. Mulole Mawu amenewo azikike mmenemo. Ine ndikuyembekeza Iwo azikika mwa ine monga chomwecho kuti pamene imfa idzafika, ine ndidzawone msewu utatseguka kutsidyako, nkumadzangopitirira kumayendabe. Uko nkulondola. Inde, bwana. Oh, chotero ine ndikungofuna zinyenyetswazi.

¹⁸⁵ Koma, iwe uyesere kuwauza ena a anthu amakono awa lero, inu mungotenga zinyenyetswazo. “Oh, ayi!” Ngati iwo sangakhale ndi malo oyambirira, iwo samafuna kalikonse nkomwe. “Inu mwina mubwera kwa ine...” Monga Namani anachitira ndi khate lake, “Inu mubwere kuno ndipo mudzamenyetse manja anu pa ine ndipo inu mudzandi wuze ine zinthu zonse zosiyanasiyana izi, ndi zina zotero, kapena ine basi sindikhulupirira Iwo mpang’ono pomwe. Ndiyo njira yake. Bwanji, ine basi sindibwereranso.” Ndi chifukwa chake inu simumapeza kalikonse. Mukuona?

¹⁸⁶ Inu muyenera kukhala ololera kutenga zinyenyetswa. Kodi inu mukumva zimenezo? Tangani zinyenyetswazi, m’bale wanga, mutenge zinyenyetswazi, mlongo wanga, mosalabadira zomwe Iye akukupatsani inu, ingolandirani Iwo. Munene kuti, “Mulungu,” mumuthokoze Iye, “Ine ndangotsala ndi chikhulupiro chapang’ono chabe, koma ine ndithudi ndigwiritsitsa kwa icho ndi kukuthokozani Inu chifukwa cha Iwo. Ine ndikukhulupirira kuti ine ndikhoza kuchiritsidwa. Inde, Bwana. Ine ndikukhulupirira Mawu a Mulungu ndi olondola, ndipo ine ndigwiritsitsabe kwa Awa. Ndipo ine ndikhala bwino.” Inu muwone chimene chingachitike. Mungotenga zinyenyetswazo, kanyenyetswa kakang’ono komalizira. Ndithudi.

¹⁸⁷ Kumbukirani, iye anali asanawonapo chozizwitsa. Iye anali wachikunja. Iye anali asanamuwonapo Iye akuchita zozizwitsa zirizonse. Iye anali asanadziwe konse kuti Iye anali Mulungu. Iye anali asanadziwe konse, kokha basi pakumva. Koma pamene iye anakafika kumeneko, mwinamwake, ndipo anawona chinachake chimene Iye anali atachita, chimenecho chinali chosiyana. Mwaona, iwo anawamva iwo akuti, “Chabwino, inu mukudziwa kuti mu Baibulo lawo Ilo limati Ambuye adzautsa Mneneri, ndipo Iye adzachita zozizwitsa ndi kudziwa zinsinsi za mu mtima, ndi kuwauza anthu chinthu ichi, ndipo zinthu zazikulu zidzachitika.” “Ndi choncho zimenezo?” Iye anali asanaziwonapo izo zikuchitidwa, koma iye anakhulupirira izo mulimonse. Ndi zimenezotu. Ndi zimenezotu.

¹⁸⁸ Ine ndikuganiza za Rahabu hule, iye anali asanamuwonapo Israeli, koma iye anamva, ndipo iye anawabisa azondi. Anawukana wake womwe—mpingo wake womwe, anthu ake omwe ndi china chirichonse, ndipo anawabisa azondi,

chifukwa iye anamva. Iye sanati konse, “Dikirani mpaka ine nditamumva Yoswa akulalikira nthawi ina. Ndiroleni ine nditenge lingaliro langa nditatha kumumva iye akulalikira. Mundirole ine ndimuwone Mulungu akutsegula Nyanja Yofiira kwina kwake, kapena mundirole ine ndimuwone Iye akuchita chinachake chonga izo. Ndiye mwinamwake ine ndikubisani inu nonse ngati ine nditawone chinachake chonga icho.” Iye sanayembekezere zimenezo. Iye anati, “Ine ndikukhulupirira. Iye tamva. Iye tamva.”

¹⁸⁹ O Mulungu, ine ndinamva, ine ndikudziwa kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ine ndikudziwa kuti Iye ndi Mulungu akuwonetseredwa mu thupi. Ine ndikudziwa kuti Iye ali moyo lero mu Mpingo Wake. Ine ndikudziwa kuti Iye ali pano tsopano. Ine ndikudziwa. Ine ndikudziwa kuti icho sichinali chithunzi changa chimene Iye anachijambula, ine ndikudziwa Icho chinali Chake. Ine ndikudziwa kuti ndiro Lawi la Moto lomwelo ndi ife lero, chifukwa Ilo likuchita ntchito zomwezo, zizindikiro zomwezo, zodabwitsa zomwezo, zinthu zomwezo zimene Iye ankachita. Ndi Lawi la Moto lomwelo limene linatsogolera Israeli. Pamene, Yesu, aliyense amene amadziwa Baibulo lanu amadziwa kuti Iye anali Mngelo wa Pangano, Mngelo amene ankapita patsogolo pawo mu chipululu. Kodi Khristu . . . Mose anachiyesa chitonzo cha Khristu chuma chachikulu kuposa icho cha Igupto? Anatsatira Lawi la Moto kupita mu chipululu.

¹⁹⁰ Yesu, pamene Iye anali . . . Lawi la Moto lija linawonetseredwa, Iye anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu ndipo Ine ndikupita kwa Mulungu.” Iye anabwerera kwa Atate.

¹⁹¹ Ndiye itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro, ndi kukwera mmwamba, Paulo, Sauli amene anali nthawi imeneyo ku Tariso, ali pa msewu waku Damasiko, anagwetsedwa pansu ndi Lawi la Moto lomwe lija, limene palibe wina aliyense analiwona Ilo. Onse a iwo ataima pozungulira, iwo sanaliwone Ilo, koma Sauli analiwona Ilo. Ndipo Liwu linati, “Saulo, Saulo, chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

Anati, “Ndinu Ndani, Ambuye?”

Iye anati, “Ine ndine Yesu.” Mukuona? “Ine ndinachokera kwa Mulungu, ine ndikupita kwa Mulungu.”

¹⁹² Tsopano, ngati ine nditakuuzani inu kuti moyo wa John Dillinger unali mwa ine, inu mungayembekezere kuti ine ndizikhala ndi mfuti zazikulu kunjika kuno kuti ndikuwombereni. Ine nditakuuzani inu kuti moyo wa wojambula uli mwa ine, inu mungayembekeze kuti ine ndizijambula chithunzi cha wojambula. Mvetserani, mpingo! Ine sindikukudzulani inu. Taonani, ngati Moyu wa Khristu uli mu mpingo, iwo udzachita . . . Ngati Mzimu Woyera uli mu mpingo, ngati Lawi

la Moto ili limene sayansi yajambula chithunzi, ndi zina zotero, zimene ife timaziwona kuno mu mpingo nthawi zonse, ngati umenewo uli Mzimu wa Khristu, Iwo udzachita ntchito za Khristu. Yesu anati, “Ngati inu simungandikhulupirire Ine, mukhulupirire ntchito zimene Ine ndikuchitazo. Izo ndi zimene zikuchitira umboni za Ine.” Ngati Mzimu Woyera ukadali weniweni, ndiye Mzimu Woyera udzachitira umboni Wokha. Mukhulupirire ntchito za Mzimu Woyera.

¹⁹³ Pakhala pali kudzipangitsa kukhulupirira kochuluka ndi zodziveka. Iwe umayembekezera zimenezo. Mulungu anati izo zikanadzabwera. Koma izo zikuyesera kuchita chiyani? Ngati pali dola yabodza, iyo iyenera kupangidwa kuchokera kwa yeniyeni. Inu mwawawona anthu akudzinenera kuti ali nawo Mzimu Woyera, ndi kumakhala mu chigololo, ndi kumamwa, ndi china chirichonse, iwo alibe Iwo. Iwo akuyesetsa kuti awutsanzire Iwo. Koma pali weniweni winawake amene ali nawo Iwo, ali nawo Mzimu Woyera, ndipo Mulungu amatsimikizira Mawu Ake ndi zizindikiro zikutsatira. Hule anamva, iye anakhulupirira Izo.

¹⁹⁴ Tsopano, mkazi uyu, mkazi wa Chisurofonika uyu, iye anakhulupirira nayenso, Mgriki uyu. Iye anati, “Ambuye.” Choyamba iye anati, “Inu Mwana wa Davide.” Wamitundu alibe chodzinenera pa Khristu ngati Mwana wa Davide; zimenezo zinali kudzera mwa Mfumu Davide, mtundu wa Ayuda. Iye sanapereke chidwi chirichonse kwa iye. Koma pamene iye anatembenuka ndikuti, “Ambuye, ndithandizeni ine!” Amen, izo zinamupezeketsa Iye. Iye anali Ambuye wake; osati Mwana wa Davide, koma Iye anali Ambuye wake. “Ambuye, ndithandizeni ine!” Izo zinamugwira Iye. Ndipo iye...Iye anatembenuka. Anati, “Izo nzoona agalu amadya nyenyetswa pagome la ambuye. Izo nzoona.” Taonani chimene, mkazi ameneyo anali ndi mafikidwe oyenera kwa mphatso ya Mulungu. Kodi iye ananena chiyani? Iye anati iye anayifikira iyo molondola.

¹⁹⁵ Iye anamuchititsa iye manyazi, Iye anati, “Ndinu...Ine sindinatumizidwe kwa inu. Ndinu agalu mu kam’badwo kanu. Mitundu yanu si kanthu koma agalu. Ine sindinatumizidwe kwa inu.”

¹⁹⁶ Ndipo iye anati, “Izo nzoona, Ambuye.” Ndi amenewo Mawu. Amen. Khalani ndi Mawu. Chikhulupiriro nthawizonse chimawazindikira Mawu. “Koma agalu amadya zinyenyetswa pansu pa gome la mbuye wawo.” Izo zinamupezeketsa Iye. “Ambuye, ndithandizeni ine!”

¹⁹⁷ Iye anapotoloka ndipo Iye anati, “Pa kuyankhula uku, O mkazi, chachikulu ndi chikhulupiriro chako. Ndipo, pa kunena uku, mdierekezi wamusiya mwana wako wamkazi.” Chiyani, iye anapeza chiyani? Iye anafika pa mphatso ya

Mulungu mwanjira yoyenera. Inu muyenera kuifikira... Ndipo, kumbukirani, ameneyo anali Wamitundu woyamba yemwe anayamba wakhalapo ndi chozizwitsa chitachitidwa pa iwo ndi Mwana wa Davide. Kumbukirani, icho chinali chozizwitsa choyamba chimene chinachitidwa kwa Wamitundu, uko nkulondola, machiritso awa a mkazi wa Chisurofonika. Uko nkulondola. Iye anali nawo mafikidwe oyenera kwa mphatso ya Mulungu. Chikhulupiro chimavomereza kuti Mawu ndi olondola. Molemekeza, modzichepetsa. Mukuona?

¹⁹⁸ Inu simukuyendayenda ndikuti, “Huh! Ine—ine sindikhulupirira zinthu zimenezo. Ngati katekisimu yathu siyikunena zimenezo, uh-huh, ine sindikuziwona.” Ziribe kanthu zomwe katekisimu yanu imanena, iwe umaika katekisimu kapena china chirichonse pamwamba pa Mawu a Mulungu? Mawu a Mulungu ndi olondola. China chirichonse ndi bodza. Mukuona?

¹⁹⁹ Ndipo iye anabwera molemekeza, mwabata, molemekeza, modzichepetsa. Iwe uyenera kukhala wodzichepetsa. Njira yopitira mmwamba ndi pansu, nthawizonse. “Iye amene adzichepetsa yekha adzakwezedwa, koma iye amene adzikweza yekha adzachepetsedwa.”

²⁰⁰ Tamuwonani Marita tsiku limenelo. Oh, ine ndikudziwa kuti ine ndikukusungani inu nthawi yayitali, koma ine—ndidzakulupirani inu nthawi ina ndikudzakupangirani waufupi kwenikweni. Mvetserani, ine ndangokhala ndi zinthu zina zingapo zoti ndinene pakali pano, ine ndizipita. Ndikuyembekeza ine sindikutopetsa chipiriro chanu. Marita, iye anali kwambiri, anali ndi khama lochuluka kwambiri mu Kukhalapo kwa Yesu. Taonani, iye anabwera kumeneko ndipo iye anati, “Ambuye.” Tsopano, kumbukirani, iye anamutumiza Iye kuti abwere adzamupempherere m’bale wake, ndipo Iye sanachite zimenezo.

²⁰¹ Tsopano, mu Yohane 5:18, Yesu anati, Yohane 5:19, ine ndikukhulupirira ndi pamenepo, Yesu anati, pamene Iye ankadutsa pa dziwe la Betsaida kumeneko, ndipo Iye anawona, Iye ankadziwa kuti munthuyo anali ndi kufooka kwa zaka sarte-eyiti. Taonani, pafupifupi anthu thuu sauzande ataima pamenepo, ana a mutu wa madzi, opuwala, akhungu, osayenda, opinimbira, opiringizika. Yesu anadutsa pa dziwelo, anayang’ana pozungulira ponse, wodzaza chikondi, wodzaza ndi chifundo. Mwaona, ife sitikudziwa chimene chikondi chimatanthauza. Ife timazitenga izo kumbali ya umunthu. Wodzaza ndi chifundo, zedi, inu mukuyankhula zachifundo cha anthu. Chifundo chenicheni ndicho kuchita chifuniro cha Mulungu. Mukuona? Ndi zimenezotu.

²⁰² “Oh, ine sindinganene kanthu kwa iye, chifukwa iye ndi mnyamata wabwino. Iye—iye—iye amamwa, iye amachita *izi*.”

Iye akusowa Khristu. “Ine sindinganene zimenezo kwa iye, chifukwa iye wakhala wa mpingo umenewo nthawi yaitali. Ine sindingatchule machiritso Auzimu kwa iye.” Oh, m’bale, iwe sukudziwa chimene chifundo chiri.

²⁰³ Yesu anadutsa kumeneko, Iye ankadziwa chifuniro cha Mulungu. Kumbukirani, Iye basi—Iye anangomudzutsa munthu wakufa. Ndipo kumbukirani zomwe zinachitika apa. Iye anadutsa dziwe limenelo kumeneko, anapita kumbali kwa dziwe ili, kumeneko kunali amayi ndi ana aang’ono. Iwo anali akuyesetsa kuti amudikirire Mngelo wa Ambuye kuti avutitse madziwo. Iye anayenda chodutsa kumeneko, Iye anapita kwa munthu amene anali ndi kufooka, tiyeni tinene kuti vuto la thumbo. Iye anali ndi zimenezo zaka sarte-eyiti. Izo zinali zitapinimbira. Izo sizinali kuti zimupha iye. Iye anati, “Kodi iwe upangidwa wamphumphu?” Nanga bwanji wakhungu uyu, wolumala, wakhungu, wosayenda, wopinimbira? Anati, “Kodi iwe upangidwa wamphumphu?” Mwaona, Iye ankadziwa basi koti apite. Mulungu, Mawu, anamutsogolera Iye. Tsopano, Iye anati, “Kodi iwe upangidwa wamphumphu?”

²⁰⁴ Iye anati, “Bwana, ine ndiribe aliyense woti andiyike ine mu dziweli.” Iye amakhoza kuyenda. Anati, “Pamene ine ndikubwera kumeneko, winawake amandiposa ine.”

²⁰⁵ Iye anati, “Tenga mphasa yako ndipo kazipita kunyumba yako.” Iye anafunsidwa. Ndipo iwo anamubweretsa Yesu ku bwalo la mulandu kuti akamufunse Iye.

²⁰⁶ Ndipo ngati Iye atachita chinthu chomwecho lero, Iye angafunsidwe. Kulondola. “Iye anasiya thuu sauzande, nanga bwanji iwowo? Ine ndikumudziwa M’bale wachikulire *Wakuti-ndi-wakuti* kumusi uko. Mlongo *Wakuti-ndi-wakuti*, iye ndi mkazi wabwino. Wakhala ali uko kwa zaka twente. Ngati pali Mulungu aliyense za Iye, Iye akanapita kumeneko ndi kukachita zimenezo.” Mdierekezi wakale yemweyo akunena chinthu chomwecho lero. “Ngati Iwe uli. Ngati ichi chiri. Ngati icho chiri.” Mdierekezi wakale yemweyo, mwaona, chinthu chakale chomwecho.

²⁰⁷ Kotero Afarisi awa ankamufunsa Iye kuntunda uko za zinthu izi. Mpenyeni Iye, “Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha koma chimene Iye awawona Atate akuchita.” Iye—Iye ankakhala ndi masomphenya. Masomphenya ankamusonyeza Iye. “Chimene Ine ndiwawona Atate akuchita, chimenecho amachita Mwana chimodzimidzi.” Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mwaona, Mulungu yemweyo.

²⁰⁸ Tsopano, Marita, mu Kukhalapo Kwake, iye anali ataima pamenepo. Iye anati, “Ambuye, ngati Inu mukanakhala muli kuno.”

209 Tsopano, nchifukwa chiyani Iye sanabwere? Chifukwa Atate anali atamuwonetsa Iye masomphenya kuti Lazaro anali woti afa. Tsopano, taonani, iwo—iwo anatumiza, ndipo Iye anapita ku mzinda wina. Ndipo iwo anatumanso, Iye anapita ku mzinda wina. Kenako potsiriza Iye anati, “Lazaro akugona.” Oh, iwo. . . Ako ndi kanenedwe kamene Iye anali nako. Sipamakhala imfa kwa Mkhristu. Ife tikudziwa zimenezo.

“Oh,” iwo anati, “ngati iye akugona, iye akuchita bwino, akupuma.”

210 Anati, “Koma iye wafa,” anawauza iwo mu chinenero chawo. “Koma Ine ndikupita ndikamudzutse iye.” Oh!

211 Akuyenda kupita kumene iye anali, oh, ine ndikukhoza kuziwona izi. Kubwera mu mzinda, ine ndikukhoza kuwamva Ayuda akuti, “Uh-huh! Ndi ameneyo mchiritsi Wauzimu! Uh-huh. Iwo anasiya tchalitchi chawo, china chirichonse, kuti amutsatire Iye. Ndipo pamene vuto lenileni linabwerapo, ngakhale bwenzi Lake, Iye anachoka mu mzindawo. Anatuma, tsopano Iye wabwererako.” Yesu anayenda mopitirira.

212 Koma Marita wamng’ono, chinachake pansi mu mtima mwake, chinachake. Iye nthawizonse amakhala ngati wozengereza, iye amafuna kuti nyumba izikhala yoyera ndi chirichonse, ndipo Maria ankamvetsera ku Mawu. Koma apa ndi pamene iye anawonetsa mtundu wake, iye anazembera apo pomwe ndipo anapita kumusi uko. Tsopano, iye, inu mukudziwa chimene ine ndimakhulupirira, iye anali atawerenga za mkazi wa Chishunemu uja, Shunemu, inu mukudziwa, mu Baibulo. Tsopano, kodi iye ananena chiyani? Iye anatuluka, iye anati, “Ambuye.” Ndicho chimene Iye anali. Izo zinkawoneka ngati iye anali ndi ufulu womuzazira Iye, kunena kuti, “Chifukwa chiyani inu simunabwere? Bwanji, ife sikuti. . .Ife tikukhulupirira tsopano Inu ndinu woyera wodzigudubuza kwenikweni.” Mwaona, chozizwitsa chimenecho sichikanati chichitike.

213 Ndipo ndicho chifukwa izo sizingakhoze kuchitika lero. Oh, Iye ali pano mu mawonekedwe a Mzimu, osati kuti inu mumamuwona Iye, koma chiyani: Iye ndi Mzimu ndi Mawu Ake. Mukuona? Oh, zedi. Inu mumapempherera chitsitsimutso, ndipo icho chimachitika mu mpingo, chinachake kapena chimzake chimachitika, ndipo winawake amafuula “ulemelero kwa Mulungu, aleluya,” inu mungatseke tchalitchi. Simukudziwa kuti chitsitsimutso ndi chiyani. Khristu amabwera ku tchalitchi, ndiyeno inu simumamulandira nkomwe Iye. Kuchita chozizwitsa ndi kumuchiritsa winawake, ndi kuti, “Chabwino, izo zikhoza kukhala kuti zinali kuwerenga maganizo.” Nzosadabwitsa Iye sangakhoze kuchita pakati panu. Nzosadabwitsa mpingo wa Laodikaya, Iye ali kunja, akugogoda, kuyesetsa kuti abwerere mu mpingo Wake Womwe. Ndiwo m’badwo umene ife tikukhalamo tsopano. Zipembedzo

izi zamukankhira Iye kunja mpaka Iye ali panja, akuyesetsa kuti abwerere mkati. Ndiko kulondola, waikidwa panja!

214 Tsopano, ife tikupeza kuti Marita anayenda kupita kwa Iye, anati, “Ambuye, ngati Inu mukanakhala kuno, m’bale wanga sakanafa. Koma ngakhale tsopano, chirichonse chimene Inu mumufunsa Mulungu, Mulungu apereka icho kwa Inu.”

215 Mpenyeni Iye, Iye anamuyesa iye. Iye anati, “M’bale wanu adzawukanso.”

216 Anati, “Inde, Ambuye. Iye anali mnyamata wabwino, iye adzabwera mu chiukitsiro cha aliyense. Iye adzawuka mu tsiku lotsiriza.”

217 Anati, “Ine ndine Chiukitsiro ndi Moyo.” Apo anaika yesero. Munthu ataima pamenepo akuti... Iye anali Munthu yekhayo amene anayamba wakhalapo, Munthu yekhayo amene ati adzakhalepo moyo amene akanakhoza kunena zimenezo, Mwana wa Mulungu, anati, “Ine ndine chiukitsiro ndi Moyo.”

218 Baibulo linati, “Analibe kukongola kuti timuyang’ane Iye.” Mwinamwake mapewa Ake aang’ono akugwa, akusanduka otuwa, pamene Iye anali usinkhu wa zaka sarte ndipo Iye ankayesedwa kuti anali fifite.

219 Anati, “Ndiwe wa usinkhu wa zaka fifite zokha, ndipo ukuti Iwe unamuwona Abrahamu. Tsopano ife tikudziwa kuti Ndiwe wamisala.” Mukuona? ntchito Yake mwinamwake inamufikitsa Iye kumeneko.

220 Iye anati, “Asanakhalepo Abrahamu, Ine ndine.” Amen. Iwo samadziwa zimenezo. Pamenepo Iye anaphimbidwa mu mnofu wa munthu.

221 Anati, “Ine ndine chiukitsiro ndi Moyo. Iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye anali wakufa, komabe iye adzakhala moyo. Aliyense amene akhala moyo nakhulupirira mwa Ine sadzafa konse. Kodi inu mukukhulupirira zimenezi?”

222 Iye anati, “Eya, Ambuye. Ine ndikukhulupirira kuti Inu ndinu Mwana wa Mulungu amene anali woti adzabwere mdziko lapansi.”

“Kodi inu munamuika kuti iye?”

223 Ine ndiri ndi kanthu kakang’ono pano kamene ine nthawizonse ndimakanena, inu mukudziwa, ine ndikuyembekeza ngati ine ndikupweteka kumverera kwa aliyense ine sindikuchita izo modziwa. Mkazi wa Christian Science anandiuza ine nthawi ina, iye anati, “M’bale Branham, inu mumabwekerera mochuluka kwambiri za Yesu.”

224 Ine ndinati, “Oh, ayi, ayi.” Ine ndinati, “Ine sindikubwekerera theka mokwanira. Ndikukhumba ine ndikanakhala ndi chinenero china chowonjezera chimene ine ndikanamubwekerera nacho Iye.” Mukuona?

Ndipo iye anati, “Chabwino, inu mukumupanga Iye kukhala Mulungu.”

Ine ndinati, “Iye anali Mulungu! Iye akadali Mulungu. Iye nthawizonse adzakhala ali Mulungu.”

Iye anati, “Iye anali wachivundi. Iye anali munthu.”

Ine ndinati, “Iye anali ziwiri zonse Munthu ndi Mulungu.”

225 Iye anati, “Ine nditsimikizira kwa inu kuti Iye anali basi munthu wachivundi, mwa Baibulo lanu lomwe.”

Ine ndinati, “Ndiroleni ine ndikumvereni inu mukuchita izo.”

226 Iye anati, “Yohane Woyera, mutu wa 11, Yesu anapita ku manda a Lazaro ndipo Iye analira.”

Ine ndinati, “Kodi limenelo ndi Lemba lanu?”

Iye anati, “Inde.”

227 Ine ndinati, “Mlongo!” Ine sindikutanthauza izi mosinjirira. Ano si malo a nthabwala, koma ine ndinangonena zimenezo kwa iye. Ine ndinati, “Zimenezo ndi zopyapyala kuposa nsuzi wopangidwa kuchokera ku mthunzi wa nkuku imene inafa ndi njala.” Ine ndinati, “Bwanji, iwe ukudziwa bwino ndipo mwabwino kuti icho sichikanakhoza kukhala chinthu chotero monga icho.” Ine ndinati, “Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake.”

228 Apa Iye akupita, wa mapewa-akugwa, akulira, Iye amalira ndi inu pamene inu mukulira. Iye amamverera kupwetekedwa kwanu. Iye ndi Wansembe Wamkulu akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zanu. Akulira, akupita kutsikira kumanda, akudziwa chimene Atate anali atamuuzza Iye. Pakuti Iye anati Iye samachita kanthu mpaka Atate atamuwonetsa Iye. Apo Iye anali, mwaona, akupita. Iye anali woti amuukitsa iye, koma Iye ankakhoza kulira mwa umunthu ndi anthu. Akupita ku manda, akulira. Koma pamene Iye anaima pamenepo, oh, mai, anati, “Chotsani mwalawo.”

229 Anati, “Iye akununkha!” Mphuno yake inali itagwera mkati. Maora sevente-thuu, mwaona, kapena masiku anai ndi mausiku. Mwaona, nkhope yake yagwera mkati, iye wavunditsidwa, iye wavunda.

230 Anati, “Chotsani mwalawo.” Iye anaima kumbuyo uko ndipo anati, “Atate, Ine ndikukuthokozani Inu kuti Inu nthawizonse mumandimva Ine, koma Ine—Ine ndangonena izi,” mwaona, Iye anali atamuuzza kale Iye, Iye anati, “Ine ndikungonena izi chifukwa cha awa amene aimirira: Lazaro, dzuka!” Ameni. Ndipo munthu amene anali atafa kwa masiku foro, anaima pa mapazi ake ndipo anakhalanso moyo. Ameneyo anali woposa munthu. Ameneyo anali woposa munthu. Ndithudi anali.

²³¹ Ameneyo anali woposa munthu amene anatsika kuchokera m'phiri usiku wina, wanjala, akufunafuna chinachake choti adye. Iye anali Munthu, Iye anali ndi njala ya chinachake choti adye. Koma pamene Iye anatenga nsomba zisanu, kapena mabisiketi asanu ndi nsomba ziwiri, ndi kudyetsa faivi sauzande, ameneyo anali woposa munthu. Uko nkulondola. Izo nzoona. Inde, bwana.

²³² Iye anali Munthu pamene Iye anali atagona kumbuyo kwa ngalawa ija usiku uja, atatopa kwambiri, ukoma unachoka mwa Iye, kulalikira ndi machiritso, ndipo mdierekezi anabwera, ndipo mwinamwake adierekezi teni sauzande a pa nyanja, anati, "Ife timumiza Iye tsopano, Iye akugona." Monga iwo anachitira ndi Paulo kunja uko mu nkuntho. "Ife tamupezeketsa Iye tsopano, ife tamukola Iye. Iye akugona, ife timiza ngalawa imeneyo." Mdierekezi akuwomba mphepo yake kudutsa pamenepo, ndipo iyo ikunjanja chokwera ndi chotsika monga choncho. Mafunde sanamudzutse Iye nkomwe. Iye anali Munthu atagona kumbuyo uko, atatopa, akugona.

²³³ Koma pamene Iye kamodzi anadzuka, oh, mai! "Oh, pitani mukamudzutse Yesu!" Anayika phazi Lake... Oh, mpingo, ndicho chimene inu muyenera kuchita. Ndikukhumba ine ndikanakhala nayo nthawi ina yomwe ine ndikanadzalalikira tsopano, onani, pa zimenezo. Mukuona? Anaika phazi Lake pa chotetezera cha ngalawayo, anayang'ana mmwamba, anati, "Mtendere, pakhale bata." Mukuona? Ndipo mafunde ndi mphepo zinamumvera Iye. Ameneyo anali woposa munthu, zinatengera Mulungu kuti achite zimenezo.

²³⁴ Eya, Iye analira pa mtanda, kufuna chifundo. Uko nkulondola. Anamva ludzu pa mtanda. Iye anafa ngati munthu. Koma mmawa wa Isitara, pamene Mngelo anagudubuza mwalawo, ndipo Munthu amene anali atafa, anagonjetsa zonse imfa, gehena ndi manda, anatulukira, anagonjetsa imfa, hade ndi manda. Anati, "Ine ndine Iye amene ndinali wakufa, ndi wamoyo kwanthawizonse." Ameneyo anali woposa munthu. Ameneyo anali Mulungu mwa Munthu ameneyo. Inde, bwana.

²³⁵ Chikhulupiriro sichikana konse Choonadi Chake. Oh, monga ngati kunena kuti, "Lawi la Moto, izo sizinali zoon. Ndipo zozizwitsa za Mose sizinali zoon," iwo nthawizonse ankati. Ziribe kanthu kuti ndi zopusa bwanji, izo zimakhala ndendende ndi Mawu. Ndendende. Oh, inu mukhoza kukhala—inukhoza kukhala olimbikira. Inu mukhoza kukhala olimbikira pamene inu mugwira kwenikweni Mawu a Mulungu, pamene inu mugwiritsitsa kwa Iwo.

²³⁶ Monga Mikaya anali, Mikaya uko komwe, pamene aneneri foro handiredi anali ataima pamenepo, akuti, "Pitani uko, Ahabu, pitanibe kuntunda uko." Mikaya ankadziwa kuti masomphenya ake anali molingana ndi Mawu a Mulungu. Iye

anayankhula Mawu mulimonse. Iwo anati, “Ife tikakuphera iwe mu ndende, ndipo tikakupatsa iwe madzi a chisoni ndi mkate wa chisoni.”

²³⁷ Iye anati, “Kandilowetseni ine mkati ngati inu mukufuna kutero.” Kodi iye anali ndani? Iye anali wolimbikira. Iye ankadziwa Mawu a Mulungu. Iye ankadziwa chifuniro cha Mulungu. Iye anali atawona masomphenya. Iye ankadziwa chimene icho chinali. Masomphenya anabwera kuchokera kwa Mulungu, chifukwa masomphenyawo ankafanana ndi Mawu a Mulungu. Lero, wokhulupirira aliyense ayenera kuti azimenyera, ndipo inu muyenera kuti muzimenyera, inunso.

²³⁸ Mwamuna kuno nthawiyina kale anali kundiuza ine, anati iye anapita ku...anati, “Inu mukudziwa, a—mdierekezi wamng’ono kwambiri wa pafupifupi kukula *chonchi* anaima patsogolo panga nthawi ina mu loto.” Iye anati, “Mdierekezi ameneyo anati, ‘buu’; ndipo ine ndinapita, ‘umph.’ Ndipo,” anati, “nthawi iliyonse ine ndikalumphira mmbuyo, iye amakula ndipo ine ndimachepera.” Anati, “Chinthu choyamba inu mukudziwa, ‘buu,’ ndipo ine ndinalumphira chammbuyo. Ndipo iye...nthawi iliyonse ankapita, ‘buu, buu’” kumalumpha pa iye. Anati iye amakhoza kubwerera, kubwerera, kubwerera. Anati, “Iye anali akukula kuposa momwe ine ndinaliri.” Ndipo anati, “Ine ndinkadziwa kuti ndinkayenera kumumenya iye. Chotero ine—ine sindinapeze kalikonse, chotero ine ndinangotola Baibulo, ndipo ine...iye anapita ‘buu’; ine ndinapita ‘buu,’ inenso.” Anati, “Iye anayamba kuchepa.” Uko nkulondola.

²³⁹ Ndicho chimene inu muyenera kuchita, muziwatenga Mawu a Mulungu. Iwe sukusowa kuti uzinena kuti “buu,” koma uziti “PAKUTI ATERO AMBUYE!” Kukhala wolimbikira, kuyima pa Mawu! Ndi Choonadi. Ife timawakhulupirira Mawu lero. Ife timawakhulupirira Iwo monga Mikaya anawakhulupirira Iwo. Ife timawakhulupirira Iwo monga ena onse a iwo amakhulupirira. Ziribe kanthu kuti ndi angati anganene kuti Iwo ndi olakwika, Iwo akadali owonabe. Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iye adzazichitanso.” Kodi munthu aliyense angakuchizeni inu? Ayi, bwana. Zinachitika kale, inu munachiritsidwa kale. Kodi munthu aliyense angakupulumutseni inu? Izo zinachitika kale. Ndi angati akukhulupirira zimenezo? “Iye *anavulazidwa* chifukwa cha zolakwa zathu. Iye *anatunduzidwa* chifukwa cha kusaeruzika kwathu.” Nkulondola uko? Kulondola. “Ndipo ndi mikwingwirima Yake ife *tinachiritsidwa*,” tensi yakale. Chirichonse chimene Iye angakhoze kukuchitirani inu icho chinachitidwa kale.

²⁴⁰ Tsopano Iye anaika mu mpingo, kuti awusunge mpingo mu mzere ndi Mawu, chiyani? Atumwi, aneneri, aphunzitsi, abusa, alaliki, maudio a mpingo. Otumidwa ndi Mulungu,

osati oitanidwa ndi munthu. Otumidwa ndi Mulungu, amuna odzodzedwa kuti awuyike mpingo mu mzere. Tsopano, ndi chiyani chimenecho? Mphatso za mzimu mu mpingo. Osati gulu la otentheka, koma moona mphatso za Mzimu mu mpingo. Ndiko kulondola, kuwusunga mpingo. Ngati mpingo weniweni unadzozedwa ndi Mulungu, unadzazidwa kwenikweni ndi Mzimu Woyera, ngati tchimo lingawonekere mu mpingo, izo zingakhale zina monga Anania ndi Safira. Pamene mpingo weniweni...ine ndikufuna kuti ndidzayende kulowa mwa umodzi, kudzawaona akazi onse ndi amuna ali pansi pa Mphamvu ya Mzimu Woyera. Ngati winawake anachita chinachake cholakwika, Mzimu Woyera nkuwuka pamenepo ndi kuwulula izo. Iwo angayeretse zimenezo. Ndizo mphatso za Mzimu mu mpingo. O Mulungu, titumizireni ife mpingo wonga umenewo, titumizireni ife umodzi wonga umenewo. Inu mukukhulupirira zimenezo? Khristu, kodi Iye anafa? Iye ali moyo.

Iye anali bwanji? Iye ananena pamenepo kwa mkaziyo . . .

²⁴¹ Iye anati, pamene Mfarisi anamufunsa Iye za chizindikiro, Iye anati, “Iwe m’badwo wachigololo umafunafuna chizindikiro.” Ndi kulondola uko? Woyipa ndi wachigololo! Iye anati, “Iwo adzachiyeza icho. Iwo adzapeza chizindikiro, woipa ndi wachigololo umenewo.” Ndi liti pamene panali m’badwo woyipa ndi wachigololo koposa umene ife tiri nawo tsopano? Ndi liti pamene panali tchimo lochulukirapo? Ife tiri nawo anthu ambiri pa dziko lapansi pakali pano, iwo amatiuza ife, monga anthu ambiri pa dziko lapansi pakali pano amene anayamba akhalapo pa dziko lapansi chiyambireni Adamu, ali pa dziko lapansi pakali pano. Uno ndi m’badwo woyipa ndi wachigololo umenewo. Amuna ogonana, zisokonezo, chirichonse, chikuwonjezekera mwa masauzande ndi masauzande. Mipingo ikugwa, “Ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa kuposa kukonda Mulungu, akuswa pangano, onenera zabodza, osadzigwira, onyozza iwo amene ali abwino, okhala nawo mawonekedwe aumulungu,” monga Mzimu unanena kuti, “ndi kumakana Mphamvu yakeyo. Kwa oterowo chokaniko!” Mukuona? Baibulo linati, “Chokaniko!” Ife tikukhala mu tsiku limenelo.

²⁴² Tsopano, kumbukirani, pali anthu amene amapita pamenepo, nkumati, “Ine ndiri nayo mphamvu yokuchiza iwe.” Munthu ameneyo akukuuza iwe bodza. Iye alibe mphamvu yokuchizani inu. Khristu anachita kale zimenezo! Oh, mwa kuvomereza kwa machimo, ndi zina zotero, ndi wansembe wina kapena kukhala mtumiki kumakhululukira machimo anu? Ayi, bwana, machimo anu anakhululukidwa kale. Pamene Khristu anafa pa mtanda, Iye anati, “Izo zatha.” Chiyani? Dongosolo lathunthu, chirichonse. Khristu anachita izo pa mtanda. Inu munapulumsidwa kale. Wochimwa aliyense

anapulumsidwa, koma izo sizidzakuchitirani inu ubwino uliwonse mpaka inu mutazivomereza izo. Inu mukhoza kupita kumeneko pa guwa ndi kukakuwa, kulira mpaka kuchita imvi ndipo tsitsi lanu nkuthothokapo, izo sizidzachita ubwino uliwonse mpaka inu mutakhulupirira, mukhulupirire kuti Khristu anafa mmalo mwanu, ndipo inu... Iye anafera chitetezero cha machimo anu, pamene inu mumuvomereza Iye ngati Mpulumutsi wanu. Zikatero chipulumutso chimabwera kwa inu. Chinthu chomwecho ndi machiritso. “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.”

²⁴³ Pali chinthu chimodzi chokha chimene Khristu akhoza kuchichita lero kuti asonyeze kuti Iye ali. Chinthu choyamba, ndicho, inu muyenera kukhulupirira pa maziko a Mawu Ake. Ndiko kulondola ndendende, choonadi cha Mawu. Koma Yesu anati, “Ntchito zimene Ine ndikuzichita!” Tsopano, Iye sanati konse, “Ine ndimuchiritsa” aliyense. Ngati Yesu anati, “Si Ine amene ndikuchita ntchitozo, ndi Atate Anga amene akukhala mwa Ine,” tsopano ngati Yesu sakanatenga dzina la “mchiritsi Wauzimu,” nanga bwanji mbuli ina yosauka monga ine, kapena wina aliyense, kapena wina aliyense, ndi kumayesera kukhala mchiritsi Wauzimu? Inu mungakhale bwanji mchiritsi Wauzimu pamene izo zinachitika kale, aliyense wokhoza kuchiritsidwa anachiritsidwa kale? Inu muyenera kuvomereza izo, kukhulupirira izo. Tsopano, kodi ndi choonadi? Ndi chimene ife tikufuna kuti tidziwe. Kodi ndi zoonadi?

²⁴⁴ Tsopano, ngati simungatenge mawu anga, inu mukhoza kumangopita, kapena anu... Ine sindingakhoze kutenga mawu anu, izo ziyenera kupita. Koma Mulungu sali mwanjira imeneyo, Iye amatumiza mphatso mu mpingo, atumwi. Kodi mtumwi ndi chiyani? Wamishonare. Mmishonare, ndi mawu a *mishonare* amatanthauza “mmodzi yemwe watumidwa.” *Mtumwi* amatanthauza “mmodzi yemwe watumidwa.” *Mneneri*, ameneyo ndi “mpenyi.” M’busa, mphunzitsi, mlaliki, zinthu zonse zimenezo, iwo amawagawa molondola Mawu a Mulungu, kuwabweretsa Iwo pansu, ndiyeno a—mphatso za Mzimu kuti zizigwira ntchito mu mpingo, kuti zikatsimikizire Mawu, kuti zikawonetsera kuti Yesu Khristu akukhala mu mpingo.

²⁴⁵ Tsopano, ife tonse tikudziwana, ili ndi gulu lathu lokha la mpingo. Ine sindikudziwa ngati alipo aliyense... Ine sindimakhala kuno mochuluka kwambiri kuti ndidziwe ngati iwo ali alendo kapena ngati iwo siali alendo, ndi zina zotero. Koma, abwenzi, lero, anthu inu amene mukudwala tsopano, ngati pakanakhala chirichonse choti ndichite kuti chikuthandizeni inu, ine ndikanachita icho. Ngati ine ndikanadziwa kuti winawake pano akudwala, makamaka mlongo uyu apa ine ndikumuwona pa machira, ngati ine ndikanadziwa kuti panali chinachake chimene ine ndikanatha

kuchichita, monga kutenga, kugwira ntchito mwakalavulagaga kuzungulira mdadada wa mu mzinda, ndikuzungulira, ine ndikanachita zimenezo. Ine ndikanakafika panja pamenepo ndi kukati, “Musakokere ambulera iliyonse pa ine, ngati kukugwa mvula, mungondilola ine ndizikankha. Ine ndikufuna kuti ndimuwonetse Mulungu kuti ndine woonamtima.” Tsopano, izo sizingachite ubwino uliwonse. Ine ndakhalapo mu Afrika, ndipo ndikudziwa kumene iwo amagona pa zisonga mu India, ndi mitundu yonse ya zinthu, kumachita nsembe kwa milungu, ndi kuwapereka ana awo kwa ng’ona, ndi china chirichonsecho. Izo si zimenezo; kumeneko ndi kudzipereka, koma munthu akhoza kudya chidulo cha karboliki kukhala mankhwala. Mukuona? Mwaona, iwe—iwe uyenera... Chinthu chimene chiri choonadi ndi chimene ife tikufuna kuti tidziwe, ndipo Mulungu amachitira umboni za Choonadi Chake. “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iye adzazichita.” Ahebrei 13:8, “Yesu Khristu yemweyo!”

²⁴⁶ Kodi Iye angakhale chiyani ngati inu mutamufuna Iye lero? Ngati ine nditakuuzani inu kuti Khristu ali mwa ine, Khristu ali mwa inu, kodi ife tingakhoze kuyembekezera chiyani? Kodi inu mungamayang’ane mwamuna amene ali ndi kolala yake yotembenezidwa, ndi chinachake? Ayi, ayi, Iye sanachite monga chomwecho, Iye ankavala monga anthu ena onsewo. Ngati iye anali ndi zipsyera mdzanja lake? Munthu aliyense akhoza kupanga zipsyera mdzanja lake, zidindo za minga. Iwo ali ndi madazeni a izo kudutsa mdzikoli tsopano, otsanzira, ndi magazi ndi moto ndi utsi, chirichonse. Zimenezo si—zimenezo si Mawu! “Ntchito zimene Ine ndikuzichita!” Yesu anati, “Ngati inu simungakhoze kundikhulupirira Ine, mukhulupirire ntchito zimene Ine ndikuchitazi. Izo zichitira umboni za Ine. Izo ndi zimene zimanena Yemwe Ine ndiri.”

²⁴⁷ Tsopano tiyeni tipemphere kamphindi chabe. Mukhale ndi zopempha zanu pa mtima wanu. Atate Akumwamba, ine ndikudziwa izi zakhala zamwano ndi zolimba. Ine ndikukupemphani Inu kuti mukhale wachifundo. Ine sindikutanthauza... Inu mukuwudziwa mtima wanga, Ambuye, koma ine ndikungopemphera kuti Inu mundithandize ine tsopano. Ine ndikupemphera kuti Inu mulole mawu awa, ngakhale iwo ali osweka ndi odulidwa, ndipo—ndipo osati monga mtumiki ayenera kuchitira, Ambuye. Ndipo ine kuno, wosaphunzira, sindikudziwa momwe ndingayankhulire kwa anthu, koma chonse chimene ine ndikudziwa ndi chakuti Inu munalonjeza ngati ine ndidzatsegule pakamwa panga Inu mukanadzapadzazitsa ipo. Izo zakhala ziri zaka sarte-wani ine ndikukudalirani Inu mu zimenezo. Chotero, Atate, penapake, mwinamwake ena a anthuwo atolera Mawu pang’ono, iwo amene akudwala, kapena iwo amene akusowa Khristu. Iwo ali—iwo ali kunjā uko kwina kwake. Iwo—iwo akukusowani

Inu, Ambuye, ndipo ine ndikuyembekeza kuti chinachake chanenedwa chimene chiti chidzadzutse chikhulupiriro chawo mu malonjezo Anu. Ine ndikupemphera kuti Inu mupereke dalitso limenelo.

²⁴⁸ Tsopano pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, kodi alipo amenewo muno amene sakumudziwa Khristu ngati Mpulumutsi, anganene kuti, “M’bale Branham, ine—ine sindingafune kuti ndife monga chonchi. Ine—ine sindiri woyenera kuti ndife. Ngati ine nditafa, ine ndingataike. Ine sindinabadwe mwatsopano. Ine—ine ndithudi ndikukhumba pemphero lanu pakali pano. Mundipempherere ine, ndine wochimwa?” Ingokwezani dzanja lanu mmwamba, mutero inu, munene kuti, “Mungondikumbukira . . .” Mulungu akudalitseni inu, inu, inu, inu. Mulungu akudalitseni inu. Mukutanthauzadi zimenezo kuchokera mu mtima mwanu. Mulungu akudalitseni inu. Dazeni kapena manja awiri mu gulu laling’ono ili la anthu pano. Anthu apang’ono odzadza mdzanja awa pano, pafupifupi handiredi kapena thuu, chinachake monga choncho, ndipo apa pali manja dazeni. Pomwepo pamene inu muli. Maguwa mwadzaza ndi ana amene akhalamo. Sizingatheke kuti ine ndingakubweretseni inu ku guwa, koma, pamene inu mulipo, mupemphere ndi ine.

²⁴⁹ Atate Akumwamba, ine ndikubweretsa kwa Inu anthu awa amene anakweza manja awo. Ine ndikukhulupirira mu kuwona mtima kwakuya iwo anachita izo. Aloleni iwo adziwe kuti iwo anaswa lamulo lililonse la sayansi pomwe apo. Sayansi imatsimikizira kuti mikono yathu iyenera kulendewera pansu, chifukwa mphamvu yokokera pansu ya dziko lapansi imatitsitsira ife pansu. Koma izo zikusonyeza kuti munali Mzimu mwa iwo umene uli ndi ulamuliro, mphamvu ya nkono umenewo, kuti iwo analikwezera ilo kwa Mlengi yemwe analipanga ilo. Izo zinasonyeza apo pomwe. Izo sizikanakhoza kutsimikiziridwa mwasayansi, chifukwa Mzimu umangodziwika . . . Ndi chikhulupiriro. Ife timakhulupirira mwa Iwo. Ndipo apa Mzimu wabwera kwa iwo ndipo wawauza iwo kuti akweze mmwamba manja awo, kuti iwo akufuna kuti apulumutsidwe.

²⁵⁰ Tsopano, Atate Mulungu, ine ndiku- . . . Ine ndikubwereza malonjezo Anu. Ambuye Yesu Khristu anati, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, “Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba. Ndipo onse amene Atate andipatsa Ine, adzabwera kwa Ine. Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya. Iye amene adya Thupi Langa ndi kumwa Magazi Anga, ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Ine ndidzamuukitsa iye pa tsiku lotsiriza.” Awa ndi malonjezo. Tsopano, anthu awa sakanakhoza kukweza manja awo kupatula ngati panali Mzimu pamenepo umene unawauza iwo kuti

amalakwitsa. Iwo sakanakhoza kuchita izi pokhapokha Inu mutawakonzeratu iwo. “Onse amene Atate ana,” *ana*, tensi yakale, “anandipatsa Ine, adzabwera.” Ife tinakonzedweratu ku Moyo Wamuyaya. Iwo amene Iye anawadziwiratu, Iye wawaitana; iwo amene Iye wawaitana, Iye wawalungamitsa; iwo amene Iye wawalungamitsa, Iye wawapatsa kale ulemelero pamaso pa Mulungu. Ndi masomphenya aakulu chabe a Mulungu amene akupita motsatira, akukwaniritsidwa. Anthu awa, asanaikidwe maziko a dziko lapansi, Inu Amene muli wopandamalire munawudziwa msonkhano mmawa uno, ndipo munadziwa kuti iwo akanadzakweza manja awo, ndipo tsopano iwo akweza dzanja lawo.

²⁵¹ Ndizo zonse zimene ine ndikuzidziwa kuti ndiyendere nazo, Ambuye, ndi Mawu Anu. Ndiye, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikupereka kwa Inu awa amene akweza manja awo, monga zikho za Mawu Anu. Asungeni iwo, O Ambuye Mulungu, palibe amene angawakhwatule iwo kuchokera mdzanja Lanu. Apatseni iwo Moyo Wamuyaya. Mulole iwo akapeze mpingo, kapena akhale pomwe pano mmawa uno ndipo abatizidwe kwa chikhululukiro cha machimo awo, kapena kuvomereza kwa chikhulupiriro chawo. Mulole iwo, pamene iwo azituluka kuchokera mmadzi, monga Mzimu Woyera pachiyambi unasanthira pa madzi, mulole Mzimu Woyera ukakhale kumeneko kuti ukadzazitse mitima yawo ndi miyoyo. Perekani izi, Ambuye. Mulole iwo akakhale moyo waumulungu masiku onse a moyo wawo, ndi kuperekedwa ngati zikho ndi ngale mu korona Wanu pa tsiku limenelo. Kudzera mwa Yesu Khristu Ambuye wathu, ife tikupempha izi. Amenii.

²⁵² Ambuye akudalitseni inu. Tsopano, ine kwenikweni ndimayenera kukhala nditachokapo ora lapitalo. Koma tsopano ife tiyitana mzere wa pemphero. Dikirani, kodi alipo makadi apemphero aliwonse kunjako? Kodi aliyense ali ndi makadi a pemphero? Billy ali kuti, kodi Billy alipo? Wani mpaka fifite? Iye akuti anapereka makadi a pemphero fifite. Chabwino, tsopano, ife sitingakhoze, alipo ochuluka kwambiri aimirira. Tsopano, kodi inu nonse mungatipatse ife mphindi pang’ono chabe tsopano? Ngati inu . . . Tsopano, zonse zimene ine ndanena . . . Tsopano, basi—mphindi chabe, ine ndikudziwa kuti chakudya chamadzulo sichipsyerera. Dikirani miniti, *Izi* ndi zoposa, *Izi* ndi zabwino kuposa chakudya chamadzulo (iwo ayenera kukhala): Mawu a Mulungu.

²⁵³ Mvetserani abwenzi, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu funso ili ine ndisananene izi. Kodi ife timapitiranji ku tchalitchi? Zonsezo ndi za chiyani? Ngati kulibeko chiwukitsiro cha akufa, ngati kulibeko chiwukitsiro, ndiye tiyeni ife tizidya, tizimwa, ndi kumasangalala, pakuti ife sitiri kanthu koma zipika, agalu, ndi zina zotero, mulimonse. Ife sitimakhulupirira zimenezo. Ife timadziwa kuti alipo Mulungu wamoyo. Ndithudi.

Chabwino, ngati Iye ali Mulungu wamoyo, ine ndikufuna kuti ndikufunzeni inu chinachake. Ndiye Mawu awa amene ine ndinati, inu mukhoza kugwirizana nane, inu mukhoza kusagwirizana nane. Koma ngati inu mukugwirizana nane, ndiye komabe inu—inu mukhoza kufunsabe izo mpaka inu mutaziwona izo zikuwonetseredwa. Uko nkulondola. Ngati iwo ali Mawu a Mulungu, Mulungu ayenera kusunga Mawu Ake. Ngati Iye sawasunga Iwo, chabwino, ndiye si Mulungu, ndiye ine—ine ndakhala wabodza, ine ndakhala a... Ine ndinapanga mawonetseredwe abodza, ine—ine ndakhala ndiri mneneri wabodza. Koma ngati Mulungu ananena chomwecho, Mulungu amasunga Mawu Ake. Ndiye ngati Mulungu amasunga Mawu Ake, Mawu amodzi, inu mukhoza kukhala wolimbikira ndiye. Inu mukhoza kugwiritsitsa ku lonjezo lanu ndi kulisunga ilo. Ndi kulondola uko?

²⁵⁴ Tsopano, taonani, kodi ine ndinakuuzani inu kuti ine ndikhoza kukuchiritsani inu? Ayi, bwana. Ine sindikanakhoza kukuuzani inu kuti ine ndingakhoze kukupulumutsani inu mochuluka kuposa momwe inu munapululumutsidwira nthawi imeneyo. Ine ndikukhulupirira kuti inu munapululumutsidwa. Inu simukanakhoza kukweza dzanja lanu popanda Mulungu kukuwuzani inu kuti mutero. Tsopano pali madzi pano, amene inu mungabatizidwe nthawi iliyonse imene inu mukufuna kutero. Ngati mukufuna kuti mubatizidwe ndi anu... mu mpingo wanu womwe, pitirirani nazo, chirichonsecho. Ife tiribe umembala kuno nkomwe, mwaona, ife basi—ife tangokhala kachisi pano. M'busa wathu wabwino pano, M'bale Neville, anali wa Methodisti, ndipo iye ali pano basi... Ndife azipembedzo zosiyanasiyana. Ife... aliyense ndi wolandiridwa. Ife timangokhala ndi osonkhana amene amabwera muno. Ife timalalikira, kupempherera odwala. Ife timakhulupirira kupanga ophunzira kwa Khristu, osati kupanga bungwe chirichonse. Mukuona? Ife sitimakhulupirira mu zimenezo. Ayi, bwana. Tsopano, inu mukufuna bungwe... inu mukufuna bungwe lanu, pitirirani nazo. Ndizo—ndizo zabwino mwangwiro, koma inu musati muzidalira pa zimenezo. Musamadaliwe zimenezo. Ayi, bwana. Inu muzipita kumeneko ku chianjano, koma inu muzidalira mwa Mulungu.

²⁵⁵ Tsopano, tsopano, pano pali chinthu chimodzi. Ngati Khristu akanali moyo... Tsopano, tiyeni titenge Lemba limodzi laling'ono kachiwiri tsopano. Ife tikufuna kuti tikhale otsimikiza tsopano kuti izo zonse ndi zomveka. Chinthu chaching'ono chimene ine ndimati ndinene kanthawi kapitako, Iye anati, "M'badwo woyipa ndi wachigololo udza—udzapeza chizindikiro." Chimenecho chinali chizindikiro cha Yona, chiukitsiro. Ndi kulondola uko? Ndi angati akukhulupirira kuti izo ndi Choonadi? Tsopano ine ndikungofuna kuti ndiwone. Woyipa uyo... Kodi inu mukukhulupirira kuti uno

ndi m'badwo woyipa, wachigololo? Chabwino, kodi chizindikiro cha Yona chidzakhala chiyani? Chikanadzakhala chiukitsiro cha Khristu. Ndi kulondola uko? Chiwukitsiro cha Khristu, chikanadzatsimikizira kwa m'badwo woipa uno umene Khristu akadali moyobe, chimene, Iye waukitsidwa tsopano kwa zaka thuu sauzande, kotero iwo udzakhala umboni wa chiwukitsiro.

²⁵⁶ Chabwino, alipo ambiri a ife Achiprotectanti kudutsa dzikoli samakhulupirira mu chiukitsiro cha thupi. Mazana a mipingo siyimakhulupirira mu zimenezo, kubwerera mwathupi, kapena chirichonse. Mukuona? Ine ndimakhulupirira mu kubadwa kwenikweni, imfa, kuikidwa mmanda, chiukitsiro, Kudza Kwachiwiri, zonse Khristu Yesu. Inde, bwana. Ine ndimakhulupirira kuti Iye ndi Khristu kwathunthu. Yesu yemweyo anatengedwera mmwamba, Yesu yemweyo adzabwerera. Ndipo ine ndimakhulupirira mwa Umunthu wa Mzimu Woyera, Iye ali pano tsopano, Mzimu Wake, Moyo Wake ukuyenda mu Mpingo.

²⁵⁷ Tsopano, ngati izi ziri za Khristu . . . Tsopano ine ndizipanga izi mwaumunthu. Ine ndikuyembekeza kuti inu simutero—inu simuzitenga izo mwa choncho. Ine ndizipanga izi mwaumunthu tsopano, mwa mphatso imene inaperekedwa. Chimene, Ichi, mu Washington Kuwala uku kunapachikidwa, Lawi la Moto limene latsimikiziridwa kwa zaka kuzungulira dziko, ndi zina zotero. Tsopano, ngati Mzimu umenewo uli muno, ndiye Iwo udza . . . Ngati Iwo uli Mzimu wa Khristu, Iwo udzachita ntchito za Khristu. Tsopano, ndiro Lemba. Ndipo Ilo ndi lowona. Ngati Mawu amenewo abwera, ndiye kuti Mawu awa amene ine ndakuzani inu mmawa uno ndi Choonadi. Chifukwa Khristu sangabwere mwa ine monga . . .

²⁵⁸ Ine sindiri—ine sindikupanga—sindikukusekani inu anthu Achikatolika, koma inu mumanena kuti ndi mzimu wa Petro unali mu mpingo wanu kumbuyo uko. Inu mukuganiza kuti Myuda angayike mafano? Inu mukuganiza kuti Myuda angaukane Mzimu Woyera ndi kupanga kachidutswa kakang'ono ka mkate kukakaika pa guwa, kumene mbewa ndi makoswe angatole iwo, ndipo inu nkumapita pamenepo mukunena kuti ameneyo ndi Mulungu? Chavuta ndi chiyani? Inu mukudziwa kuti ameneyo si Mulungu. Mzimu Woyera ndi Mulungu akubwera pansu kuchokera Kumwamba, Mzimu. Inu mumadzilambatitsa nokha pamaso pa mafano, kuyesetsa kuti muwunyengerere a—moyo mu zimenezo. Inu ndinu fano, Mulungu amabweretsa Mzimu Wake mwa inu ndipo ndinu womuimirira Wake wamoyo. Mwaona, Mulungu ali mwa inu, akuliyanjaniitsa dziko kwa Iyemwini.

²⁵⁹ Tsopano ife tiyitanitsa mzere wa pemphero. Kodi inu mukuti munapereka kuti, kuyambira wani mpaka fifite? Tiyeni tiyambire, tiyeni tiyambire pa wani. Chotero mukuti chiyani? Chabwino, ife tikungoyenera kuyitana ochepa pa nthawi,

chifukwa awo...Tiyeni tiwone, tiyeni tingoitana pafupifupi eyiti kapena teni pa nthawi. Ndani ali ndi khadi la pemphero nambala wani? Tsopano musati...Basi, muzingodzuka pamene nambala yanu yatchulidwa, chifukwa ili si bwalo la mjaha tsopano, muno ndi m'tchalitchi. Chabwino. Mukuti chiyani? A—A, nambala wani. Ndani ali nayo iyo? Kodi inu mungabwere cha apa, dona, kapena motsatira apa penapake? Pomwe pano, mudzaima apa pomwe patsogolo pa guwa. A, nambala thuu, ndani ali ndi nambala thuu? Khadi la pemphero nambala thuu. Tsopano, kwezani dzanja lanu mwamsanga kuti ife—ife ti... Chabwino, pitani kumbuyo komwe kwa donayo, ngati inu mungathe. Nambala firii, nambala firii. Chabwino, mlongo, inu simungathe kudzuka, chotero mungogona pamenepo, ndipo ine ndibwera ndidzapemphere nanu pomwe apo. Nambala foro, A, nambala foro, kwezani mmwamba dzanja lanu. A, nambala foro, nambala foro. Kumbuyo komwe, kutali, kumbuyo komwe. Chabwino, mwaona, iwo amangobwera kuno, ndipo aliyense amene akuwafuna iwo, iwo amawasakaniza makadi amenewa ndi kuwapereka iwo kwa anthu monga chonchi, kumene inu mukuwafuna iwo. Ife sitimadziwa. Chabwino, nambala foro, bwerani kuno, dona. Nambala faivi, ndani ali ndi nambala faivi? Khadi la pemphero nambala faivi, kodi inu mungakweze mmwamba dzanja lanu mwamsanga. Tsopano ife sitingatenge nthawi yochuluka tsopano, inu muphonya nthawi yanu. Nambala faivi, nambala sikisi, chabwino, nambala seveni.

²⁶⁰ Tsopano, tiyeni tiwone, asiyeni—asiyeni—asiyeni—asiyeni—asiyeni ena onsewo abwere. Ife tikhoza kuwatenga awa mwanjira iyi. Nambala eyiti, khadi la pemphero nambala eyiti, ndani ali ndi nambala eyiti? Kodi ndinu khadi la pemphero eyiti, dona, inu muli ndi eyiti? Chabwino. Kwezani dzanja lanu kuti ine ndikhoze kukuwonani inu, mwaona, pamene. Nambala naini, ndani ali ndi nambala naini? Chabwino, izo nzabwino, dona. Nambala teni, khadi la pemphero nambala teni, ndani ali ndi nambala teni? Kodi inu mungakweze dzanja lanu, yense yemwe iye... Chabwino. Ine ndikupepesa. Chabwino, bambo uyu cha apa. Chabwino, bwana, bwerani kuno. Nambala leveni, nambala leveni. Chonde kwezani dzanja lanu, nambala leveni.

²⁶¹ Musalandire khadi pokhapokhapo ngati mutaigwiritse iyo ntchito, abwenzi, chifukwa ngati inu—inu—inu—inu—inu... Inu mukuona, ngati inu mungadzuke ndi kutuluka panja, ndipo osagwiritsa ntchito khadi lanu la pemphero, ndiye inu—ndiye inu—ndinu...inu musachite zimenezo. Nambala leveni, nambala thwelovu. Chabwino. Cha apa pomwe, mlongo, bwererani mmbuyo kuzungulira kumbuyoko. Nambala sartini, kuzungulira komwe uko. Nambala fortini, nambala fifitini. Izo nzabwino, ndiyo njira yochitira izo. Nambala sikisitini. Tsopano inu mukuchita zimenezo. Nambala seventini. Mungotenga malo anu kumbuyo uko. Seventini. Tiyeni tiwone ndi angati

ena amene ife tiri nawo tsopano. Mukuti chiyani? Bwerani chozungulira kumbali imeneyo ngati inu mungathe, m'bale, kotero ife tikusokonezeka cha kuno. Nambala seventini, nambala eyitini, naintini, twente, twente. Chabwino. Ine ndikuganiza izo zikungofotokoza izo apo pomwe, kwa—kwa pang'ono chabe. Tiyeni tiwone momwe tifikire mmusi apa mu mzere, ife tiwona. Twente, twente-wani, twente-thuu, twente-firii, twente-foro, twente-faivi. Tsopano tiyeni tiwone za iwo, tiwone ndi angati ali pamenepo tsopano. Nambala twente-faivi. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti tangotsala pafupi kuti tidzadzane kuno, kodi inu simukuganiza chomwecho? Twente-faivi, ine ndikuganiza, twente-faivi. Chabwino, tsopano ife tiri nawo ena twente-faivi akubwera basi mwamsanga pamene ili—gulu ili liti lithe. Ife tiri nawo ena twente-faivi akubwera. Chabwino, twente-faivi.

²⁶² Chabwino, tsopano tiyeni tiwone ndi angati muno amene ali ndi makadi a pemphero. Ndi angati muno amene alibe makadi a pemphero ndipo inu mukufunabe kuti Mulungu akuchizeni inu, kwezani mmwamba manja anu. Khulupirani. Kutu inu muli. . . Inu mulibe makadi a pemphero koma inu mukufuna kuti Mulungu akuchizeni inu, kwezani mmwamba dzanja lanu.

²⁶³ Tsopano, pamene iwo akuwaika iwo pa mzere, ndipatseni ine tcheru chanu tsopano, chifukwa ngati muphonye izi tsopano inu—inu simudziwa choti muchite. Tsopano, ife titenga nthawi yathu, tingotenga nthawi yathu. Tsopano, musakhale pa liwiro. Ine ndiyenera kuti ndikhale chete, inemwini, chifukwa Mzimu Woyera mu zinthu za mtundu uwu sungadzoze mwanjira ya kachitidwe kameneko.

²⁶⁴ Tsopano, ndi angati mchipinda chino, kapena mzere wa pemphero uwu waima apa, amene akudziwa kuti—kuti. . . ine ndikuwadziwa ena a anthu awa. Ine ndikukhulupirira ine ndikutero. Ine ndikudziwa ndikumudziwa dona uyu pomwe pano, dona uyu apa. Iye amabwera kuno ku tchalitchi, sindingakhoze kutchula dzina lake. [Mlongo akuti, "Baker"—Mkonzi]. Baker, uh-huh, ine ndikumudziwa iye. Ine sindiri wotsimikiza, ine sindiri. . . Ine ndikukhulupirira munthu wamtali wamkulu uyu waima pomwe pano, ine ndikukhulupirira ine ndikumudziwa iye. Ine sindikudziwa dzina lake, koma ine ndamuwonapo iye pano.

²⁶⁵ Chabwino, mulimonse, mmodzi aliyense wa inu mu mzere, ndipo aliyense wa inu kunja mwa omvetsera amene akudwala, amene akudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za inu, kwezani dzanja lanu, mukudziwa kuti ine sindikudziwa. Eya. Mukuona? Ayi. Ine sindikudziwa kanthu za inu. Ndine mlendo. Tsopano tiyeni tiwone mzere wa pemphero kachiwiri, kwezani mmwamba dzanja lanu, mukudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za chimene chakuvutani inu tsopano. Chabwino, chabwino, chabwino, pafupifupi handiredi peresenti basi, ine ndikuganiza.

Chabwino, ndipo mwa omvetsera tsopano, tsopano kwezani mmwamba manja anu, inu amene mukudwala ndipo kwezani mmwamba dzanja lanu ndipo muzinenabe kuti ine. . . “Iye sakundidziwa ine kapena kanthu za ine.” Mwaona, alipo anthu ambiri pano. Ine ndimabwera ndi kutuluka, ndipo anthu ena ine ndikuwadziwa ndipo ena ine sindikuwadziwa. Mukuona? Ndipo ine—ine sindikudziwa. Koma iwo amene ine ndikuwadziwa, ine sindingadziwe chimene chinali vuto ndi iwo.

²⁶⁶ Tsopano ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu chinachake. Tsopano ngati. . . Tsopano, taonani, panali mkazi wamng’ono. Anthu amene simukhala mu mzere wa pemphero, mwaona, inu anthu amene simukhala mu mzere wa pemphero. Tsopano, panali mkazi wamng’ono, nthawi ina, iye sanali woti akhala mu mzere wa pemphero nayenso, ndipo iye anali ndi vuto la magari. Koma iye ankakhulupirira kuti ameneyo anali Munthu waumulungu. Tsopano, mvetserani mwatcheru tsopano, musaphonye izi. Iye ankakhulupirira kuti Yesu anali Khristu, ndipo iye anati “Ngati ine ndingakhoze kokha kukhudza mphonje ya chovala Chake.” Tsopano, iye analibe Lemba lirilonse la zimenezo, mwaona, osaposa basi mwina wake monga Eliya anatenga. . . kapena anatenga ndodo yake ndi kudzaigoneka iyo pa mwanayo, kapena chinachake, mwaona, kapena kukhudza mafupa a Eliya iye atafa. Koma iye anakhulupirira kuti ngati atamukhudza Iye angapeze chimene iye anapempha. Iye anazembera pakati pa anthuwo ndipo anakamufikira. Tsopano, ngati aliyense anayamba wakhalapo ku Palestina, iwo amakhala ndi chovala chamkati ndi chovala cha pamwamba, ndipo icho chimalendewera. Ndi chifukwa chake iwo amakhala ndi kutsukana mapazi ndi zinthu, fumbi limakwera pa mapazi awo. Ndipo iye anakhudza mphonje ya chovala Chake. Tsopano, ngati iye atakhudza chikhotho changa, monga *choncho*, ine sindingamverere izo, ndipo icho chikulendewera pafupi ndi ine. Koma iye anakhudza pansu ku mphonje, mmalire, chimene mwina wake anali kutali *chomwecho* ndi mapazi Ake, kapena, thupi Lake. Iye anakhudza mphonje ya chovala Chake, ndipo anabwerera ndi kukakhala pansu, kapena chirichonse chimene iye anachita. Yesu anaima.

²⁶⁷ Ndipo, kumbukirani, unyinji wonse unali ndi mikono yawo. . . “Moni, Rabbi!” “Wokondwa kukuwonani Inu!” “Kodi Ndinu Mneneri?” “Ife—ndife okondwa kukuwonani Inu.” “Oh, Iwe wachinyengo!” “Ndiwe Munthu wabwino!” Oh, basi kufotokozero kosiyanana.

²⁶⁸ Tsopano mvetserani mwatcheru kwenikweni. Ndiye mkazi wamng’ono uyu, iye anakhudza chovala Chake, ndipo anabwerera mmbuyo chifukwa iye anali atakhutitsidwa kuti iye wamukhudza Mulungu. Yesu anaima, anati, “Ndani wandikhudza Ine?”

269 Petro anamudzudzula Iye, anati, “Onse akukukhudzani Inu. Chifukwa chiyani Inu mukunena chinthu ngati chimenecho?”

270 Iye anati, “Koma Ine ndazindikira kuti Ine ndafooka, ukoma wachoka mwa Ine.” Iye anayang’ana pozungulira ponse pa omvetsera mpaka Iye anamupeza mkazi wamng’ono ameneyo, ndipo Iye anamuza iye za vuto lake la magazi, ndipo ilo linali litatha. Ndi kulondola uko? Tsopano, tsopano, tsopano gwiritsitsani zimenezo. Tsopano, inu munene “ameni” kwa izo, izo zikutanthauza “zikhale chomwecho.” Tsopano, zindikirani tsopano, kodi Baibulo limanena, kwa inu Akhristu owerenga, kuti Yesu Khristu tsopano ndi Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumvera kwa zifoko zathu? Ndi angati akudziwa kuti Baibulo linanena zimenezo? Chabwino, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, kodi Iye sangachite mwanjira yomweyo imene Iye anachitira nthawi imeneyo? Chabwino, ndiye, ngati inu mwakhala kunja uko mukanamukhudza Iye kuntunda uko, ndipo ngati ine ndiri womuimirira Wake, Liwu Lake pano tsopano, kodi Iye sanganene chinthu chomwecho chimene Iye anachita nthawi imeneyo? Kodi zimenezo sizikumveka Mwamalemba? Kodi izo si zoono? Mukuona? Inu mudziwa bwanji kuti inu mwamukhudza Iye ngati Iye sachita chimodzimodzi? Mukuona? “Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita.”

271 Chabwino, tsopano inu opanda makadi a pemphero, inu muzingopemphera ndi kumati, “Ambuye Yesu, ine sindinafike kuno mu nthawi yoti ndipeze khadi la pemphero, koma ine—ine ndikupemphera kwa Inu, ndipo ine ndikukhulupirira zimene munthu uyu ananena ndi Choonadi. Chotero ine nditero... Kodi Inu chonde mungandilole ndikhudze chovala Chanu, Ambuye Yesu? Ndinu Wansembe Wamkulu wanga. Ine sindikuyang’ana kwa bambo wamng’ono wa mutu wadazi uja waima pamwamba apo pa nsanja. Ine ndikuyang’ana kwa Inu, ndipo ine ndikukukhudzani Inu, ndipo ine ndikukhulupirira kuti Inu mundichiritsa ine. Chotero, ine ndikukukhudzani Inu, Inu muyankhule ndi M’bale Branham ndipo muchite chinthu chomwecho pano monga Inu munachitira kwa mkazi uja. Ndipo ine ndikukhulupirira Inu ndi mtima wanga wonse.” Kodi inu muchita zimenezo? Ndi angati amene achite zimenezo, kwezani dzanja lanu, ndikuti, “Ine—ine ndichita zimenezo.” Chabwino, inu mungopemphera. Tsopano pano pali malo oti muyikepo chikhulupiriro chanu kuti chigwire ntchito. Inu mukukhulupirira zimenezo, inu musakaikire zimenezo. Inu mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse. Ameni.

272 Ndiyeno inu mu mzere wa pemphero, tsopano ndi... Kodi munthu woyamba ndi ndani? Ingobwerani pomwe apa miniti. Tsopano, ingoimani apo pomwe. Ndizo—ndizo zabwino mokwanira, mwaona, imirirani apo pomwe. Ine ndikukhulupirira, kanthawi kapitako, inu munakweza dzanja

lanu, ine sindinakudziweni inu. Uko nkulondola. Ndife alendo kwa wina ndi mzake. Chabwino.

273 Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwafunse omvetsera awa chinachake. Manja anga ali mmwamba pamaso pa Mulungu, ndipo iye anakweza dzanja lake kuti ife sitikudziwana wina ndi mzake. Tsopano, kodi ichi si chithunzi cha Baibulo cha Yohane Woyera 4, pamene Yesu anakumana ndi mkazi pa chitsime? Mwamuna ndi mkazi anakumana nthawi yoyamba. Ndipo kodi Yesu anachita chiyani? Iye anapita kukayankhulana naye. Kodi Iye anali kuchita chiyani? Tsopano, Iye anati, “Atate. . .”

274 Iye ankasowa kuti apite ku Yerusalemu, kapena uko ku Samaria. Tsopano, onani, a—Ayuda anali atawona chizindikiro chimenecho, pakuti Iye anali Mneneri ndipo Iye anasonyeza chizindikiro cha mneneri. Ndipo pali—pali mitundu itatu yokha ya anthu, ndiyo anthu a Hamu, Shemu, ndi anthu a Yafeti. Tsopano, Ayuda anali atawona chizindikiro chawo, chifukwa iwo anali akuyembekezera Mesiya. Iwo anachiwona icho. Tsopano Asamaria ayenera kuziwona izo, chifukwa iwo anali kuyembekezera Mesiya.

275 Osati Amitundu, palibe nthawi imodzi yomwe Iye anachita konse izo pa Wamitundu, koma Iye analosera, “Mmasiku otsiriza,” monga Iye anachitira, “monga zinali mmasiku a Nowa ndi mmasiku a Loti,” pamene Mngelo uja anabwera nayankhulana ndi Loti, anamuza Sarah zimene iye anachita mu hema kumbuyo Kwake. Yesu anati izo zidzabwereza kachiwiri pa tsiku lotsiriza. Ndi owerenga Baibulo angati akudziwa zimenezo? Mwaona, kulondola. Mukuona? Tsopano ife tiri mmasiku otsiriza, ndi nthawi ya Amitundu. Ngati Iye. . . Mwaona, ine ndinanena poyambirira pa ulaliki wanga, ngati Mulungu achita chirichonse, podzizindikiritsa Yekha nthawi ina, Iye ayenera kukhalabe mwanjira imeneyo.

276 Chotero kodi—Nataniele anadziwa bwanji kuti Iye anali Mwana wa Mulungu? Chifukwa chakuti Iye anamuza iye kumene iye anali, chinachake chokhudza iye.

277 Kodi mkazi uyu anadziwa bwanji? Taonani, tiyeni titenge zokambirana zake, tiwone kuchuluka kwake—kuchuluka kwa momwe iye ankadziwira za izo kuposa alaliki onse awo kumusi uko. Iye anapita kumeneko. Iye mwina anali mkazi wokongola. Iye anali woti akatenge chidebe cha madzi. Iye anakokera mmwamba chidebe cha madzicho. Iye anali Myuda, iye anali a—Msamariya. Ndipo kotero, anakoka chidebe cha madzicho, ndipo chapafupi ndi pamalo aang’onowo apo pamene chitsime chiri. Akadali kumeneko ku Sukari. Chotero ndiye Iye anali atakhala pamenepo monga choncho, Iye anati, “Mkazi, ndibweretsere Ine akumwa.” Iye anatembenuka. Tsopano, iye anali mkazi wa mbiri yoipa, inu mukudziwa, iye anali atakwatiwa nthawi zochuluka kwambiri. Ndipo anati, “Ndibweretsere Ine akumwa.” Iye. . .

278 Iye anati, “Si mwambo wake kuti inu Ayuda mumufunse mkazi wa Chisamariya chinachake monga chomwecho.”

279 Kukambiranako, mwaona. Atate anali atamutumiza Iye kumeneko. Tsopano kumbukirani, Iye sanachite kanthu mpaka Atate atamuwonetsera Iye. Mukuona? Chotero tsopano Iye anakhala pamenepo, kotero kodi Iye anali akuchita chiyani? Iye anali akuyesetsa kuti apeze chomwe vuto lake linali, kuchitira kuti iye akhoze kutengera uthenga kwa anthu amenewo. Anati. . . Ankafuna kuti apeze vuto lake, inu mukudziwa. Anati, “Ndibweretsere Ine akumwa.”

Iye anati, “Si mwambo wake.”

280 Iye anati, “Koma ngati iwe ukanadziwa Yemwe iwe ukuyankhula naye, iwe ukanandipempha Ine akumwa.”

281 Iye anati, “Chabwino, chitsimechi ndi chakuya, Inu mulibe kanthu kotu mutungire. Inu mungatunge bwanji madzi kuchokera apa?”

282 Ndipo anapitirira kuyankhula, kukambiranako kunabwera, za kupembedza ku Yerusalemu. Kodi Iye anali kuchita chiyani? Iye anali kuyesetsa kuti awupeze mzimu wake, kuti awone chimene chinali cholakwika. Iye anawupeza iwo. Inu mukudziwa chimene iwo unali? Iye anali ndi amuna faivi. Ndipo Iye anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo mubwere kuno.”

Iye anati, “Ine ndiribe mwamuna aliyense.”

283 Anati, “Iwe wanena bwino, iwe wanena bwino, pakuti iwe wakhala nawo faivi ndipo mmodzi yemwe iwe ukukhala naye tsopano si mwamuna wako.”

284 Tsopano penyani. Tsopano, iye sananene kuti, “Iye ndi wambwebwe,” monga alaliki aja anachitira. Iye sanati, “Iye ndi Bezebule.” Iye anati, “Bwana,” mvetserani, “Ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri. Ife tikudziwa pamene Mesiya adzabwera Iye adzatiuza ife zinthu izi.” Chimenecho chinali chizindikiro cha Mesiya.

Yesu anati, “Ine ndine Iye amene akuyankhula ndi iwe.”

285 Iye anathamangira mu mzinda, ndipo anati, “Bwerani ndipo mudzamuwone Munthu yemwe wandiuza ine zinthu zimene ine ndachita. Kodi uyu si Mesiya yemwe?”

286 Chabwino, ngati chimenecho chinali chizindikiro cha Mesiya kwa Ayuda, kwa Asamaria, kodi icho sichingakhale chizindikiro cha Mesiya kwa Amitundu? Kodi sakanadzatero Mesiya ndiye, ngati Iye anauka kwa akufa ndipo akukhala mu Mpingo Wake, akudziwonetsera Yekha kupyoleramo, kodi Iye sangachite ntchito zomwezo pamene Iye analonjeza kuti Iye akanadzachita izo?

287 Tsopano ine nditaima apa ndikuyankhula ndi inu, ine sindikukudziwani inu, sindinayambe ndakuwonanipo inu mmoyo wanga. Mukuona? Koma ngati Ambuye Mulungu ati andiuze ine chinachake chimene inu mwadzera pano, inu mudziwa ngati izo ziri zoon kapena ayi. Mwaona, kundiuza ine chinachake chimene inu mwachita, chinachake chimene inu simumayenera kuti muchite. Ngati Iye angakhoze kukuuzani inu zomwe inu mwachita mmbuyomu, ndithudi Iye angadziwe zomwe tsogolo linali. Ndi kulondola uko, ngati Iye angakhoze kukuza inu zimenezo? Ndithudi. Ndipo ngati Iye ati andiuze ine chomwe inu mwadzera pano, kodi inu mungamukhulupirire Iye kuti ndi Mwana wa Mulungu, mukhulupirira zimenezo? Ndi angati mwa omvetsera ati akhulupirire zimenezo? Ndipo ine ndi mkazi yu pano ndi manja athu mmwamba, ife—ife sitiri. . . ife, mwaona, ndife mlendo. Ine ndiribe lingaliro, inu mukudziwa ine sindikutero. Inu mumaima pamenepo, mlendo basi kwa ine. Koma ngati Ambuye Mulungu. . . ine ndikuyankhula ndi inu kuti ndiwuyambitse Mzimu uyambe kuwadoza anthu, inu mukuona, ndiyeno izo zimangotswa modutsa. Ndipo ine—ine ndikungoyang'ana pa inu kuti ndiwone chimene Iye ati andiuze ine, chifukwa ine sindikudziwa kanthu za izo. Koma ngati Iye ati akuuzeni inu chinachake, ndiye inu mudziwa ngati icho chiri choonadi kapena ayi, sichoncho inu? Kodi aliyense angakhulupirire, ngati Iye angachite zimenezo?

288 Atate athu Akumwamba, ine sindingakhoze kuchita zinanso tsopano. Izo ziri mpaka ku nthawi ino, izo zitengera Inu kuchokera pano mpakana, Ambuye. Ine ndawabweretsa anthu ku Mawu Anu. Ndizo zonse zimene ine ndikuzidziwa. Inu munalonjeza zinthu izi. Ndipo izo zingatenge masabata ndi masabata, ife tikhoza kukhalabe pa zimenezo, kunena za malonjezo Anu a zinthu zomwezi izi za masiku otsiriza. Monga ife takhala nthawi zonsezi kuzungulira dziko, Inu simunayambe mwatilepherapo ife, Ambuye. Tsopano apa paima omvetsera a anthu. Ine ndikudziwa kuti amodzi a masomphenya awa amatifooketsa ife. Ine ndikuzindikira zimenezo. Ukoma unatuluka kuchokera mwa Inu, Mwana wa Mulungu, Mwana wa Mulungu wosaipitsidwa. Zidzakhala mochuluka bwanji kwa ine, wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo Chanu?

289 Ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mulole izo zichitike tsopano, kuti Uthenga uwu mmawa uno usapite wopanda chipatso, koma owatembenuza aang'ono awa, mwina mwake twente kapena sarte a iwo amene angokwezera manja awo kwa Inu, kuti iwo akhutitsidwe, Ambuye, kuti Mulungu wawo wauka kwa akufa ndipo Iye ali moyo kwanthawizonse, kudzipangitsa Yekha kudziwika, Mulungu yemweyo amene amadziwa chinsinsi cha mtima, ndipo analonjeza mmasiku otsiriza izo zikanati zidzachitike kachiwiri. Ndi ife apa, mapeto a nthawi. Ndipo Amitundu akhala nazo zaka thuu sauzande, chimodzimodzi

monga momwe Ayuda anachitira, kuti aphunzire za Mulungu, ndipo tsopano iwo akutenga chizindikiro chomwecho ndi kuchikana Icho chimodzimidzi basi monga Ayuda anachitira. Ayuda anamukana Mesiya wawo, chifukwa iwo anali nazo zonsezo zitapanga chipembedzo. Ndipo chomwechonso iwo achita zimenezo lero, Ambuye, achita chinthu chomwecho. Koma ife sitingachongere zimenezo. Ife tikungochitira umboni basi, Ambuye. Chimodzimidzi monga nkhoa, iyo siyimapukusa chirichonse, iyo imabala ubweya chifukwa iyo ndi nkhoa. Ndipo, Ambuye Mulungu, tiloleni ife tibale Mzimu wa Mulungu, chifukwa ndife Akhristu. Ife timakhulupirira mwa Inu. Ife timakhulupirira mwa Mwana wa Mulungu. Tsopano, Ambuye, ndine wosayenera, koma kutenga...Ndani ali woyenera? Ndani ali woyenera, Ambuye? Palibe mmodzi wa ife. Ife tonse tinabadwa mu tchimo, tinawumbidwa mu kusaeruzika, tinabwera mdziko tikuyankhula mabodza. Tikhulukukireni ife zathu—zonyansa zathu, Ambuye. Ndipo tsopano mutigwiritse ife ntchito mu tsiku lotsiriza lino limene Inu mukuchita nawo mtundu wa anthu. Mu Dzina la Yesu. Amen.

²⁹⁰ Tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikuwutenga mzimu uliwonse panso pano, mkati muno, panso pa ulamuliro wanga. Mukuona? Tsopano mukhale molemekeza. Posakudziwani inu, osadziwa kanthu za inu. Iyo ndi mphatso. Basi momwe inu mumadzikokerera nokha, pamaso pa Mulungu, kudzikhuthula nokha. Kumulola Iye kuti achite kuyang'ana. Ine sindikudziwa, koma ine ndikudziwa kuti Iye ali pano. Ine ndikudziwa Iye wayima pano. Inde, amayi, vuto lanu ndi ili. Inu mukufuna pemphero chifukwa cha khansa. Khansa imeneyo ili pa nkhope yanu; iyo siikuwoneka, ngati, koma iyo ili mmwamba kuzungulira diso lanu. Uko nkulondola, kwezani dzanja lanu.

²⁹¹ Ine ndinazimverera zimenezo zikubwera kumene kuchokera kunja uko mwa omvetsera, inu munati, “Iye wapeka zimenezo kapena anaziyang'ana izo pa nkhope.” Ine sindinachite zimenezo. Imani njii. Mundilole ine. . . Satana, iwe ukulakwitsa. Imani njii, mlongo. Inu mumuyambitsa iye, ngati iye ayamba, ndiye iye adzapita paliponsepo. Ife tikumudzudzula mdierekezi ameneyo, mu Dzina la Yesu Khristu, ndi kumuchititsa iye manyazi.

²⁹² Inu muli ndi vuto loposa limenelo ndi inu. Inu muli ndi vuto la mtima, nanunso. Zosokonezeka, basi zonsezo chikhulidwe chamanjenje, zakhala ziri mwanjira imeneyo kwa zaka. Uko nkulondola ndendende, mumatopa, mumamverera kutopa ndi chirichonse. Ndizo...Ngati izo ziri zoono, kwezani mmwamba dzanja lanu. Tsopano inu mwachiritsidwa. Chikhulupiriro chanu chakupulumutsani inu. Inu mukhoza kupita kwanu tsopano ndi kukakhala bwino. Izo zatha. Ingopitani, mukukhulupirira, zonse zimene inu mukuyenera kuchita. Kumuthokoza Mulungu.

293 Inu mukukhulupirira? Ingoimani apo pomwe, dona, muyang'ane mbali iyi. Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? Kodi Mulungu angachiritse vuto la mtima? [Mlongo akuti, "Inde, Iye akhoza."—Mkonzi]. Chabwino, Iye wachiritsa wanu, ndiye, ngati inu muti mukhulupirire. Pitani, mukhulupirire.

294 Inu mukukhulupirira kuti Iye wachiritsa khansa? Ndiye bwererani ku mpando wanu, mukuti, "Zikomo Inu, Ambuye Yesu."

295 Bwanji ngati ine ndikanati ndisanene mawu amodzi kwa inu koma basi. . . Kodi inu mungakhulupirire ngati ine nditatu inu munachiritsidwa pamene inu munafika apo mu mzere? Kodi inu mungatenge mawu anga pa zimenezo? Inu muli, ndipo palibe chifukwa chokuuzirani inu izi, inu munachiritsidwa kale. Ine sindinamukhudze munthuyo.

296 Inu simutero, inu simusowa kuti mukhale ndi oparesoni ngati inu muti mumukhulupirire Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo ndi mtima wanu wonse? Chotupacho chapita. Pitani kwanu ndipo mukakhala bwino.

297 Tayang'anani mbali iyi, mlongo. Inu mukundikhulupirira ine kukhala wantchito Wake? Mphindi yokha. Tsopano, pali mwamuna yemwe akungowonekerawonekera pamaso panga pano, iye ali ndi chinthu chomwecho chimene mkazi uyu ali nacho, penapake mwa omvetsera. Ndipo taonani Kuwala kuja pa chithunzi, Kumene kwaima pomwe pano. Kodi inu simukuziwona izo? Ndi bambo uyu wakhala pomwe apa. Inu muli ndi khadi la pemphero, bwana? Mnyamata, ine ndikukhulupirira ndinu M'bale Hupp, sichoncho inu? Ine ndangokuzindikirani inu. Ine sindiri—ine sindikudziwa chimene chakuvutani inu, M'bale Hupp. Inu mukudziwa ine sindikutero. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine lomwe liri vuto lanu? Inu muli ndi vuto. Inu munakhala apo, mukukhulupirira. Inu muyenera kukhulupirira pa chifukwa cha mwana wanu wamkazi kuno posachedwapa. Inu mukukhulupirira, sichoncho inu? Mkazi uyu ali ndi nyamakazi; inu mukutero, nanunso. Ngati uko nkulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse ndipo inu nonse mukhoza kuchiritsidwa. Mulungu akudalitseni inu. Satana amaganiza kuti wathana naye bambo ameneyo, iye waziphonya izo. Khalani ndi chikhulupiriro tsopano. Musakaikire. Tsopano, bambo uyu apa, nthawizonse. . . M'bale Hupp, inu mulibe khadi la pemphero, sichoncho inu, M'bale Hupp? Eya, inu mwangokhala pamenepo, mukukhulupirira. Inu mupenye zimene zichitike kwa inu. Mungokhulupirira tsopano ndi mtima wanu wonse.

298 Aliyense mu pemphero. Inu mukukhulupirira tsopano? Tsopano, inu mukuzindikira zinthu izi zimangondifooketsa ine

kwambiri ine basi . . .

²⁹⁹ Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu? Ngati ine nditakuuzani inu kuti mukhala bwino, kodi inu—kodi inu mungatenge mawu anga pa izo ndi kuzikhulupirira izo? Ndiye kazipitani ndipo Yesu Khristu wakuchizani inu. Mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse.

³⁰⁰ Kodi inu mukuganiza kuti Mulungu akhoza kuchiritsa manjenje ndi kukupangani inu kukhala bwino? Pitani, mukhulupirire zimenezo. Ine ndikukhulupirira ine . . . Ine sindiri wotsimikiza, ine ndimaganiza kuti ndikumudziwa mkazi ameneyo. Ine sindinali wotsimikiza. Masomphenya anatulukira pa iye koma ine—ine ndinawaimitsa iwo, ndinangoyang'ana mmbuyo mbali inayo; chifukwa ine ndikukhulupirira ine—ine ndimamudziwa mkaziyo, koma ine—ine sindinali wotsimikiza.

³⁰¹ Tsopano mukhale molemekeza, aliyense. Kodi inu mukukhulupirira? Mwaona, ine ndiri waukulu, mzere wautali wa pemphero apa, ine sindikufuna . . . Ingoimirirani. Ndipo, pakali pano, ine ndalalikira kwa inu kwa pafupifupi maora awiri kapena atatu, koma pakali pano ndine wofooka kuwirikiza kawiri kuposa momwe ine ndinaliri ndi kulalikira konse. Mwaona, zikungowononga moyo wanga. Koma, awa, ife tikhoza kumapitirira kuyankhula ndi anthu, izo zingakhale zabwino bwino, izo sizimapanga kusiyana kulikonse. Iwe ukhoza kuimirira, nkumayankhula ndi anthuwo nthawi yayitali momwe iwe ukufunira, kwenikweni ngati zikuchitikabe, koma ndaimikira kuti ine ndikhoze kupulumutsa mphamvu zanga pang'ono pokha kwa ena omwe akubwera mu mzere. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ndi angati anayamba aziwonapo izo pamene nthawi zambiri ine ndimaima ndi kuyankhula ndi anthu, Izo zimawauza iwo zonse za iwo, ndi za omwe iwo ali ndi kumene iwo akuchokerako? Mai, inu mwakhala muli mu misonkhano ndipo munaziwonapo izo, inu mukuzidziwa.

³⁰² Ichi—chotsatira ichi, ndinu wotsatira? Chabwino, bwana, inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Chabwino, zabwino. Ndife okhulupirira, kukhulupirira ndi mtima wathu wonse. Ndipo posakudziwani inu, Ambuye Yesu akhoza kundiuza ine chinachake cholakwika ndi inu, inu mungadziwe ngati izo zinali zolondola kapena ayi, sichoncho inu, bwana? Inde, bwana. Iyi pokhala yathu . . . Ine ndikuganiza ndife alendo kwa wina ndi mzake. Ine sindikuikumbukira nkhope yanu. Ndife atumiki limodzi, ndipo ndife . . . koma ife sitikudziwana wina ndi mzake mwaumunthu basi monga abwenzi. Chabwino, bwana. Ndiye inu muyang'ane mbali iyi, bwana, ndipo mundikhulupirire ine kuti ndine wantchito wa Khristu ndi mtima wanu wonse. Chabwino, bwana. Munthu uyu akuvutika ndi nthenda ya thumbo. Izo ziri mu thumbo lake. Ndi vutonso la mtima lomwe inu muli nalo. Ndinu mtumiki, izo nzoona, ndinu wa United Brethren Church. Inu mumachokera ku Ramsey,

Indiana. Dzina lanu ndinu Bambo Beanblossom. M'busa Beanblossom, izo ndi zoonu. Ndi kulondola uko, kwezani dzanja lanu. Ndiye pitani kwanu ndipo mukakhale bwino, bwana. Yesu Khristu wakuchizani inu. Inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

³⁰³ Nyamakazi si ntchito kwa Mulungu. Inu mukukhulupirira kuti Iye akhoza kukupangani inu kukhala bwino? Inu mukukhulupirira kuti Iye akuchizani inu? Pitani ndipo mukamukhulupirire Iye ndi mtima wanu wonse ndipo inu mukhoza kukhala nazo zonse...mungokhulupirira ndi zonse...

³⁰⁴ M'bale, ine ndikukudziwani inu, ndikudziwa chikhalidwe chanu. Inu mukukhulupirira pakali pano, pamene ine ndiri pansu pa kudzodza kwa Mzimu Woyera, kuti Mulungu akuchizani inu ndipo akupangani inu kukhala bwino? Pitani ndipo mukakhulupirire izo, M'bale Collins, ndipo mukakhale bwino. Chabwino.

³⁰⁵ Ine—ine...zimawoneka ngati ine ndinakuwonani inu, koma ine sindiri wotsimikiza. Koma ngati Mulungu ati andiuze ine lomwe liri vuto lanu, kodi inu mundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake, kapena Wake—wantchito Wake? Inu mukukhulupirira zimenezo? Chabwino. Inu mukuvutika ndi chikhalidwe cha manjenje. Ndi chimene inu mukufuna pemphero. Ndi kulondola uko? Kwezani mmwamba dzanja lanu ngati izo ziri zoonu. Pitani kwanu, mukakhale bwino. Mukhulupirire izo. Muthane nazo izo tsopano. Khalani ndi chikhulupiriro chaching'ono icho chimene kwenikweni chimapangitsa izo kukhala bwino.

³⁰⁶ Inu mukukhulupirira kuti Khristu akupangani inu kukhala bwino pakali pano pamene inu mukuima pamenepo? Mukhulupirire izo, ndipo mupite kwanu ndi kumati, "Yesu Khristu wandichiritsa ine pakali pano." Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Inu muyenera kukhulupirira, kuti mukhale moyo. Inu mukudziwa zimenezo, sichoncho inu, mlongo? Ngati inu simutero, inu muyenera kufa. Inu mukudziwa zimenezo. Koma Iye amachiza mitundu yonse ya matenda, khansa, china chirichonse, ndipo amakupangani inu kukhala bwino. Inu mukukhulupirira zimenezo ndi mtima wanu wonse? Ndiye kazipitani ndipo mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, ndipo mukakhale bwino, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.

³⁰⁷ Chabwino, m'bale, inu mukudziwa ine ndikukudziwani inu, ndipo kotero ine ndikungoyesera kuti ndigwire, chonchobe. Koma kodi inu mukukhulupirira kuti Yesu Khristu akuchizani inu pakali pano pamene inu muli pansu pa kudzoza Kwauzimu kwa Mzimu Woyera? Pitani ndipo mukakhulupirire zimenezo ndi mtima wanu wonse.

308 Tsopano chiyani? Chabwino. Mphindi chabe tsopano. Kuchokera pati pamene ine ndinaimira, ndinaimira pati kanthawi kapitako? Twente-faivi, twente-sikisi, twente-seveni, twente-eyiti, twente-naini, sarte, pitani uko ndipo mukalowe mu mzere. Sarte, sarte-wani, sarte-thuu, sarte-firii, sarte-foro, sarte-faivi, sarte-sikisi, sarte-seveni, kupitirira mpaka fifite, zifoletseni pomwe apo tsopano, iwo amene muli ndi makadi anu a pemphero, chotero inu muwapereke iwo kwa wothandizira kapena abale pamene iwo akudutsa.

309 Tsopano tiyeni tingotenga nthawi ya mphindi kuti tipume, miniti yokha. Kodi inu mukukhulupirira? Zinthu zonse ndi zotheka, kungokhulupirira.

310 M'bale ndi Mlongo Spencer, ine ndakudziwani inu kuyambira ndiri mwana wamng'ono. Ine ndikudziwa chimene vuto lanu liri, ndi kudziwa chimene inu mwaimira pamenepo. Inu mukukhulupirira kuti Yesu Khristu akuchizani inu, mutaima pamenepo? O Mulungu wa Kumwamba, mupereke madalitso Anu pa banja lachikulire ili, kuwatumiza iwo kuti akakhale bwino, Atate. Patali mu zaka apa, komabe akukutumikirani Inu. Ine ndikuwadalitsa iwo mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Amen. Bwererani kwanu. . . Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Iye atenga eyite-firii, inu muli ndi zaka zambiri zimene zikubwera, mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse ndipo Mulungu akhala ndi inu. Ndipo inu, nanunso, M'bale Jess. Mulungu akudalitseni inu apa.

311 Inu mukukhulupirira tsopano ndi mtima wanu wonse? Dikirani, ine ndikukhulupirira ine ndamuphonya mlongo wamng'ono uyu kumusi kuno. Chabwino. Ife tiri ndi machira awiri, ife tiyenera kuti tifike kwa iwo miniti yokha. Inu simukusamala kudikirira miniti yokha, mlongo apo, kapena aliyense yemwe munthu winayo ali?

312 Tsopano mukhale molemekeza kwenikweni ndipo muyime chete, aliyense akhale molemekeza. Mwaona, inu muyenera mukhale kwenikweni, molemekeza kwenikweni. Tsopano tiyeni ife tipume mphindi yokha, mwaona, kuchokera ku masomphenya, mphindi chabe. Ndipo tikhale molemekeza kwenikweni. Tsopano aliyense ayang'ane mbali iyi, ndipo tiyeni tiyimbe mwakachetechete, *Kungo Khulupirira*, tsopano. Tonse a ife limodzi tsopano. (Ndiroleni ine.)

Kungo khulupirira, kungo khulupirira,
Zinthu zonse ndi zotheka, kungo khulupirira;
Kungo khulupirira, kungo khulupirira,
Zinthu zonse ndi zotheka, kungo khulupirira.

313 Tsopano, iye anandifunsa ine kuti ndipite ndikawapempherere iwo tsopano, koma ine ndikungokhala ngati ndamasuka pang'ono pokha tsopano. Mundirole ine ndiyambe mzere kachiwiri, mu miniti chabe ine ndiyimikira.

Tsopano, ali kuti anthu amene ali oti apemphereredwe, dona uyo apo mu mpando? Chabwino, mphindi chabe, ine ndi—ine nditenga. . . Ine ndibwera kwa iye, mwaona, miniti yokha. Chabwino, mphindi chabe. Tsopano, aliyense molemekeza kwenikweni. Ine ndikutsimikiza inu muli—inu mukuzindikira chimene ine ndiri panso pano. Mukuona? Osati kuno kokha, koma, mmaiko akunja, nthawizina masauzande kuchulukitsa masauzande.

³¹⁴ Ine ndinamva pang’ono, ndinamverera kukanizidwa pang’ono kanthawi kapitako, za dzina la winawake linaitanidwa. Kodi inu simukuzindikira kuti Yesu akudziwa dzina lanu? Kodi inu simunawone zimenezo? Ayenera kukhala alendo muno, iwo sanaziwone izo. Bwanji, mai, nthawizina pano pa nsanja Iye amawauza anthu machimo awo onse, ndipo amawakumba iwo. Inu mukudziwa zimenezo. Aliyense. . . Kodi Yesu sanamuuze Petro, “Dzina lako ndi Simoni. Dzina la abambo ako linali a Yonasi. Mwana wa a Yonasi”? Mukuona? Kungosonyeza kuti Iye ali pano. Tsopano, aliyense akudziwa, aliyense pano ali woti anene kuti pali mtundu wina wa Mzimu umene ukuchita zimenezo. Tsopano, inu mukhoza kunena kuti, “Ndi Bezebule,” kapena inu mukhoza kunena kuti, “Khristu.” Mulungu adzaweruzwa chirichonse chimene icho chiri. Mukuona? Ine ndikukuuzani inu kuti ndiro lonjezo la Baibulo, Baibulo Loyera la Mulungu apa limapereka lonjezo limenelo.

³¹⁵ Tsopano, tsopano mukhale molemekeza kwenikweni miniti. Tsopano, mphindi yokha. Kodi uyu ndi munthu wotsatira? Chabwino, muyendere mbali iyi, bwana. Sindikumudziwa munthuyo. Mulungu akumudziwa iye. Koma, bwana, ngati Mulungu ati anene kwa ine chimene inu mwadzera pano, chabwino, izo zingakupangeni inu kukhulupirira. Sichoncho izo? Izo ndithudi zingatero. Ndi angati ena kunja uko omwe angati akhulupirire? Pano pali anthu awiri akukumana, mwamunayo ndi wamng’ono kuposa ine. Mulungu wamudyetsa iye moyo wake wonse. Iye waima pamenepo ndi maso ake otsekedwa. Koma ngati Mulungu ati awulule kwa ine chimene munthuyo wadzera pano, kapena chinachake chokhudza izo, izo ziyenera kumupanga aliyense wa inu kukhulupirira ndi mtima wanu wonse. Kodi inu simukuganiza chomwecho?

³¹⁶ Apa, mphindi chabe, kumbuyo komwe kuno, wakhala mu mzere kumbuyo komwe kuno, ndi mwamuna, akupemphera. Iye ali ndi chinthu chosamvetseka kwambiri. Ine ndikuwona kuthwanima. Eya, iye wakanthidwa ndi mphezi. Eya. Khalani ndi chikhulupiriro, m’bale wanga. Ndine mlendo kwa inu, bwana. Ngati uko nkulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu, ife sitikudziwana wina ndi mzake. Mulungu akukudziwani inu. Mukhale ndi chikhulupiriro tsopano.

³¹⁷ Tsopano inu mukuti, “Kodi inu mukuchita chiyani, M’bale Branham?” Ine ndikuyang’ana Kuwala kumeneko.

Iko kukuyenda.

³¹⁸ Vuto la chikhodzodzo, wakhala pamenepo akupempherera... ali ndi vuto la chikhodzodzo, mwamuna akuyang'ana pa ine. Ndife alendo kwa wina ndi mzake, sichoncho ife? Ndiuzeni ine chimene munthu ameneyo anakhudza. Vuto lanu la chikhodzodzo latha, bwana. Kodi iye anakhudza chiyani? Iye ali mapazi sarte kuchokera kwa ine. Iye wamukhudza Wansembe Wamkulu yemwe angakhoze kukhudzidwa ndi kumverera.

³¹⁹ Bambo uyo wakhala pafupi ndi inu, iye akupemphera, nayenso. Izi ndi zomwe iye akupemphera, “Ambuye, mulole ndikhale ine motsatira.” Iye ananena izo pakali pano. Uko nkulondola. Ine ndinadziwa bwanji zimene inu mukupempherera? Iye amene amayankha pemphero. Mwela uwo umene inu mukupempherera, ndicho chimene inu muli nacho, mwela. Ngati uko nkulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino, ngati inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, chinthucho chichira.

³²⁰ Ine ndikutsutsa chikhulupiro chanu. Mu Dzina la Yesu Khristu, inu mukhulupirire! Oh, mai, ndi kumverera kotani! Iye ali pano. Inde. Tsopano mulole izo zichitike. Tsopano inu mumuwona Yemwe ali Bwana. Iye ndi Bwana. Mulole wachikunjayo anene chinachake tsopano, wosakhulupirira. Ambuye Yesu Khristu, kuti atsimikizire kwa inu kuti nthawi yotsiriza ili pano, umenewo ndi Mzimu Wake pa ine. Ndi Iyeyo. Si ineyo, ine sindikukudziwani inu. Ndi Iyeyo. Inu mungokhulupirira ndi mtima wanu wonse.

³²¹ Bambo uyu, ine ndikukhulupirira amene anali wotsatira, bambo uyu apa. Bwana, ndine—ine ndikungoyenera kuti ndipenye momwe Izo zikupitira. Ine sindikukudziwani inu. Ngati Mulungu ati awulule kwa ine chimene inu mwadzera pano, kodi inu mungandikhulupirire ine kuti ndine mneneri Wake, wantchito Wake? Ndinu munthu wochirimika. Inu mwaima pano chifukwa cha winawake, uko nkulondola, amapita ku tchalitchi ndi inu, zilonda za mmimba. Uko nkulondola. Inu si wochokera kuno. Kuno si kwanu. Inu munachokera kutali ndithu. Mukukhulupirira kuti Iye akhoza kundiuza ine kumene inu mukuchokera? Missouri. Uko nkulondola ndendende. Bambo Friels, tsopano ngati inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kupita kwanu ndi kukakhala bwino, ndi zinthu zanu zonse zimene inu mukuzipempha. Pitani ndipo mukawakhulupirire Ambuye Yesu Khristu.

³²² Inu mukukhulupirira? Zikuwoneka ngati ine ndiyenera kuti ndikukudziwani inu. Ine ndakuwonani inu penapake. Oh, ine ndikutero, ine ndikudziwa pamene inu munali. Ndinu... Tsopano, dikirani miniti. Ine sikuti ndabalalika, koma uku ndi kudzoza. Inu muli... Tsopano, dikirani miniti.

Inu munachiritsidwa ku Louisville, Kentucky, kapena mlongo wanu anachiritsidwa. Ndinu amene...Hupp, mtsikana wa Mlongo Hupp. Uko nkulondola. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, kuti muchiritsidwa monga mlongo wanu anachitira? Pitani kwanu, landirani izo, Yesu Khristu wakupangani inu kukhala bwino.

³²³ M'bale, mukhulupirire kuti manjenje achoka kwathunthu, ndipo muzingopita kwanu, mukuti, "Zikomo Inu, Ambuye Yesu, ine ndikupita kwathu, ndikukachiritsidwa." Ndipo Iye akachita zimenezo.

³²⁴ Inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, bwana? Bwanji ngati ine ndikanabwera ndi kudzaika manja pa inu, ndi kudzoza uku? Inu mungakhulupirire kuti izo zingachitike, kuchitika kwa inu? Ine ndibwera kumeneko ndi kudzachita izo, mu Dzina la Yesu Khristu. Inu mufa mutagona pamenepo, ndinu kwambiri, mwadwalika kwambiri, palibe chimene chingachitidwe. Muli ndi madzi mmapapo. Uko nkulondola. Inu mufa mutagona pamenepo, motsimikiza basi monga dziko. Tsopano, bwanji osangomukhulupirira Iye ndi mtima wanu wonse? Imirirani, mu Dzina la Yesu...?...

[M'bale Branham akuwapempherera anthu angapo, ambiri a mawu ake sakumveka—Mkonzi]. Mulungu, perekani izi. Iye anamva pemphero langa mu Dzina la Yesu. Mulungu, perekani izi.

Musandipitirire, O wodekha...

³²⁵ Mupemphere, aliyense, tsopano, limodzi, ife tidzayika manja. Kudzoza kwa Mzimu Woyera kuli pano, ine ndiyika manja pa anthu. Baibulo linati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Chabwino.

[M'bale Branham akupitiriza kumawapempherera anthu, ambiri a mawu ake sakumveka—Mkonzi]...?...Tuluka mwa iye, Satana, mu Dzina la Yesu Khristu...?...Mu Dzina la Ambuye Yesu...?...Mu Dzina la Ambuye Yesu...?...Atate Akumwamba...?...

³²⁶ Tiyeni tipemphere tsopano chifukwa cha mipango iyi apa. Atate athu Akumwamba, iwo anatenga kuchokera mthupi la Paulo Woyera, mipango, kapena tizovala, ndipo llo linanena kuti "Mizimu yonyansa inachoka kwa iwo." Ife tikuzindikira kuti ife sitiri Paulo Woyera, koma ife tikudziwa kuti Inu mukadali Yesu yemweyo, pakuti Ndinu wamoyo mochuluka basi lero monga Inu munali mmasiku a Paulo Woyera. Ine ndikupempherera zopempha izi, Ambuye, zomwe mipango iyi ikuimirira. Zovala zapang'ono ndi mipango, ndi tinsapato tating'ono ta ana. Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mupereke zimenezo.

³²⁷ Ife timaphunzitsidwa kuti Israeli anali pa kuguba kwake waku dziko lolonjzedwa, Lawi la Moto lalikulu linkapita patsogolo pawo, mneneri ankawaimirira iwo, ankaimirira

Mulungu, kwa iwo pa dziko lapansi. Ndipo iwo...mneneri uyu anawatsogolera iwo mpaka ku Nyanja Yakufa, ndipo iyo inatseka msewu. Panali chinachake mnjira pamene iwo anali kuyenda mu mzere wa ntchito. Mulungu anayang'ana pansi kuchokera Mmiyamba kupyolera mu Lawi la Moto lija, ndipo nyanja inachita mantha, ndipo iyo inayalulidwira mmbuyo ndipo inatsegula njira yodutsa pa nyanja pomwe, kuti Israeli azipitirira pa njira ya ntchito, ndipo iwo anapita ku dziko lolonjezedwa.

³²⁸ Mulungu, pamene mipango iyi iti ikaikidwe pa odwala ndi osautsika... Satana wadutsa mzere wawo, iye akuwachinga iwo pa njira ya ntchito. Mulole Mphamvu imene inadutsa Ambuye wathu, Yemwe ali pano tsopano, ibwere pa mipango iyi. Ndipo, pamene iyo ikakhudze odwala, mulole mdierekezi akawopsyezedwe, pamene Iye azikayang'ana pansi kupyolera mu Magazi a Yesu Khristu, ndipo mulole aliyense wa iwo achiritsidwe ndipo apitirire pa njira ya ntchito. Perekani izi, Ambuye. Ife tikukuthokozani Inu. Kukhalapo Kwanu kuli pano. Oh, kudzoza kwaulemelo uku kwa Mzimu Wanu kumene kukutigwedeza ife anthu achivundi, Ambuye. Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha ubwino Wanu! Adalitseni awa tsopano, mu Dzina la Yesu.

³²⁹ Ndi mitu yanu yoweramitsidwa, munthu aliyense muno. Osati kokha kuweramitsa mitu yanu, tsopano ine ndikufunsani inu kuti muweramitse mitima yanu ndi iyo. Ndi chiyani chinanso chimene Mulungu akanachita kukulolani inu kuwona kuti Iye ali pano? Tsopano mutenge mawu anga. Kudzoza uku ndi kopambana kwambiri pakali pano mpaka ine ndiri pafupi kuchita chizungulire pano. Ine sindine wotentheka. Inu mukudziwa ine sindiri. Ine sindimanyengedwa ndi zabodza. Ine ndikungokuuzani inu chimene chiri choonadi. Ndizo Mwamalemba. Kuwala kumeneko ndithudi kwafalikira ponseponse, izo zikuwoneka ngati Kuli paliponse pozungulira pano. Kusowa kwakukulu koteroko! Ndikhulupirireni ine.

³³⁰ Baibulo linati, mu Marko 16, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Ndi okhulupirira angati ali pano? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino, Baibulo linati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Kotero kuti inu mudziwe kuti si ine, inu muli basi mochuluka mu zimenezo monga momwe ine ndiriri. Iyi ndi mphatso chabe yochokera kwa Mulungu, kuti idzamuwonetsere Iye, Iyo imafotokoza zinthu. Ndipo ine nditenge aliyense kuti alembe, kudutsa mu zakazi, kodi Iwo unayamba wayankhulapo chirichonse koma chimene chinadzachitika ndendende basi? Zooni mwangwirowi, nthawi iliyonse. Ndizo—izo ziyenera kutero, chifukwa ndi Mulungu. Tsopano, osati mungoyang'ana mwa theka, muchiyang'ane chinachake mwakuya kotaliko. Taonani, Iye ali pano tsopano,

pakali pano!

³³¹ Tsopano, ngati inu muli wokhulupirira, ikani dzanja lanu pa winawake wapafupi ndi inu, ndipo iwo ayika dzanja lawo pa inu. Inu musadzipempherere nokha, inu muwapempherere iwo chifukwa iwo akhala akukupemphererani inu. Tsopano kuti inu mukhoze kudziwa, ndipo—ndipo ngati inu muti muchite izi, ine ndikutsimikizirani inu. Chabwino, palibe machira kapena mabedi otsala, onse apita. Koma inu mwakhala muli pano pamene machira ndi mabedi anali atagona apa, opunduka, olumala, opuwala, akhungu, palibe nthawi imodzi koma kanthu kalikonse ka izo. Tsopano, momwe inu mumapemphera mu tchalitchi, ngati ndinu wa Methodisti, mupemphere monga Amethodisti amachitira. Ngati ndinu wa Baptisti, pempherani monga a Baptisti amachitira. Ngati ndinu wa Chipentekoste, pempherani monga iwo amachitira. Chirichonse chimene inu muli, pempherani. Koma inu mumupempherere munthu yemwe inu mwayikapo manja anu. Zikatero mukhulupirire.


³³² Tsopano, kumbukirani, Baibulo linati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Tsopano inu mumupempherere aliyense, monga aliyense payekhapayekha. Ine ndikupemphererani inu, pamodzi, kuchokera pa nsanja. Tsopano, aliyense mwanjira yanu yanu.

³³³ Atate athu Akumwamba, ife tikuyandikira zifundo Zanu. Ife sitikanabwera mu dzina lathu lomwe, ife sitinapatsidwe lonjezo ndi limenelo. Koma ife tinapatsidwa lonjezo ndi Mwana Wanu Yemwe wokonedwa, kuti, “Ngati mudzafunsa Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho.” Limenelo linali lonjezo Lanu. Tsopano, Atate, ine ndikupemphera kuti Inu mudziwonetsere Nokha ndi okhulupirira awa. Iwo akuyika manja awo pa odwala, pa wina ndi mzake, ndipo ife tikubwera tsopano ku Mpandowachifumu wa Mulungu, kuwabweretsa iwo. Mu Baibulo, mu Marko, mutu wa 11, ndime ya 23, iyo imati, “Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, ‘Sunthidwa,’ ndipo osakaika mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti zimene inu mwanenazo zichitika, inu mukhoza kukhala nazo zimene inu mwanenazo. Ngati inu mukhala mwa Ine ndi Mawu Anga mwa inu, pemphani chimene inu mukufuna, ndipo icho chidzaperekedwa.”

³³⁴ Tsopano, Atate, pa lamulo lirilonse la Mawu Anu, ine ndawavomereza Iwo mosalabadira zimene ena akunena. Ine ndawakhulupirira Iwo basi momwe Iwo analembdewera. Pakuti Iwo si kutanthauzira kwa mseri, ife timauzidwa, koma basi momwe Iwo analembdewera. Ngati Inu mudzatiweruze ife pogwiritsa ntchito Bukhu ili, Inu ndithudi mumawonetsetsa kuti Ilo likubwera kwa ife mmawonekedwe a mtundu woyenera, chifukwa ndife oti tidzaweruzidwe ndi Bukhu. Ndipo tsopano, Atate, ine ndikulikhulupirira Ilo ndi mtima wanga wonse, ndi

kuposeraipo, ngakhale mphatso ya Mzimu wa uneneri imene Inu mumaidziwitsa. Ndipo ndi chifukwa chake ine ndikudziwa Iwo ndi Inuyo, chifukwa Iwo nthawizonse umakhala ndendende ndi Lemba. Tsopano ife tikubwera, Ambuye, ndipo tikukuthokozani Inu chifukwa cha Iwo. Ndipo mutidzoze ife tsopano. Ife tikuyandikira malo a mdani.

³³⁵ O Satana, ndiwe chinthu chogonjetsedwa. Iwe ulibe mphamvu. Mwana wa Mulungu anatenga mphamvu yako, anakuvula iwe chirichonse chimene iwe unali nacho, pa Kalvare; anatsimikizira kuti Iye ali ndi ife, mwa chiwukitsiro. Ndipo monga aja akubwera kuchokera ku Emau, Iye wawonekera kwa ife mmawa uno ndipo wachita chinachake momwe Iye anachitira izo kupachikidwa Kwake kusanachitike, chotero ife tikudziwa kuti Iye anawuka kwa akufa. Ndipo, Satana, ife tikubwera mu Dzina Lake, Dzina la Yesu, ndi Mphamvu ya Khristu. Ndipo iwe wagonjetsedwa, ndipo ndiwe wonyenga chabe. Ndipo ngati ife tingavomereze kunyenga kwako, iwe ukhoza kutipha ife nthawi isanakwane. Koma iwe sungakhoze kuchita zimenezo. Ife tikubwera, kudzatsutsa zimenezo mwa Mawu a Mulungu, mwa kuvutika kolowa mmalo kwa Yesu. Ife tikugonjetsa chinyengo chako. Ife tikuitana dzanja lako, Satana. Ndipo ife tikutuluka kudzaitsatira nkhoa imeneyo, monga mkango mmasiku a Davide. Ife tikubwera kuti tidzaibweretse nkhoa imeneyo kubwerera ku thanzi labwino ndi mphamvu. Amasule iwo, mu Dzina la Yesu Khristu! Tuluka pa malo awa! Tuluka mwa anthu awa, Satana! Ife tikukudzudzula iwe, mu Dzina la Yesu Khristu. Asiye iwo azipita, pakuti mwa Dzina la Khristu, ife tikuwabweretsa iwo ku Mpandowachifumu wa Atate mmawa uno, ndi thanzi ndi mphamvu, kupyolera mu Dzina la Yesu Khristu.

³³⁶ Anthu nonse inu tsopano amene mukukhulupirira kuti pemphero la chikhulupiriro lapemphereredwa, kuti inu mwaika manja anu pa winawake, kuti inu mwakhulupirira, ndipo mukukhulupirira kuti Khristu wawachiritsa iwo, ndipo inu mukukhulupirira kuti inu mwachiritsidwa chifukwa munthuyo anakupemphererani inu, ndipo inu mukuvomereza izo pakali pano kuti inu mwachiritsidwa, ine sindikusamala kaya ndinu wolumala bwanji, wakhungu bwanji, wogontha bwanji, chirichonse chimene inu muli, wofooka bwanji, wodwala bwanji, imirirani pa mapazi anu, mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo mulandire izo. Amen. Dzukani, paliponsepo, ziribe kanthu chimene chavuta. Imirirani pa mapazi anu, kwezani mmwamba manja anu ndi kumutamanda Mulungu chifukwa cha ubwino Wake. Amen. 

62-0218 Khama
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org